


2025
JAN - MAL

Vol. 104, No. 1
Maphunziro AnBaibulo Apa Sabata
Chigawo cha akulu



GAWO LOYAMBA

Uthenga Wabwino **Malinga ndi Yohane**

Wophunzira wakondedwayo adafotokozza Yesu Khristu,
Mwana wa Mulungu wamuyaya kuti ndi mankhwala a
Mulungu a tchimo la dziko lonse lapansi.

Ziri mkati

| | |
|--|----|
| 1. Uthenga Wabwino Molingana Ndi Yohane..... | 5 |
| 2. Mwanawankhosa Wa Mulungu | 10 |
| 3. Ukwati Ku Kana | 15 |
| 4. Yesu Mu Yesu Mu Kachisi | 20 |
| 5. Yesu Ndi Nikodemo | 26 |
| 6. Kuyenda Kwa Mzimu Woyera..... | 31 |
| 7. Yesu Ndi Yohane M'batidzi | 36 |
| 8. Yesu Ndi Mzimayi Wakusamariya | 41 |
| 9. Kubadwa Kwa Mtumiki | 47 |
| 10. Yesu Ndi Mwana Wa Mkuru Wa Ayuda..... | 52 |
| 11. Yesu Ndi Opuwala Wa Ku Betesaida | 57 |
| 12. Ulamuliro Wa Mwana Wamunthu | 62 |
| 13. Yesu Adyetsa Khamu La Anthu | 67 |

Maphunziro a Baibulo apa Sabata, phunziro la tsiku ndi tsiku, lazikidwa pa Baibulo ndi Mzimu wachinenero basi popanda ndemanga zowonjezera. Mawu andemanga ndi achidule momwe mungathere kupereka malingaliro achidule, achindunji. Dzikutiro [] zamaperekedwa nthawi zina kuti atsimikizire kumveka bwino, nkhani yoyenera, ndi kuwerenga kosalala. Kuphunzira kopitilira kupyolera m'mene mwachokera ndemanda kumalimbikitsidwa kwambiri

Zitsanzo: Mchere wabwino pachikuto chakutsogolo; Map Resources pa pp. 4, 46, 72.

Copyright © 2025 by the Seventh Day Adventist Reform General Conference, Chigawo cha Sabata Sukulu, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019, USA.

Telefoni: 1-540-362-1800 • Webusaiti: www.sdarm.org • Imelo: info@sdarm.org

Kumalawi: SDARM Malawi Mission P.O. Box 200069 Lilongwe 2.

Foni: +265 999 701 423, +265 884 288 535

Maphunziro a Baibulo pa Sabata (USPS 005-118), Vol. 101, No. 1, January–March 2025. Lofalitsidwa pa kotala ndi Seventh Day Adventist Reform General Conference, chigawo cha Sabata Sukulu Kusindikizidwa, ndi kugawidwa ndi Reformation Herald Publishing Association, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019–5048, U.S.A. Malipiro anthawi ndi nthawi ku Roanoke, Virginia 24022-9993.

U.S.A. ndi Canada

Lumikizani: Telefoni 1-540-366-9400 • Webusaiti: www.reformationherald.com • Imelo: info@reformationherald.org
Kulembetsa pachaka ku U.S.A.: U.S. \$22.00. Kusindikiza kwakukulu \$33.00. Mayiko \$21.00 kuphatikiza kutumiza. Kusindikiza kwakukulu kwapadziko lonse \$31.00 kuphatikiza kutumiza. Kope limodzi \$6.00. Kusindikiza kwakukulu \$9.00. Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira (mu ndalama zaku U.S. zokha) pa keyala ali pansipa. Mitengo zitha kusintha popanda chidziwitso. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata,

South Africa

Lumikizani: Telefoni & Fax 27-011-336-7064 • Webusaiti: www.sdarm.sa.org

za • Imelo: admin@sdarm.sa.org za Kulembetsa kwapachaka mu South Africa: R120-00 (kope limodzi R35-00).

Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa.

POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 7950, Johannesburg 2000, South Africa

Malawi

Lumikizani: Telefoni +26 999 701 423, +265 884 288 535

za • Imelo: sdarmmalawi@yahoo.com Kulembetsa kwapachaka Malawi: MK 2000 (kope limodzi MK 500).

Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa.

POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 20069, Lilongwe 2. Malawi

MAWU OTSOGOLERA

Chaka chino, tiphunzira magawo anayi akotala pa buku la Uthenga Wabwino wa Yohane. Chifukwa cha kudzichepetsa, mlembi wa Uthenga Wabwino wachinayi sakudzizindikiritsa yekha, ndipo samadzitchula kuti ndi mmodzi wa ophunzira awiri amene anatsatira Yesu poyamba (Yohane 1:37). M'malo mwake, iye ananena kuti “wophunzira wina,” “wophunzira ameneyo,” “wophunzira... amene anamkonda,” “wophunzira amene Yesu anamkonda,” ndi “wophunzira amene akuchitira umboni za izi” (Yohane 18:15; 19:26; 21:20, 23, 24). Mfundo yakuti ophunzira ena otchuka amatchulidwa ndi mayina pamene dzina la Yohane silinatchulidwe, ikuwoneka kuti ikusonyeza kuti iye ayenera kuti anali mlembi wauthenga wa bwinowo.

Malingana ndi Mzimu wa Wachinenero, mlembi wa Uthenga Wabwino wachinayi anali Yohane, “wophunzira amene Yesu anamkonda.” Iye anali mmodzi wa ophunzira atatu amene anaona ulemerero wa Kristu pa phiri la kusandulika ndi zowawa Zake m'munda atangotsala pang'ono kumangidwa. Moyo wake uli chitsanzo chapadera chosonyeza mmene mphamvu ya Mulungu ingasinthire kotheratu “mwana wa bingu” kukhala munthu wa chikondi ndi wozindikira mwakuya.

“Yohane anamamatira kwa Kristu monga mpesa umakangamirira kumzati wolemekezeka. Chifukwa cha Mbuye wake anapyola muzoopsa zabwalo la milandu ndi kukayandikira pa mtanda, ndipo pa uthenga wa kuti Khristu wauka, anathamangira kumanda, mu changu chake anapotsa ngakhale Petro wopupuluma.

“Chikondi chodalira ndi kudzipereka kopanda undekha zosonyezedwa m'moyo ndi mukhalidwe la Yohane zimapereka maphunziro amtengo wapatali kumpingo Wachikristu. Yohane mwachibadwa analibe kukongola kwakhalidwe kumene kunaonekera kudzera mu zimene zinamuchitikira pambuyo pake. Mwachibadwa anali ndi zilema zazikulu. Iye sanali kokha wonyada, wodzikuzza, ndi wofuna ulemu, komanso anali wopupuluma, ndi waukali povulazidwa. Iye ndi mbale wake ankatchedwa ‘ana a bingu.’ Kupsa mtima koipa, khumbo la kubwezera, mzimu waoneneza, zonse zinali mwa wophunzira wokondedwayu. Koma pansi pa zonsezi Mphunzitsi waumulunguyo anazindikira mtima wachangu, wowona mtima, ndi wachikondi. Yesu anadzudzula kudzikonda kumeneku, kukhumudwitsa zokhumba zake, kuyesa chikhulupiriro chake. Koma Iye anamuululira chimene moyo wake unkalakalaka—kukongola kwa chiyero, mphamvu yosintha ya chikondi.”— *The Acts of the Apostles*, p. 539, 540.

Maulamuliro onse akale amanena kuti Uthenga Wabwino wa Yohane unalembedwa ku Efeso cha m'ma A.D. 90 kapena mbuyo mwake. Wophunzirayu anaikidwa m'mbiya yamafuta owira ndikupulumuka imfa m'njira yozizwitsa, ndipo pambuyo pake anakaikidwa kuchisumbu cha Patmo (Chivumbulutso 1:9). Pamenepo iye analemba Chivumbulutso. Kulowa kwa Nerva pampando wachifumu (AD 96) kunamupangitsa kuti abwerere ku Efeso, kumene chimakhulupiridwa kuti anapitirizabe kukhala mpaka imfa yake mu ulamuliro wa Trajan (AD 98-117).

Mzimu wa Khristu utsogolere maphunziro athu a mukotala lino, ndi kukhudza mitima yathu poyankha ku chikondi chake!

A gawo la sabata skulu a ku General Conference

Chopereka cha Sabata loyamba Sabata, Januwale 4, 2025



Malo ochitira zinthu zosiyanasiyana a zathanzi ndi maphunziro ku Paraguay

Dziko la Paraguay ndi dziko lopanda lozunguliriridwa ndi maiko osiyanasiyana ku South America, linacita malire ndi Argentina, Bolivia, ndi Brazil. Chiwerengero cha anthu ndi pafupifupi 6.1 miliyoni, 96.1% ndi omwe amati ndi Akhristu (88.3% Chikatolika ndi 7.8% zipembedzo zina za chikhristu); 2.6% amati ndi osapembeza, ndipo otsalawo ndi a zipembedzo zina kapena sanazitchule. Chuma cha dziko chimakhazikika pa ulimi makamaka wa soya—ndipo pazaka 50 zapitazi, Paraguay yakuzanso kwambiri makampani opanga magetsi ochokera kumadzi. Mamembala oyamba a SDA Reform Movement anafika kuno kuchokera ku Hungary m’ma 1940 ndipo ntchito inakula kwambiri m’ma 1950 kudzera m’mautumiki a ukopotala ndipo pambuyo pake m’ma 1970 kupyolera muzamishonale wanchito za machiritso. Panopa tili ndi gulu lodabwitsa la mamembala okhulupirika mu mizinda ikuluikulu. Kwa zaka zambiri tinali ndi chipatala chachilengedwe chomwe chinkagwira ntchito mumzinda waukulu wa Asunción, kutipangitsa ife kuthekera kwa kugawana uthenga wabwino ndi miyoyo yambiri ndi Kuphunzitsa moyo waanthu otsala a Mulungu. Ndi thandizo la Mulungu ndi gulu lathu la akatswiri lotcedwa inter disciplinary, tikuyembekeza kutsitsimutsa chipatalachi—koma tsopano kuti chigwire ntchito yofikira anthu mumzinda, ndi m’midzi kuti akwaniritse lamulo la umulungu lakuti: “Chokani mizinda. Khazikitsani zinyumba zanu, masukulu anu, ndi maofesi kutali kuchokera pakati pa anthu.’ ”—*Selected Messages, bk. 2, p. 357.* Poganzira masomphenya amenewa, tinapeza malo kumudzi wina wokongola kwambiri m’dera la Paraguari, pafupifupi 66 km. (41 miles) kuchokera kulikulu. Tili kale ndi malo opatulika ndi opembedza pa malowa, koma ichi ndi chiyambi chabe. Cholinga ndi kukhazikitsa malo ochitira zinthu zosiyanasiyana, malo okhala ndi zipatala zoyambira, sukulu ya tchalitchi, tchalitchi, ndi a malo opangira mabizinesi odzipezera okha chakudya chaumoyo.

Tikupempha abale athu padziko lonse kuti atithandize kukhala owolowa manja kuti tichikwaniritse cholinga ichi. Kugwirizana kwanu kudzapereka chilimbikitso chatsopano cha gawo lomaliza lofunika kumaliza ntchitoyi. Tikudalira mu mphamvu ndi chisomo chodabwitsa cha Mulungu ndipo tili otsimikiza kuti Yehova adzadalitsa kuyesetsa kwa anthu athu onse padziko lonse lapansi kulimbikitsa ndi kukulitsa kulalikira uthenga mu dera lino la munda wake wamphesa.

Abale ndi alongo anu ochokera ku filudi ya Paraguay

UTHENGA WABWINO MOLINGANA NDI YOHANE

VESI LOLOWEZA: “Ndipo Mawu anasandulika thupi, nakhazikika pakati pathu, (ndipo tinawona ulemerero wake, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate), wodzala ndi chisomo ndi chowonadi” (Yohane 1:14).

Zowelenga zoonjezera: Patriarchs and Prophets, pp. 44–51, 111–116.

“Kuyambira kunthawi zosayamba Kristu analumikizidwa ndi Atate, ndipo pamene Iye anadzitengera pa Iye yekha khalidwe la umunthu, Iye anali ammodzibe ndi Mulungu.”— *Selected Messages*, bk. 1, p. 228.

1. YESU, M'MODZI NDI ATATE

Loyamba, Dis. 29

a. **Kodi Mawu a Mulungu amati chiyani za Yesu asanakhale munthu? Yohane 1:1,**

“Kuyambira masiku amuyaya Ambuye Yesu Khristu anali mmodzi ndi Atate; Iye anali ‘chifaniziro cha Mulungu,’ chifaniziro cha ukulu ndi ulemerero Wake, ‘chinyezimiro cha ulemerero wake.’ Kunali kusonyeza ulemerero umenewu kuti anadza ku dziko lathu lapansi. Ku dziko lapansi lokhala ndi mdima wa uchimo Iye anabwera kudzaulula kuwala kwa chikondi cha Mulungu—kukhala ‘Mulungu nafe.’” — *The Desire of Ages*, p. 19.

“Kristu, Mawu, wobadwa yekha wa Mulungu, anali mmodzi ndi Atate wamuyaya—m’modzi mwachibadwa, m’makhalidwe, m’chifuniro—munthu yekhayo amene akanatha kulowa mu uphungu ndi zifuno zonse za Mulungu.”—*Patriarchs and Prophets*. p. 34.

b. **Kodi Atate ndi angelo ankamuona bwanji Yesu? Masalmo 45:6; Yesaya 9:6; Ahebri 1:3, 6-8.**

“Angelo ndi atumiki a Mulungu, onyezimira ndi kuunika koyenda kosalekeza kuchokera pamaso pake ndi kufulumira kuchita chifuniro Chake. Koma Mwana, wodzozedwa wa Mulungu, ‘chifaniziro choonekera cha umunthu Wake,’ ‘kuwala kwa ulemerero Wake,’ wonyamula zinthu zonse ndi mawu amphamvu yake,’ ali ndi mphamvu pa onse.”— *Ibid.*

a. Kodi ndi ndani amene analenga zinthu zonse? Yohane 1:3, 10; Akolose 1:15-17; Ahebri 1:2.

“Anali Kristu amene anayala miyamba, nakhazikitsa maziko a dziko lapansi. Linali dzanja Lake limene linapachika maiko mu mlengalenga, ndi kupanga maluwa a kuthengo. ‘Mphamvu yake inakhazikitsa mapiri.’ ‘Nyanja ndi yake, ndipo anaipanga.’ Masalmo 65:6; 95:5. Anali Iye amene anadzaza dziko lapansi ndi kukongola, ndi mpweya ndi nyimbo. Ndipo pa zinthu zonse zapadziko lapansi, mumlengalenga, ndi mlengalenga, Iye analemba uthenga wa chikondi cha Atate.”— *The Desire of Ages*, p. 20.

b. Fotokozani mmene maiko ndi chilengedwe chonse zinalengedwera. Masalmo 33:6, 9; 104:1–6.

“Mulungu analankhula, ndipo mawu ake analenga ntchito zake m’chilengedwe. Chilengedwe cha Mulungu ndi nkhokwe ya zinthu zokonzedwa kuti Iye azizigwiritsa ntchito nthawi yomweyo kuchita zimene Iye amafuna.”—*The SDA Bible Commentary [E. G. White Comments]*, vol. 1, p. 1081.

“Pamene dziko lapansi linatuluka kuchokera m’dzanja la Mlengi wake, linali lokongola kwambiri. Pamwamba pake panali mapiri, zitunda, ndi zigwa, zophatikizika ndi mitsinje yolemekezeka ndi nyanja zokongola; koma zitunda ndi mapiri sizinali zoopya ndi zokhotakhota, zodzala ndi maphompho owopsa, monga momwe zimakhallira tsopano; nsonga zakuthwa, zosongoka za maziko a miyala ya dziko lapansi zinakwiridwa pansu pa nthaka yobala zipatso, imene paliponse inatulutsa kumera kochuluka kwa maluwa. Panalibe zithapwi zonyansa kapena zipululu zopanda kanthu. Zitsamba zokongola ndi maluwa osakhwima zinkalonjera diso kulikonse. Pamwamba pake panali mitengo yamtengo wapatali kwambiri kuposa ina iliyonse yomwe ilipo tsopano. Mpweya, wosaipitsidwa ndi mafungo onyansa, unali wabwino komanso wathanzi. Panthaka ponse panaposa kukongola kwa malo okongoletsedwa ozungulira nyumba yachifumu yokwezeka kwambiri. Khamu la angelo linawona chochitikacho mokondwera, ndipo anakondwera ndi ntchito zodabwitsa za Mulungu.”— *Patriarchs and Prophets*, p. 44.

“Baibulo silimafotokoza za zaka zambiri zammene dziko lapansi linasintha pang’onopang’ono kuchoka ku chipwirikiti. Pa tsiku lililonse lotsatizana la kulenga, malembo opatulika amafotokoza kuti kunali madzulo ndi m’maŵa, mofanana ndi masiku ena onse amene anatsatirapo. Kumapeto kwa tsiku lililonse kumaperekedwa chotulukapo cha ntchito ya Mlengi.”—*Ibid.*, p. 112.

a. Kodi ndi ndani amene ndi Oyambitsa wa zamoyo zonse ndi kuunika konse —ndipo kodi zimenezi zili ndi phindu lanji kwa ife? Yohane 1:4-9; Machitidwe 17:28.

“Anali [Khristu] amene analankhula kudzera mwa aliyense amene kupyora m’mibadwo yonse analengeza mawu a Mulungu kwa anthu. Mwa Iye maulemerero wonse woonekera mu miyoyo ya anthu olemkezekera ndi okwezeka kwambiri apadziko lapansi anali chinyezimiro chake.”—*Education*, p. 73.

“Khristu ndiye ‘Kuunika kwenikweni kumene kuunikira anthu onse akulowa m’dziko lapansi.’ Yohane 1:9. Pakuti kudzera mwa Khristu munthu aliyense ali ndi moyo, momwemonso kudzera mwa Iye mzimu uliwonse umalandira kuwala kwina kwa umulungu.”—*Ibid.*, p. 29.

“Mphamvu ya Mulungu ikugwiritsidwabe ntchito posamalira zinthu za chilengedwe Chake. Sichifukwa cha chipangizo chimene chinaikidwa ndi kuyamba kuyenda kamangopitirizabe kugwira ntchito ndi mphamvu zake kuti mtima umagunda, ndi kupuma kumatsatira kupuma. Kupuma kulikonse, kugunda kulikonse kwa mtima, ndi umboni wa chisamaliro cha Iye amene tikukhala ndi kuyendayenda ndi kukhala ndi moyo wathu. Kuyambira kachiroombo kakang'ono kufikira munthu, cholengedwa chilichonse tsiku lililonse chimadalira pa chisamaliro Chake... “Mphamvu yamphamvu imene imagwira ntchito m’chilengedwe chonse ndi kuchirikiza zinthu zonse siili, monga momwe anthu ena asayansi amanenera, si mfundo yofala ponseponse, yosonkhezera zinthu. Mulungu ndiye mzimu; komabe Iye ndi munthu payekha, pakuti munthu anapangidwa m’chifanizo Chake. Monga munthu, Mulungu wadziulula Yekha mwa Mwana Wake.”—*Ibid.*, p. 131.

b. Kodi Yesu akunena chiyani za Iyemwini? Yohane 9:5; 8:12; 3:19; 12:46.

“M’mawu akuti, ‘Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi,’ Yesu anadzitcha yekha Mesiya. Simeoni wokalamba... analankhula za Iye monga ‘kuunika kukuunikira amitundu, ndi ulemerero wa anthu anu Israyeli.’ Luka 2:32. M’mawu amenewa anali kunena kwa Iye ulosi wodziwika kwa Aisraeli onse. Mwa mneneri Yesaya, Mzimu Woyera analengeza kuti, ‘Ciri cinthu copepuka ndithu kuti Iwe ukhale mtumiki wanga wakuutsa mafuko a Yakobo, ndi kubwezera osungika a Isiraeli; ndizakupatsanso ukhale kuunika kwa amitundu, kuti ukhale chipulumutso Changa kufikira malekezero a dziko lapansi.’ (Yesaya 49:6, R.V.). Uneneri umenewu kaŵirikaŵiri umazindikiridwa kuti unalankhulidwa ponena za Mesiya, ndipo pamene Yesu anati, ‘Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi,’ anthu sanalephere kuzindikira kudzinenera Kwake kukhala Wolonjezedwayo.”—*The Desire of Ages*, p. 465.

a. Kodi Yesaya analosera chiyani za dzina la Kristu? Yesaya 7:14. Kodi ulosi umenewu unakwaniritsidwa liti? Mateyu 1:22, 23.

“Popeza Yesu anabwera kudzakhala nafe, tikudziwa kuti Mulungu amadziwa mayesero athu, ndipo amamva chisoni tikamamva chisoni. Mwana aliyense wa Adamu angamvetsetse kuti Mlengi wathu ndi bwenzi la ochimwa. Pakuti mu chiphunzitso chirichonse cha chisomo, lonjezo lirilonse la chisangalalo, ntchito iriyonse ya chikondi, kukopa kulikonse kwa umulungu koperekedwa mu moyo wa Mpulumutsi pa dziko lapansi, tikuona ‘Mulungu nafe.’” — *The Desire of Ages*, p. 24.

b. Kodi Yesu anachita chiyani kuti atifikire mu khalidwe lathu wakugwa? Yohane 1:14; Afilipi 2:5-8; Ahebri 2:14-18.

“Kuti tidziwe khalidwe Lake la umulungu ndi moyo wake, Khristu anatenga chikhalidwe chathu nakhala pakati pathu. Umulungu unavumbulutsidwa mu umunthu; ulemerero wosaoneka m’maonekedwe ooneka aumunthu. Anthu atha kuphunzira za wosadziwika kudzera mu wodziwika; Zakumwamba zinavumbulutsidwa kudzera mwa zapadziko lapansi; Mulungu anaonekera m’mafanizidwe a anthu.” — *Christ’s Object Lessons*, p. 17.

“Mwana wa Mulungu anaukiridwa pa sitepe iliyonse ndi mphamvu za mdima. Atatha kubatizidwa anatsogoleredwa ndi Mzimu kupita ku chipululu, ndipo adayesedwa kwa masiku makumi anayi... Ngati Iye sakanakhala wogawana nawo chikhalidwe chathu, sakanayesedwa monga mmene munthu amayesedwera. Ngati sikunali kotheka kwa Iye kugonja ku mayesero, sakanakhala mthandizi wathu. Chinali chenicheni chotsimikizirika kuti Kristu anabwera kudzamenya nkondo monga munthu, m’ malo mwa munthu. Mayesero ndi chigonjetso chake zimatiuza kuti umunthu uyenera kutengera Chitsanzo; munthu ayenera kukhala wogawana nawo mkhalidwe waumulungu.” — *The SDA Bible Commentary [E. G. White Comments]*, vol. 5, p. 1082.

“Kuti asunge ulemerero Wake wophimbika monga mwana wa mtundu wamunthu wakugwa, ichi chinali chilango chokhwima kwambiri chimene Kalonga wa moyo anazipereka yekha kudusamo. Momwemo adayeza mphamvu Zake ndi Satana. Iye amene anathamangitsidwa kumwamba anamenya nkondo molimba mtima kuti apambane ndi Iye amene m’ mabwalo akumwamba amamuchitira nsanje. Imeneyi inali nkondo yotani nanga! Palibe chinenero chokwanira kuchifotokoza. Koma posachedwapa zidzavetsetsedwa ndi awo amene alakika kudzera mu mwazi wa Mwanawankhosa ndi mawu a umboni wawo.” — *Ibid.*, pp. 1081, 1082.

- a. **Kodi Yesu anabwera kudzachitira chiyani kwa mtundu wa munthu? Yohane 3:16, 17; 1:12; Luka 19:10.**
-
-

“Khristu anachitiridwa monga kuyenera ife, kuti ife tichitidwe monga kuyenera Iye. Iye anaweruzidwa chifukwa cha machimo athu, amene analibe nawo gawo, kuti ife tikayesedwe olungama ndi chilungamo chake, chimene ife tinalibe nacho gawo. Iye anavutika ndi imfa yomwe inali yathu, kuti ife tikhoze kulandira moyo umene unali Wake. ‘Ndi mikwingwirima Yake ife tachiritsidwa.’ ”— *The Desire of Ages*, p. 25.

- b. **Kodi timabwezeretsedwa bwanji kudzera mu nsembe ya Kristu? Agalatiya 4:5-7; Ahebri 2:10.**
-
-

“Khristu anapereka nsembe yodzaza ndi yokwanira, nsembe yokwanira kupulumutsa mwana wamwamuna ndi wamkazi aliyense wa Adamu amene angathe kulapa kwa Mulungu chifukwa cholakwira lamulo Lake, ndi kusonyeza chikhulupiriro mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.... Khristu ndiye woyang’anira chipulumutso chathu, ndipo kudzera mu mazunzo ndi nsembe Yake Iye wapereka chitsanzo kwa otsatira ake onse kuti kukhala maso ndi kupemphera, ndi kuyesesa kulimbikira, ndi zofunikira ku mbali yawo ngati iwo angathe kuimirira moyenera chikondi chimene chinakhala pachifuwa chake kwa mtundu wakugwa.”— *Testimonies for the Church*, vol. 2, p. 664.

“Mulungu amakonda ana ake omvera. Iye ali ndi ufumu wokonzedwera, osati kwa anthu osakhulupirika, koma kwa ana Ake amene anawayesa ndi kuwayesa m’dziko loipitsidwa ndi uchimo. Monga ana omvera, tili ndi mwayi wokhala paubwenzi ndi Mulungu. ‘Ngati ana,’ akutero, ‘ndiye olandira cholowa’ chosafa.... Kristu ndi anthu Ake ndi amodzi.”— *The SDA Bible Commentary [E. G. White Comments]*, vol. 6, p. 1077.

1. **Kodi ndi khalidwe lanji limene Yesu wakhala ali nalo kuyambira nthawi zosamba?**
2. **Ndani anayala kumwamba, nakhazikitsa maziko a dziko lapansi?**
3. **Kodi kuunika konse koono kumachokera kwa ndani?**
4. **Kodi Yesu akutchedwa chiyani pa Yesaya 7:14?**
5. **Kodi Yesu anakhala chiyani atatenga umunthu wathu?**

MWANAWANKHOSA WA MULUNGU

VESI LOLOWEZA: “Iye anatsenderezedwa, koma anazichepetsa yekha osasegula pakamwa pace; ngati nkhusa yosogoleredwa kukaphedwa, nndi ngati mwana wa nhosa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa pace” (Yesaya 53:7).

Zowelenga Zoonjezera: *The Desire of Ages*, pp. 132–143.

“Lolani wochimwa wolapayo akhazikitse maso ake pa ‘Mwanawankhosa wa Mulungu, amene achotsa chimo lace la dziko lapansi.”— *The Faith I Live By*, p. 107.

1. UMBONI WA YOHANE MBATIZI

Loyamba, Jan 5

a. Kodi Yohane M’batizi analengeza chiyani zokhudza Yesu? Yohane 1:15-18.

b. Kodi Yohane anadzizindikiritsa yekha bwanji kwa atsogoleri achipembedzo? Yohane 1:19-23. Kodi ndi ulosiwotani umene iye anakwaniritsa—ndipo tikulimikizana nawo bwanji ulosiwu? Yesaya 40:3-5.

“M’gawo lililonse la mbiri ya dziko lapansi Mulungu wakhala ali ndi mabungwe akekuti apititse patsogolo ntchito Yake, imene iyenera kuchitidwa m’njira Yake yoikika. Yohane M’batizi anali ndi ntchito yapadera, imene iye anabadwira ndi imene anaikidwirako—ntchito yokonza khwalala la Ambuye....

“[Utumiki wake wa m’chipululu] unali kukwaniritsidwa mosazembaitakwa ulosi kochititsa chidwi koposa.”— *The Southern Watchman, March 21, 1905*.

“Ambuye anapatsa [Yohane M’batizi] uthenga wake. Kodi anapita kwa ansembe ndi olamulira ndi kuwafunsa chilolezo kuti akalengeze uthenga umenewu?— Ayi, Mulungu anamuchotsa kwa iwo kuti asatengeke ndi mzimu ndi chiphunzitsa chawo. Iye anali liwu la wofuula m’chipululu [Yesaya 40:3–5]. Uwu ndiwo uthenga womwe uyenera kuperekedwa kwa anthu athu; tiri pafupi ndi kumapeto kwa nthawi, ndipo uthenga ndi wakuti, Konzani khwalala la Mfumu; sonkhanitsani miyala; kwezani muyezo kwa anthuwo. Anthu ayenera kudzutsidwa. Ino si nthawi yofuula mtendere ndi chitetezo.”—*Selected Messages, bk. 1, p. 410*.

a. Pamene Yesu anadza kwa Yohane kudzabatizidwa, kodi Yohane anaonetsera Iye motani ndi kuchitira umboniza ntchito yake kwa anthu? Yohane 1:29, 34. Kodi ndi ulosi wanji umene unakwaniritsidwa? Yesaya 53:4-7.

“Khristu anali Mumbolo wa munthu pa chiyambi cha dziko monga alili lero. Asanaveke umulungu wake ndi umunthu ndi kubwera ku dziko lathu lapansi, uthenga wabwino unaperekedwa ndi Adamu, Seti, Enoke, Metusela, ndi Nowa. Abrahamu m’Kanani ndi Loti ku Sodomu analengeza uthengawo, ndipo kuchokera ku mibadwo kufikira mibadwo ina amithenga okhulupirika analengeza Wakudzayo. Miyambo ya chuma cha Ayuda idakhazikitsidwa ndi Khristu Mwiniwake. Iye anali maziko a dongosolo lawo la nsembe zoperekedwa, choimira chachikulu cha utumiki wawo wonse wachipembedzo. Mwazi okhetsedwa monga nsembe imapelekedwa kuimira nsembe ya Mwanawankhosa wa Mulungu. Zopereka zonse zomwe zinali mthuzi zinakwaniritsidwa mwa Iye” — *Christ’s Object Lessons*, p. 126.

b. Kodi Yohane anamufotokoza motani Yesu kwa ophunzira ake? Yohane 1:35, 36. Kodi mawu ake anawakhudzabwanji, nanga n’chiyani chinachitika patsogolo pake mmoyo wake? Yohane 1:37.

“Tsiku lotsatira lake [patsogolo pa ubatizo wa Khristu], pamene ophunzira awiri anaimirira pafupi naye, Yohane anamuonanso Yesu ali pakati pa anthu. Kachiwirinso nkhope ya mneneriyo inawalitsidwa ndi ulemmerero wochokera kwa Osaonekayo, pamene anafuula, ‘Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu!’ Mawuwa anasangalatsa kwambiri ophunzirawo. Sanawamvetse bwino lomwe. Kodi dzina limene Yohane anamupatsa—‘Mwanawankhosa wa Mulungu’ linkatanthauza chiyani? Yohane mwiniyo anali asanafotokoze. Atamusiya Yohane, iwo anapita kukafunafuna Yesu.” — *The Desire of Ages*, p. 138.

“Yohane anauza ophunzira ake kuti Yesu ndiye Mesiya wolonjezedwayo, Mpulumutsi wa dziko lapansi. Pamene ntchito yake inali kutha, anaphunzitsa ophunzira ake kuyang’ana kwa Yesu, ndi kum’tsatira monga Mphunzitsi Wamkulu. Moyo wa Yohane unali wachisoni komanso wodzikana. Iye analengeza za kudza koyamba kwa Khristu, koma sanaloledwe kuchitira umboni zozizwitsa Zake, ndi kusangalala ndi mphamvu yosonyezedwa ndi Iye. Pamene Yesu anayenera kudzikhazikitsa monga mphunzitsi, Yohane anadziwa kuti iye mwini ayenera kufa. Liwu lake silinkamveka kawirikawiri, kupatula m’chipululu. Moyo wake unali wosungulumwa. Sanamamatire ku banja la atate wake, kuti asangalale ndi chiyanjano chawo, koma anawasiya kuti akwaniritse ntchito yake.” — *Early Writings*, p. 154.

a. Kodi ena mwa ophunzira oyambirira a Yesu anali ndani? Mateyu 4:18, 21. Kodi anasonyeza chidwi chotani mwa Khristundipo kusunkhana kwawo koyamba ndi Iye kunali kwakutali motani? Yohane 1:38, 39.

“M’modzi wa awiriwo [amene anatsatira Yesu] anali Andreyo, mbale wake wa Simoni; winayo anali Yohane mlaliki. Amenewa anali ophunzira oyambirira a Khristu. Mosonkhezere ndi chisonkhezere chosaleseka, iwo anatsatira Yesu—ofunitsitsa kulankhula naye, komabe anachita mantha ndi kukhala chete, otayika mu lingaliro lofunikira kwambiri lakuti, ‘Kodi ameneyu ndi Mesiya?’”

“Yesu anadziwa kuti ophunzirawa anali kumutsatira. Iwo anali zipatso zoyamba za utumiki Wake, ndipo munali chisangalalo mu mtima wa Mphunzitsi waumulungu pamene miyoyo imeneyi inalabadira chisomo Chake. Koma popotoloka adafunsa yekha, Mufuna chiyani? Iye Ankawasiya ndi ufulu obwerera m’mbuyo kapena kulankhula za chikhumbo chawo.

“Pa cholinga chimodzi chokha anali kuzindikira. Kukhalapo kumodzi kunadzaza malingaliro awo. Iwo anafuula kuti, ‘Rabi,... kodi mumakhala kuti?’ Mu kuyankhulana kwachidule panjira iwo sanathe kulandira zomwe iwo amazilakalaka. Iwo anafuna kukhala okha ndi Yesu, kukhala pa mapazi ake, ndi kumva mawu ake....

“Ngati Yohane ndi Andreyo anakakhala ndi mzimu wosakhulupirira wa ansembe ndi olamulira, iwo sakadapezeka monga ophunzira pa mapazi a Yesu. Iwo akadabwera kwa Iye monga otsutsa, kudzaweruzo mawu Ake. Motero ambiri amatseka chitseko cha mwayiwantengo wapatali kwambiri. Koma sizinali choncho ndi ophunzira oyambirirawa. Iwo anavomera ku kuitana kwa Mzimu Woyera mu ulaliki wa Yohane M’batizi. Tsopano anazindikira mawu a Mphunzitsi wakumwamba. Kwa iwo mawu a Yesu anali odzaza ndi kutsitsimutsa ndi choonadi ndi kukongola. Kuunikira kwaumulungu kunatsanuliridwa pa chiphunzitso cha Malemba Achipangano Chakale. Mitu yambiri ya choonadi inaonekera m’kuunika kwatsopano.”— *The Desire of Ages*, pp. 138, 139.

b. Kodi ophunzira oyambirira anachita chiyani atangokumana ndi Yesu? Yohane 1:41, 42.

“Andreyo ankafuna kugawa chimwemwe chimene chinadzaza mtima wake. Popita kukafunafuna mbale wake Simoni, anafuula kuti, ‘Tamupeza Mesiya’. Simon sanadikirire kuti amuitanireso kachiwiri. Iye anamvanso kulalikirira kwa Yohane Mbatizi, ndipo anafulumira kupita kwa Mpulumutsi.”—*Ibid.*, p. 139.

a. Fotokozani zimene zinachitika pamene Yesu anaitana wophunzira wotsatira kuti amutsatire Iye. Yohane 1:43-45.

“Filipo anamvera lamulolo, ndipo pomwepo anakhalanso wantchito wa Khristu. Filipo anamuitana Natanayeli.”— *The Desire of Ages*, p. 139.

b. Kodi tingaphunzire chiyani pa zimene Khristu anachita pogonjetsa kukaikira kwa Natanayeli? Yohane 1:46-49.

“Pamene Natanayeli anayang’ana Yesu, iye anakhumudwa. Kodi munthu ameneyu, amene anali ndi zizindikiro za kuvutika ndi kusauka, angakhale Mesiya? Komabe Natanayeli sakanatha kusankha kumkana Yesu, chifukwa uthenga wa Yohane unamuthandiza kukhudzika mtima.

“Panthawi imene Filipo anamuitana iye, Natanayeli anali atachoka n’kupita kutchireko kuti akasinkhesinkhe zimene Yohane analengeza komanso za maulosi onena za Mesiya. Iye anapemphera kuti ngati amene analengezedwa ndi Yohane anali mpulumutsi, ichi chidziwike kwa iye, ndipo Mzimu Woyera unakhala pa iye ndi chitsimikiziro chakuti Mulungu anayendera anthu Ake ndi kuwadzutsira iwo nyanga ya chipulumutso....

“Yesu anayankha nati kwa iye, Filipo asanakuitane iwe, pokhala iwe pansi pa mkuyu, ndinakuona iwe.’

“Zinali zokwanira. Mzimu wa Mulungu umeneunachitira umboni Natanayeli m’pemphero lake lapayekha pansi pa mkuyu tsopano unalankhula naye m’mawu a Yesu. Ngakhale anali kukaikira, ndi kugonjera ku tsankho, Natanayeli anadza kwa Khristu ndi chikhumbo chowona chofuna choonadi, ndipo tsopano chikhumbo chake chinakwaniritsidwa. Chikhulupiriro chake chinaposa cha iye amene anamubweretsa kwa Yesu. Iye anayankha nati, ‘Rabi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu; Inu ndinu Mfumu ya Isiraeli.’

“Natanayeli akanadalira arabi kuti amutsogolere, sakadamupeza Yesu. Ndikudzera mu kuzionera yekha ndi kuweluzwa yekha kumene kunampanga Iye kukhala wophunzira. Chotero kwa ambiri lerolino amene tsankho limawalepheretsa kuchita zabwino. Zotsatira zikanakhala zosiyana motani nanga ngati ‘anakadza ndi kudzawona’!

“Pamene iwu akudalira chitsogozo cha olamulira a anthu, palibe amene adzafike ku chidziwitso chopulumutsa cha choonadi. Mofanana ndi Natanayeli, tiyenera kuphunzira mawu a Mulungu patokha, ndi kupemphera kuti mzimu woyera utiunikire. Iye amene anaona Natanayeli pansi pa mtengo wa mkuyu adzationa ife m’ malo obisika a pemphero. Angelo ochokera ku dziko la kuunika ali pafupi ndi awo amene modzichepetsa amafunafuna chitsogozo chaumulungu.”—*Ibid.*, pp. 139–141.

a. Kodi Khristu anamulonjeza chiyani Natanayeli—ndipo nchifukwa chiyani? Yohane 1:50, 51.

“[Potengera Yohane 1:50, 51.] Apa Khristu moonekeratu akunena kuti, M’mphepete mwa Yordano miyamba inatseguka, ndipo Mzimu anatsikira pa Ine monga nkhunda. Chochitika chimene chija chinali chizindikiro chabe kuti ndine Mwana wa Mulungu. Ngati mukhulupirira mwa Ine chomwecho, chikhulupiriro chanu chidzafulumizitsidwa. Mudzaona kuti kumwamba kwatseguka, ndipo sikudzatsekedwa konse. Ndatsegulira inu. Angelo a Mulungu akukwera, akusenza mapemphero a osowa ndi opsinjika mtima mkupititsa kwa Atate wakumwamba, ndi kutsika, kubweretsa madalitso ndi chiyembekezo, kulimba mtima, chithandizo, ndi moyo kwa ana a anthu.”— *The Desire of Ages*. pp. 142, 143.

b. Kodi chimachitika ndi chiyani pamene tamulandira Khristu? Yohane 4:14; Chivumbulutso 22:17.

“Pamene wina walandira chowonadi m’chikondi cha choonadichi, adzasonyeza ichi mwa kukopa kwa kachitidwe kake ndi kamvekedwe ka mawu ake. Iye amadziwikitsa zimene iye mwini anazimva, kuziona, ndi kuzigwira za mawu a moyo, kuti ena akhale ndi chiyanjano ndi iye mwa chidziwitso cha Khristu. Umboni wake, wochokera ku milomo yokhudzidwa ndi khala lamoto la pa guwa la nsembe, uli choonadi ku mtima womvera, ndipo umagwira ntchito ya chiyeretso pa khalidwe....

“Mulungu akanatha kufikira cholinga chake populumutsa ochimwa popanda thandizo lathu; koma kuti ife tikhale ndi makhalidwe ngati a Khristu, tiyenera kutenga nawo gawo mu ntchito yake. Kutu tilowe mu chisangalalo Chake—chisangalalo cha kuona miyoyo yawomboledwa ndi nsembe Yake—tiyenera kutenga nawo mbali mu ntchito Zake za chiombolo chawo.”— *Ibid.*, p. 142.

6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

1. N’cifukwa ciani Yohane M’batizi anaitanidwa kukakhala ku chipululu?
2. Kodi tingatsatire bwanji moyo wa Yohane Mbatizi pa moyo wathu?
3. Kodi tingaphunzire chiyani kuchokera kwa Yohane ndi Andireya atakumana ndi Yesu?
4. Kodi chilengezo choyambirira cha Natanayeli chingatilimbikitse motani?
5. Kodi chimasonyeza m’chiyani ngati chikhulupiriro changa mwa Khristu ndi chenicheni kapena ayi?

UKWATI KU KANA

VESI LOLOWEZA: “Chilichonse chimene anena kwa inu, chitani” (Yohane 2:5, gawo lomaliza).

Zowelenga Zoonjezera: *The Desire of Ages*, pp. 144–153;
Messages to Young People, pp. 403–418

“Yesu anayamba ntchito yokonzanso poyandikirana mwa chifundo kwambiri ndi umunthu.”—
The Desire of Ages, p. 150.

1. CHIYAMBI CHA UTUMIKI WA KHRISTU

Loyamba, Jan 12

a. Kodi Yesu anayambira kuti utumiki wake padziko lapansi? Yohane 2:1, 2.

“Yesu sanayambe utumiki Wake ndi ntchito ina yaikulu pamaso pa a Sanhendrini ku Yerusalemu. Pamsonkhano wa pakhomu m’udzi waung’ono wa ku Galileya mphamvu Yake inaperekedwa kuonjezera chisangalalo cha phwando laukwati. Kotero Iye anasonyeza chifundo chake ndi anthu, ndi chikhumbo chake chotumikira ku chisangalalo chawo. M’chipululu cha mayesero Iye mwini adamwa chikho cha tsoka. Iye anabwera kudzapatsa anthu chikho cha m’dalitso, mwa dalitso Lake kuti ayeretse ubale wa moyo wa umunthu.”—
The Desire of Ages, p. 144.

b. Kodi chinachitika n'chiyani phwando laukwati lisanathe? Yohane 2:3.

“[Mariya] ankafunitsitsa kuti [Yesu] atsimikizire kwa anthu kuti Iye analidi Wolemekezeka wa Mulungu. Iye amkayembekeza kuti pakhoza kukhala mwayi kuti Iye achite chozizwa pamaso pawo.

“Unali mwambo wa nthawiyo kuti mapwando aukwati apitirire masiku angapo. Pa nthawiyo, phwandolo lisanathe kunapezeka kuti vinyo watha. Zimenezi zinachititsa kuti anthu asokonezeke maganizo komanso kuti anong’oneze bondo. Zinali zachilendo kuti vinyo athe pazochitika za zikondwerero, ndipo kusapezeka kwake kunkaoneka ngati kuperewera kwa kuchereza alendo.”— *Ibid.*, pp. 145, 146.

a. Kodi amayi ake a Khristu ananena chiyani, ndipo yankho Lake linali lotani? Yohane 2:3, 4.

“[Kuchokera pa Yohane 2:4] Yankho limeneli, lodzidzimutsa monga momwetikuwonera ife, silinasonyeze kunyoza kapena mwano. Mayankhulidwe a Mpulumutsi kwa amayi Ake anali ogwirizana ndi mwambo wakumeneko. Kayankhidwe kotere kankagwiritsidwa ntchito kwa anthu amene amafunika kuchitiridwa ulemu. Mchitidwe uliwonse wa moyo wapadziko lapansi wa Khristu unali wogwirizana ndi lamulo limene Iye mwini anapereka, 'Lemekeza atate wako ndi amako.' Eksodo 20:12. Pamtanda, m'macitidwe ake otsiliza a cifundo kwa amayi ake, Yesu analankhulanso nawo mofanana, pamene amawapereka ku chisamaliro cha wophunzira wake wokonedwa koposa. Ponse pawiri pa phwando laukwati ndi pamtanda, chikondi chosonyezedwa mu kamvekedwe ka mau ndi mmayang'anidwe ndi mmachitidwe zinatanthauzira mawu Ake.”— *The Desire of Ages*, p. 146.

b. Kodi amayi a Khristu ananena chiyani kwa anthu amene anali kutumikira—ndipo kodi mawu amenewa akugwiranso ntchito motanikwa ife lerolino? Yohane 2:5.

“[Otsatira a Khristu] ayenera kukhala amphamvu mowonjezereka m'kulengeza choonadi pamene akuyandikira ku ungwiro wa chikhulupiriro ndi chikondi cha pa abale awo. Mulungu wapereka chithandizo chaumulungu pazochitika zonse zadzidzidzi zomwe chithandizo cha umunthu sichingathe kuyerekezedwa. Iye amatipatsa Mzimu Woyera kutithandiza mu vuto lililonse, kulimbitsa chiyembekezo chathu ndi chitsimikizo, kuunikira malingaliro athu ndi kuyeretsa mitima yathu. Iye akutanthauza kuti zipangizo zokwanira zidzaperekedwa kuti igwiridwe ntchito ya mapulani ake. Ndikukuuzani kuti mufunefune uphungu kwa Mulungu. Mufunefuneni ndi mtima wonse, ndipo 'chilichonse chimene anena kwa inu, chitani. Yohane 2:5.’”— *Testimonies for the Church*, vol. 6, pp. 414, 415.

c. Kodi Yesu anauza wotumikira pa ukwatiwo kuti achite chiyani? Yohane 2:6-8.

“Pafupi ndi khomo panali mitsuko yamadzi isanu ndi umodzi ikuluikulu yamyala, ndipo Yesu anawuza atumiki aja kuti aidzaze ndi madzi. Izo zinachitidwa. Ndiye pamene vinyo anafunidwa kuti agwiritsidwe ntchito nthawi yomweyo, Iye anati, 'Tengani tsopano, ndipo mupite nawo kwa kazembe wa phwando.' M'malo mwa madzi amene zotengerazo zinadzazidwa, munatuluka vinyo.”— *The Desire of Ages*, p. 148.

a. Pamene vinyo anaperekedwa kwa anthu, kodi kazembe wa phwandolo analankhula chiyani? Yohane 2:9, 10.

“Kazembe wa phwando komanso oitanidwawo sankadziwa kuti vinyo watha. Atalawa yemweotumikirawo anabweretsa, Kazembe wa mphwandoyo adazindikira kutivinyoyo anali opambana kwambiri kuposaamene iye adamwapo kale, ndipo ndiwosiyana kwambiri ndi yemwe analandira kumayambiriro kwa phwando.”— *The Desire of Ages*, p. 148.

b. Kodi ndi mtundu wanji wa vinyo amene Khristu anapeleka? Yesaya 65:8.

“Vinyo amene Khristu anapereka paphwando, ndi amene anapereka kwa ophunzira monga chizindikiro cha mwazi wake, anali madzi ofinyidwa ku mphesa. Mneneri Yesaya akunena za zimenezi pamene akunena za vinyo watsopano ‘m’tsango,’ nati, ‘Musamuwononge; pakuti m’menemo muli dalitso. Yesaya 65:8....

“Vinyo wosasasa amene Iye anapereka kwa oitanidwa paukwati anali chakumwa chokoma ndi chotsitsimusa. Zotsatira zake zinali kupangitsa kukoma kwake kukhala kogwirizana ndi chilakolako chachakudya chopatsa thanzi.”—*Ibid.*, p. 149.

c. Kodi Malemba amati chiyani za vinyo wosasa? Miyambo 20:1; 23:29-35.

“Anali Khristu amene m’Chipangano Chakale anapereka chenjezo kwa Aisrayeli, ‘Vinyo achita chiphwete, chakumwa chaukali chisokosa; wosochera nazo alibe nzeru.’ Miyambo 20:1. Ndipo Iye mwini Sadapereke chakumwa choterocho. Satana amayesa anthu kuti azigwiritsa nchito zinthu zomwe zingasokoneze kulingalira ndi kufooketsa malingaliro auzimu, koma Khristu amatiphunzitsa kubweretsa chikhalidwe chonse pansu pa kumvera. Moyo wake wonse unali chitsanzo cha kudzikana yekha. Kuti athetse mphamvu ya chilakolako cha chakudya, Iye anavutika m’malo mwathu chiyeso choopsa kwambiri chimene anthu angapirire. Anali Khristu amene analamula kuti Yohane M’batizi asamwe vinyo kapena chakumwa choledzeretsa. Iyenso ndi Yemwe adapereka lamulo lofanana ndi lomweli kwa mkazi wa Manowa. Ndipo anatemberera munthu amene adzaika botolo ku milomo ya mnansi wake. Khristu sanatsutsane ndi chiphunzitso Chake.”— *Ibid.*

- a. **Kodi ndi zolinga zotani zimene zinakwaniritsidwa kudzera muzinthu ziwiri kupezekapo kwa Khristu ndi chozizwitsa Chakepaphwando laukwati, ngakhale kwa ife lerolino? Yohane 2:11.**

“Khristu amadziwa zinthu zonse; Iye anayang’ana kupyola mumibado kufikira ku m’nthawi yathu ino, ndipo anaona mmene zinthu zidzakhalire kumapeto kwa mbiri ya dziko. Iye anaona anthu zikwizikwi akuwonongeka chifukwa chakumwa vinyo ndi zakumwa zoledzeretsa. Pang’ono ndi pang’ono dziko lidzafika mumkhalidwe wofanana ndi umene unali m’masiku a chigumula chisanachitike. Koma kumwamba kwakweza chizindikiro chachenjezo, kuti anthu atenge chenjezo, ndi kugwirizana ndi Mulungu kuti adzitetzeze. Iye watipatsa zitsanzo za kudziletsa kotheratu, ndipo wapereka malangizo amene, ngati atsafiridwa, padzatulukapo kulengedwa ndi kusungidwa kwa nyonga, luso, ndi chipambano cha ana athu.”— *The Signs of the Times, April 16, 1896.*

- b. **Fotokozani mtundu wakhalidwe losisimusa umene Khristu anausonyeza mu utumiki Wake wonse. Mateyu 11:29.**

“Yesu anayamba ntchito yokonzanso kudzera mukubwera chifupi mwa chifundo ndi anthu. Pamene Iye amasonyeza kulemekeza kwambiri lamulo la Mulungu, anadzudzula khalidwe lodzionetsera la Afalisi, ndipo anayesa kumasula anthu ku malamulo opanda nzeru amene anawamanga. Iye ankafuna kuphwanya zotchinga zomwe zinkalekanitsa magulu osiyanasiyana a anthu, kuti Iye akhoze kubweretsa anthu pamodzi monga ana a banja limodzi. Kupezeka kwake paphwando laukwati kunalinganizidwira kukhala sitepe lakukwaniritsa ichi.”— *The Desire of Ages, p. 150.*

“Yesu anadzudzula kudzikonda m’njira zonse, komabe anali ndi chikhalidwe chotha kulumikizana ndi anthu. Iye anavomereza kucherezedwa ndi magulu onse, kuyendera nyumba za olemera ndi osauka, ophunzira ndi osadzindikira, ndi kufuna kukweza maganizo awo kuchokera ku mafunso a zinthu zawamba za mmoyo kupita ku zinthu zauzimu ndi zamuyaya. Iye sanapereke chilolezo cha chitayiko, ndipo panalibe mthunzi wa makhalidwe a dziko umene unaipitsa khalidwe Lake; komabe adakondwera ndi zochitika za chisangalalo chopanda zoipa, ndipo mwa kupezeka Kwake adavomereza kusunghanako. Ukwati wa Ayuda unali chochitika chochititsa chidwi, ndipo chimwemwe chake sichinali chosakondweretsa kwa Mwana wa munthu. Kudzera mu kupezeka pa phwando limeneli, Yesu analemekeza ukwati monga dongosolo laumulungu.”— *Ibid., pp.150, 151.*

- a. **Kodi tiyenera kuphunzira chiyani pa chitsanzo cha Khristu chimene chimamusiyanyitsa Iye mosiyana ndi atsogoleri achipembedzo amasiku Ake? Miyambo 18:24.**

“Utumiki wa Khristu unali wosiyana kwambiri ndi wa akulu Achiyuda. Kulemekeza kwawo kwa chikhalidwe ndi miyambo kunawononga ufulu weniweni wa kuganiza kapena kuchitapo kanthu. Iwo anakhala ndi mantha osalekeza omaopa kudetsedwa. Kuti apewe kuyanjana ndi ‘odetsedwa,’ amadzimatula, osati kwa amitundu okha, komanso kwa anthu ambiri a mtundu wawo, osafuna kuwapindulira kapena kuwapindura kukhala abwenzi awo. Kudzera mu kulimbikira za nkhani zimenezi, iwo anachepetsa malingaliro awo ndi kufupikitsa njira ya moyo wawo. Chitsanzo chawo chinalimbikitsa kudzikuzana ndi kusalolerana pakati pa magulu onse a anthu.”— *The Desire of Ages*, p. 150.

- b. **Kodi cholinga chathu chikhale chiyani m'mayanjano onse? Miyambo 11:30.**

“Titha kuwonetsa chidwi zikwi chaching'onochingono m'mawu achikondi ndi mukuyang'ana kwachifundo, zomwe zidzawaliranso pa ife. Akhristu osaganizira ena amaonesera kudzera mukunyozero kwawo zaena kuti sali olumikizana ndi Khristu. Ndi zosatheka kukhala mu umodzi ndi Khristu koma kukhala opanda chifundo kwa ena ndi kuiwala za ufulu wawo.

“Tonse tiyenera kukhala mboni za Yesu. Mphamvu ya chiyanjano, yoyeretsedwa ndi chisomo cha Khristu, iyenera kukuzidwa mu kupindula miyoyo kwa Mpulumutsi. Lolani kuti dziko liziona kuti sitili otangwanika ndi chisamaliro cha ife eni mwa undekha, koma kuti Ife timakhumba ena kugawana nafe madalitso ndi mwayi. Awonetseni kuti chipembedzo chathu sichimatipangitsa kukhala opanda chifundo kapena ofuna zathu zokha. Lolani onse amene amadzinenera kuti apeza Khristu atumikire monga Iye anachitira pothandiza anthu. Sitiyenera konse kupereka ku dziko malingaliro abodza akuti Akhristu ndi anthu achisoni, osasangalala.”— *The Adventist Home*, p. 428.

1. Fotokozani zipatso zauzimu zobalidwa kudzera mu chozizwitsa cha Khristu ku Kana.
2. Fotokozani ubale umene unalipo pakati pa Khristu ndi amayi Ake.
3. N'chifukwa ciani kazembe wa phwandolo anaonetsa kudabwa?
4. Kodi ndi vinyo wotani amene moyenerera amaimira mwazi wa Khristu?
5. Pamapwando, kodi tiyenera kukumbukira chiyani pa chitsanzo cha Yesu?

YESU MU KACHISI

VESI LOLOWEZA: “Koma Yehova ali M’kachisi wake wopatulika; ndipo dziko lonse lapansi likhale chete pamaso pake” (Habakuku 2:20).

Zowelenga zoonjezera: *Testimonies for the Church*, vol. 5, pp. 491–500.

“Malo a mpingo akuyenera kukhala ndi ulemu wopatulika.”— *Testimonies for the Church*, Vol. 5, p. 494.

1. KACHISI ADETSEDWA

Loyamba, Jan 19

a. **Fotokozani momwe zinalili mu kachisi wa kuYerusalemu pomwe Khristu amayamba utumiki wake. Yohane 2:13, 14.**

“Pa chaka, Myuda aliyense amayenera kupereka theka la masekeli ngati ‘dipo la moyo wake’…… pambali pa izi ndalama zambiri zinalinso kuperekedwa ngati zopereka za ufulu, kuti zisungidwe ku thumba losungiramo la m’kachisi. Ndipo kunali kuti ndalama zonse za kunja zinayenera kutsinthidwa kupita ku malupiya otchedwa masekeli a m’kachisi, omwe anali olandirika pa ntchito ya utumiki wa m’kachisi. Kusintha ndalamako kudatsekula makomo ku khalidwe la chinyengo ndi lolanda, ndipo izi zidakulira kufika pochotsa ulemu, ndipo izi zinali ngati njira zopezera ndalama kwa aseme.

“Ogulitsawo amawonjezera mitengo yogulitsira nyama namagawana phindu lake ndi aseme komanso atsogolerii, omwe mukutero amazilemeretsa okha mmmalo mwa anthu.”—*The Desire of Ages*, p. 155.

b. **Kodi izi zinakhudza bwanji utumiki wa m’kachisi? Ezekeili 22:26 (mbali yotsiriza).**

“Mu nthawi ya paskha, nsembe zambiri zinali kuperekedwa, ndipo ndalama za zogulitsa za m’kachisi zinali zambiri koposa. Zotsatira zake pamakhala chisokonezo, malo mwa kachisi opatulika wa Mulungu, malowo anayamba kukhala ngati mtsika wa nyama chifukwa cha phokoso la nyama. Munali phokoso la kunenelera malonda, kulira kwa ng’ombe, nkhusa, nkhusa pamodzi ndi kulira kwa malupiya ndi mikangano yoonetsa kusamvesetsana pa malonda. Chisokonezochi chinali chachikulu kotero kuti opembeza amasokonezedwa, ndipo mawu omwe amayenera kupita kwa wa Mwambamwamba anali kumizidwa mu phokoso lomwe linali m’kachisimo.”—*Ibid.*

- a. **Kodi Mulungu amawatenga motani malo omwe Iye amaonetsera kupedzeka kwake-ndipo langizo lake loyamba linali lotani pa Phiri la Sinai? Ekisodo 3:1–5; 19:12, 13.**

“pamene Ambuye adatsikira pa Phiri la Sinai, malowo adayeretsedwa ndi kupezeka kwake....ili ndi phunziro kuti paliponse pomwe Mulungu amapezeka malowo amakhala oyeru”—*The Desire of Ages*, pp. 155, 156.

- b. **Kodi Yesu anachita chiyani kutsatira pa kuipitsidwa kwa kachisi? Yohane 2:15, 16.**

“Pamene Yesu analowa m’kachisi, adayang’ana ponseponse. Adaona malonda achinyengo. Adaona nkhwawa za osauka, omwe amaganiza kuti popanda kukhetsa mwazi palibe kukhululukidwa ku machimo awo. Adaona bwalo la kunja litasandulika malo ochitira malonda odetsedwa. Malo opatulika adasandulika malo ochitira malonda.”—*Ibid.*, p. 157.

“Akutsika pa makhwerelo, adakweza mwamba nkwapulo wa zingwe zomwe zinaunjikidwa polowera. Iye adalamulira ogula kuti achoke pa malo akachisiwo. Mu nthawi yoyamba Iye adagubuduza matebulo otsinthirapo ndalama mwa mphavu ndi mosanyengelera. Malupiya anataika pansu akuchita phokoso. Palibe yemwe anamufusa za ulamuliro wakewu. Yesu sadawakwapule ndi nkwapu koma ka nkwapu komwe kadali m’manja mwake kamaoneka ngati lupanga la moto. Akulu akulu a m’kachisi, alembi, mavenda ndiso ogulitsa ng’ombe, pamodzi ndi nkhusa ndi abulu awo, anathawa pa malowo kuopa kuweruzidwa ndi kupezeka kwake.”—*Ibid.*, p. 158.

- c. **Kodi kuyeretsedwa kwa kachisi ndi Yesu kumatanthauzanji? Malaki 3:1–3.**

“Mabwalo a kachisi ku Yerusalemu, ozadzidwa ndi malonda onyasa odetsedwa, amaimirira kachisi wa mtima, odetsedwa ndi zikhumbitso zoipa komanso malingaliro osalungama. Poyeretsa kachisi kuchosa ogulitsa ndi ogula aku dziko, Yesu adaonetsa cholinga chake choyeretsa mtima kuuchotsera zodetsa – za m’dziko, zilakolako za thupi, zizolowezi zoipa zomwe zimaononga moyo.”—*Ibid.*, p. 161.

- a. **Kodi cholinga cha Mulungu pokhazikitsa kachisi pakati pa anthu ake chidali chiyani? Ekisodo 25:8.**

“Kachisi yemwe adamangidwa kuti Mulungu akhalemo, adapangidwa kuti akhale phunziro kwa Israeli ndiso ku dziko. Kuyambira nthawi zosayamba, chinali cholinga cha Mulungu kuti cholengedwa chilichonse chikhale mokhalamo Mlengi kuyambira serafi woyera ndi wowala mpakana munthu.”—*The Desire of Ages*, p. 161.

- b. **Kodi n’chifukwa chiyani okhulupirira akutengedwa kukhala kachisi wa Mulungu? Ndipo tikuyenere kuchitanji mwa mtima wonse kuti kachisiyu akhalebe wopatulika? 1 Akorinto 3:16, 17; Yesaya 57:15.**

“Chifukwa cha uchimo, munthu adaleka kukhala kachisi wa Mulungu. Wodetsedwa ndi kuonongedwa ndi zoipa, mtima sunathenso kuvumbulutsa ulemelero wa umulungu. Koma kudzera mu umulungu wa mwana wa Mulungu, cholinga cha kumwamba chikukwaniritsidwa. Mulungu amakhala mwa anthu, ndipo kudzera mu chisomo chake chopulumutsa mtima wa munthu umakhalanso kachisi wake.”—*Ibid.*

“Ngati timakhulupirira kuti chimaliziro cha zinthu zonse chili pafupi, ‘kodi tikuyenera kukhala anthu otani? Mu mayankhulidwe a chiyero ndi umulungu.’

“Moyo uliwonse womwe umakhulupirirachoonadi mopanda chinyengo udzakhala mu ntchito zomwezo. Onse adzakhala oona ndi okhulupirika, ndi osatopa pogwira ntchito yobwezera miyoyo kwa Khristu. Pamene choonadi chadzalidwa ndi kuzika midzu m’mitima yawo, pamene adzafunanso kuti achidvale m’mitima ya wena. Choonadi kwambiri chikumasungidwa m’mabwalo akunja. Chibweretseni icho mkati mwa mtima, chichite ufumu m’menemo ndi kulumulira moyo. Mawu aMulungu akuyenera kuphunziridwa ndi kumveredwa, ndipo moyo udzapeza mpumulo, mtendere ndiso Chimwemwe, ndipo udzimbikitsidwa mu zakumwamba; koma pamene choonadi chaikidwa pambali m’moyo, m’mabwalo akunja, moyo sutenthesedwa ndi Malawi a moto ochokera ku ukoma wa Mulungu.”

“Kwa ambiri chipembezo cha Khristu, chikumangochitidwa kwa masiku ena, kapena muzochitika zina ndipo mu nthawi ndi zochika zina chimaikidwa pambali ndi kunyozeledwa. Mfundo za choonadi sizikuyenera kugwira ntchito kwa maola ochepa okha monga pa sabata, kapena mu ntchito zochepa zachifundo, koma chikuyenera kubweretsedwa m’moyo kuti chitsuke ndi kuyeretsa khalidwe.”— *Testimonies for the Church*, vol. 5, p. 547.

- a. **Kodi tikuyenera kuzindikira chiyani za kulephera kwathu kwa kuyeretsa kachisi? Yeremiya 2:22; Yobu 14:4.**
-
-
-

“Palibe munthu pa yekha angathe kuchotsa kuipa kwake komwe kwamanga nthenje mu mtima mwake.”—*The Desire of Ages*, p. 161.

- b. **Kodi ndi chinsisi chanji chomwe chimatiimitsa pamaso pa Mulungu woyera ndi mtima woyeretsedwa? Ezekeieli 36:25–27; Zakariya 3:3–5.**
-
-
-

“Yakobo anali wopalamula pa zomwe anamuchitira Esau; koma adalapa. Tchimo lake linakhululukidwa ndi kusukudwa; ndipo anatha kupirira pa nthawi yomwe Mulungu anazivumbulutsa kuzionetsera kwa iye. Koma anthu amaonongedwa pamene abwera pamaso pa Mulungu mwadala akukakamirabe zoipa zawo. Pakudza kwa Khristu kachiwiri oipa adzathedwa ndi mzimu wa mkamwa mwake,’ ndi kuonongedwa ndi kuwala kwa kudza kwake.’ 2 Atesalonika 2:8. Kuunika kwa ulemmero wa Mulungu, kumene kumapereka moyo kwa olungama, kudzapha ochimwa.”

“Mu nthawi ya Yohane m’batizi, Khristu anali kuti aonekere monga mvumbulutsi wa khalidwe la Mulungu. Ndipo kukhala kwake kunali kuti kuonetsere uchimo wa anthu. Pamene anali kufuna kuti machimo awo ayeretse ndi pomwe amagwirizana naye. Oyera mtima okha ndi omwe angaime naye.”—*Ibid.*, p. 108.

“Khristu yekha ndi yemwe angathe kuyeretsa kachisi. Koma sadzakamiza kuti alowe. Sabwera mu kachisi monga ngati wakale uja; koma akuti, ‘taona ndaima akhomo ndio ndigogoda: munthu akamva mawu anga nakatsekula chitseko, ndidzakhala mwa iye.’ Chibvumbulutso 3:20. Sadzakhala kwa tsiku limodzi lokha; Iye akuti, ‘ndidzakhala mwa iwo ndikuyendayenda mmwemo..... ndipo adzakhala anthu anga.’ ‘Adzachotsa zoipa zathu; ndi kuzitaya pansu pa nyanja.’ 2 Akorinto 6:16; Mika 7:19. Kupezeka kwake kudzayeretsa ndi kupatula moyo, kuti ukhale kachisi wa moyo wopatulikira Ambuye, ndi mokhalamo Mulungu mwa mzimu.’ Aefeso 2:21, 22.”—*Ibid.*, pp. 161, 162.

“Pamene Yesu adakali kutumikira m’kachisi m’mwamba, adakalibe kutumikira mpingo pa dziko kudzera mwa mzimu wake.”—*Ibid.*, p. 166.

- a. **Kodi ndi motani momwe Mulungu amawawerengerera mulandu atsogoleri a anthu ake amene amapeputsa malo a nyumba yake yopatulika? Habakuku 2:20; Ezekieli 44:23.**

“Malo akachisi wa Mulungu akuyenera kukhala opatulika. Koma pofuna kupeza phindu zonsezi zinaiwalidwa.”

“Asemble ndi atsogoleri anaitanidwa kukhala omuilira Mulungu ku dziko lonse; adayenera kuti azudzulepo za kuonongedwa kwa kachisi. Adayenera kupereka kwa anthu chitsanzo chanzero ndi chifundo.”—*The Desire of Ages*, p. 156.

“Ndizoonza ndithu kuti ulemu wa mkachisi wa Mulungu watha. Zinthu ndi malo opatulika sizikulemekezedwanso; woyera ndi wamkulukulu sakuyamikidwa.... Mulungu adapereka malamulo, angwiro ndi acindunji kwa anthu ake akale. Kodi khalidwe lake latsintha? Kodi Iye si ndiye Mulungu wa mphamvu ndi wamkulu olamulira kumwamba? Kodi sizingakhale zabwino kuti kawirikawiri tiziwerenga malangizo omwe aheberi adapatsidwa ndi Mulungu, kuti ife amene tili ndi kuunika kuti titengereko ulemu wa m’kachisi wa Mulungu?”—*Testimonies for the Church*, vol. 5, pp. 495, 496.

- b. **Fotokozani chipambano chomwe chimapezeka mu mphamvu za Khristu. Mateyu 5:8; 1 Yohane 3:1–3.**

“Ndikuitanira wina aliyense yemwe amati ndi mwana wa Mulungu kuti asaiwale choonadi chachikulu chotere, kuti tikufunika mzimu wa Mulungu m’kati mwathu kuti tikalowe m’mwamba, ndi ntchito ya Khristu kunja kwathu kuti atipatse chilolezo pa cholowa chamuyaya.”—*Testimonies to Ministers*, p. 442.

5. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

Lachisanu ndi chimodzi, Jan 24

1. **Kodi ndi ndani omwe anali otsogolera malonda oipa m’kachisi?**
2. **Kodi tikuyenera kukhala ndi ganizo lotani pamene tikudza pamaso pa Mulungu?**
3. Fotokozani kufunika kwa uzimu komwe kachisi wa ku Yerusalemu adayenera kukhala nawo.
4. **Kodi Khristu amalenegeza chiyani poyeretsa kachisi?**
5. **Kodi kachisi wathu wa mtima woipa angayeretsedwe bwanji**

Zopereka zoyamba zapasabata

Sabata, Febuluwale 1, 2025



CHITHANDIZO CHA NGOZI ZOGWA MWAZIZIDZI PA DZIKO LONSE

Sitingafunse za nkhondo, ndi mbiri za nkhondo, ngozi zoopsa kwambiri, chilala, madzi otsefukira, mphepo ya mkuntho, zibvomerezi, moto, ndi miliri zikuchulukira pa dziko lonse lapansi ndi changu chachikulu kwambiri- zonsezi zili zongokwanitsa maulosi a m’Baibulo amene timawawerenga. Zoonadi, mungozi zonsezi, tikhonza kumaona bwino lomwe za kuyandikira kwa Mulungu kudza ku dziko lapansi. Anthu ochuluka zikwi zikwi amazunka kwambiri ndi zovuta zoopsazi, ndipo chifukwa chazimenezi akuitanira chithandizo chosiyanasiyana kuchokera kwa akazembe a Yesu Khristu kuti apereke mankhwala ochilitsa a ku giliyadi.

Mavuto opweteka kwambiri awa, A gawo loona umoyo wabwino wa anthu la ku GC lakhala likugawa madalitso amene amaperekedwa kuchokela mu chuma cha zopereka zathu chimene chimatimizidwa ndi inu, abale athu odzungulira pa dziko lonse. Zoperekazi zimatimizidwa mu njira yapadera ypawekha kuti ikafikile zotsowazi, komanso kudzera mu njira ya zopereka za pa Sabata loyamba. Okonedwa abale ndi alongo zopereka zanu zakhala zikutumikira monga thandizo kwaiwo amene analuza pokhala pawo mu ngozi zachilengedwe zogwa mwazizizi; zakhala zikuthandizira zokudya kwa mabanja ambiri mazana mazana ndi kutsamalira ana amasiye ndi akazi amasiye, powafikitsira chitsamaliro ndi chithandizo kwa iwo. Zopereka zimenezi zakhala zikuthandizira makolo mukupedza mbewu zoti adzale ndi kumadyetsa mabanja awo kapena kuyamba business yaing’ono ndi kuti anthu ambiri osawelengeka achikhulupiriro chathu azitha kupedza mwayi opedza ndalama ndi ntchito imene kwa iwo ikanakhala yotsatheka kupedzeka kwaiwo.

Tithokoze Mulungu kuti mu nthawi ino ya mavuto, anthu ambiri akhala akukhudzika kuti ayike zopereka zawo pa guwa la Nsembe la Ambuye. Mmallo mwa iwo amene akuthandizidwa, tikukuthokozani kwambiri zedi!

Komano ngakhale zili chomwechi, zotsowazi sizimatherapo mmalo mwake, zikuchulukila kwambiri tsiku ndi tsiku, chotelo zopeleka zanu zimathandiza kwakukulu zedi.

“Mtanda wa khristu ukudandaulira kuolowa manja kwa otsatila aliyense wa Mpulumutsi odala. Mfundo imene ikuonetseredwa apapa ndi yopereka, pakupereka. Zinthu izi, pochitika mmafuno abwino ndi muntchito za moyo wa chikristu.” – ***Counsels on Stewardship, P. 14.***

Lero pamene mukupereka zopereka zanu zapadera za Sabata loyamba, chonde chitani mwakuthekera kwanu kuti mulemekeze Mulungu wanu. Kaya ndi zochepe kapena ndi zambiri, zonsezo zikhonza kuchita mbali yake yaikulu. Kuchokera ku chuma cha chikondi chogawidwachi, tidzakhala tikupitiliza kugwawa madalitso kwa abale athu pa dziko lonse lapansi. “Iye amene amapereka kwa anthu amakhala akudalitsa ena, ndipo amakhala adalitsikanso iye mwini kumuyeso wambiri” (Ibid., p. 13) Ambuye Mulungu wathu akudalitseni kopotsa!

Kuchokera ku nthambi yoona za umoyo wa anthu ku likulu la mpingo.

YESU NDI NIKODEMO

VESI LOLOWEZA: “Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, Indetu, ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu” (Yohane3:3).

Zowelenga zoonjezera: Steps to Christ, pp. 67-75.

“Kasupe wa mtima ayenera kuyeretsewa msinje usanakhale oyera. Iye amene akuyetsa kupita kumwamba posunga malamulo, akuyesa chosateka.” – *The Desire of Ages*, p. 172

1. MUNTHU WOTCHUKA AFUNAFUNA YESU

Loyamba, Jan 26

a. Kodi Nikodemu anali ndani, nanga ndi motani mmene amaoneledwa mmaso mwa anthu? Yohane 3:1, 10.

“Nikodemu anali ndi udindo waukulu wodalilika mufuko la chiyuda. Anali ndi maphunziro apamwamba, ndi matalenti akhalidwe lapamwamba osati lachisawawa, ndipo anali membala olemkezeka munkhosolo ya dziko...Ngakhale anali wachuma, ophunzira, ndi olemkezeka, iye anakhala okopeka mtima mwadzidzidzi ndi munthu wodzichepetsa waku Nazareti.” – *The Desire of Ages*, p. 167.

“Anali Mfalisi weniweni wodzitsata, ndi womazitamandira iye mwini pa ntchito zake zabwino. Ndipo iye amatamandidwaponse pa ntchito zake zabwino ndi zachifundo zimene amathandizira nazo mautumiki akukachitsi, ndipo amadzimva kukhala opindula kukondela kwa Mulungu.” – *Ibid.*, p. 171

b. Kodi ndi ola liti limene Nikodemu ananyamuka ndi kukakumana ndi Yesu? Yohane3:2 (mbali yoyamba).

“Pakhala ndi kudzindikira pa kafukufuku yemwe anafunsa zokhudzana ndi malo amene Mpulumutsi angakapumile muphiri la azitona, iye anadikilira mpakana mzinda utakhala bata, ndipo kenako anayamba kumutsaka iye.” – *Ibid.* p.168.

a. Kodi ndi chani chimene chikuonetsa kumvetsetsa kwa chikondi kwa Khristu mukumulandira mlendo wake mu maola otaika kwambiri autsiku? Masalmo 31:20, 21.

“[Nikodemo] anafunitsitsa zedi kukambilana ndi Yesu, komano anazibitsa posamafuna iye moonekela. Zikanakhala zinthu zochotsa ulemu kwambiri kuti mtsogoleri wa chiyuda aziphatikye yekha molumikizana ndi mphunzitsi wosachuka. Ndipo ulendo wake ukanakhala kuti unadziwika ndi gulu la chisanihedrini, zikanamuputira iye mavuto achitonzo ndi kutsalidwa. Iye analingalira kuti akumane naye mwa chinsinsi, anachita izi potengela kuti ngati angapiteko moonekela, anthu ena akhonza kutsatira chitsanzo chake.” – *The Desire of Ages*, p. 168.

b. Fotokozani mmene Nikodemo anayambila kukambilana kwake ndi Yesu? Yohane 3:2.

“Nikodemo anazimva kukhala ndi mantha achilendo, pamaso pa Khristu, ndipo anayesetsa kudziibitsa pansu pa kuzilimbitsa ndi ulemu. Iye anati, ‘Mphuzitsi,’ ‘Ife timadziwa kuti inu ndi Mphuzitsi ochokela kwa Mulungu: popedza palibe munthu amene angachite zozizwa zotele zimene inu mukuchita, pokhapokha ngati Mulungu sali ndi iye.’ Kudzera mukulankhula za mphatso zotsowa za khristu monga Mphunzitsi, komanso ndi mphanvu zake zodabwitsa zochitila zozwizwa, iye amaona kuti akukonza njira yoti akhale ndi kulankhulana naye kwabwino. Mawu ake anakonzedwa kuti awonetse ndi kuitanitsa chidaliro; komano amaonetsa muzenizeni zake kusakhulupirira. Iye samamubvomereza Yesu kuti ndi Mesiya, amangoti ndi mphunzitsi chabe ochokela kwa Mulungu.” – *Ibid.*

c. Kodi ndi ganizo lanji limene Khristu mwadzidzidzi anadabwitsa nalo Nikodemo? Yohane 3:3.

“Mmalo molandira moni waulemu oteleyu, Yesu anaika maso ake pa iye wolankhulayo, monga ngati kuwelenga moyo wake wonse. Ndipo kudzera mu nzeru zake zopandamalire iye anaona munthu pamaso pake wofunafuna choonadi. Ndipo iye anadziwa cholinga chakuyendeledwa kotele, ndipo ndi khumbo lofuna kukudza kukhudzika kumene kunali pa malingaliro a iye amene amamunvetsera, Iye anangolankhula mwa chindunji, ndi kunena mwakachetechete, komano mwa chikondi, ‘Indetu, Indetu, ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwa tsopano, sakhonza kuona ufumu wa Mulungu.’ Yohane 3:3.

“Nikodemu anabwera kwa Ambuye poganizira kuti alowe mukukambirana ndi iye, komano Yesu anaika poyera mfundo za madziko achoonadi.” – *Ibid*, pp. 168-171.

a. Kodi ndi motani mmene Nikodemo anayankhila ku zimene Khristu anamuuza kuti akusoweka- ndipo monga iye, kodi ndi chifukwa chani ife tonse tikusoweka chochitika chakubadwanso mwatsopano? Yohane3:4-8.

“Chitsanzo cha kubadwanso mwatsopano, chimene Yesu anachigwiritsa ntchito, sichinali chosaziwikiratu kwa Nikodemo. Anthu otembenuka ndi kupita kuchikhulupiriro cha a Israeli kawirikawiri amafanizidwa ndi ana oti angobadwa kumene. Chotelo iye samayenera kunva mawu a Khristu ndi kuwatenga ngati ndi ongozewela achibwana. Komano chifukwa cha chibadwidwe chake chabwino chokhala mu Israeli, Iye amadziona yekha kukhala ndi malo otsimikizika muufumu wa Mulungu. Iye amadzinva yekha kukhala otsasowa kusinthika, ndi chifukwa chake anali odabwa pa mawu a mpulumutsi. Iye anakhumudwa chifukwa choti mawu anali kufotokoza pafupifupi za iye. Kunyada kwa mfalitsi kunali kulimbana ndi khumbo loona la kufunafuna choonadi. Iye anadabwa kuti ndi chifukwa chani Khristu analankhula naye monga anachitilamu, posalabadira za udindo wake monga mtsogoleri mu Israeli.

“Podabwitsika ndi udindo umene anali nawo, iye anamuyankha Khristu mmawu ozadizidwa ndi kusiyana ndi zimene khristu amanena, nati`Kodi munthu, angabadwe bwanji iye atakula kale? Monga anthu ena onse ambiri pamene choonadi chodula moyo wakale chabweretsedwa kuchikumbumtima, iye amaonetsera chilungamo choti munthu wachibadwa samalandira konse zinthu za Mzimu wa Mulungu. Mumakhala mulibe mwaiye kanthu kalikonse kamene kamavomera ku zinthu za uzimu; popedza zinthu zauzimu zimazindikilika mwa uzimu.

“Komano Mpulumutsi samayankha ndi chitsutso kuchitsutso ayi. Iye anakwedza mkono wake mwapadera, ndi mwaulemu mwakachetechete, iye anatsindikidza choonadi mu mtima pamodzi ndi chitsimikizo chachikulu, `Indetu, Indetu, ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi mwa Mzimu, sangakhoze konse kulowa muufumu wa Mulungu.” – *The Desire of Ages, p 171.*

b. Kodi ndi liti komanso ndi motani mmene munthu angabadwensho mwa tsopano? Yohane 1:12, 13.

“Mulungu anakondetsetsa dziko lapansi, chotelo kuti iye anapereka mwana wake obadwa yekha, ndi kuti munthu akathe kulumikizana ndi Mulungu. Kudzera mukuyenera kwa Khristu iye akhoza kubwezeletsedwanso kwa Mlengi wake. Mtima wake ukuyenera kukonzedwanso ndi chisomo cha umulungu; iye akuyenera kukhala ndi moyo watsopano ochokera kumwamba. Kusintha uku ndiko kubadwa mwa tsopano, kumene ngati sikuchitika, Yesu anati, `munthu sadzakhonza kuona ufumu wa Mulungu.” –*The Great Controversy, p. 467.*

“Kudzera muchochitika chophweka cha kukhulupilira Mulungu, Mzimu Woyera umatenga malo amoyo watsopano mmoyo mwanu. Mumakhala monga ngati mwana wobadwa mubanja la Mulungu, ndipo iye amakukondani inu monga amamukondera mwana wake.”-*Steps to Christ, p 52*

a. Kodi ndi chiyani chimene chimaonetsera kuyeretsa ndi kukonzanso kumene kumadza ndi kubadwanso mwatsopano? Mariko 16:16 (mbali yoyamba).

“Mphanvu yotsintha ya Mulungu imatha kusintha zidzolowezi zobadwa nazo ndi zotengela kwa ena; popedza chipembedzo cha Yesu ndi chokwedza. ‘kubadwanso’ kumatanthauza kusinthika, kubadwa mwatsopano mwa Khristu Yesu.” – *The Adventist Home, p. 206.*

“Khristu anapanga ubatizo kukhala chidzindikilo cholowela muufumu wake wa uzimu. Iye anapanga ichi kukhala chinthu chofunikira chimene anthu onse akuyenela kuchivomeleza ngati amakhumba kuti adzizdzindikilidwa monga okhala panso pa ulamuliro wa Atate, Mwana, ndi Mzimu woyera. Munthu asanayambekupedza malo okhala mu mpingo, asanathe kudutsa pakhomo polowera pa ufumu wa uzimu wa Mulungu, iye akuyenela kaye kuti alandile kutsindika kwa dzina la umulungu loti, ‘Ambuye ndiye chilungamo chathu.’ Yeremiya 23:6.

“Ubatizo ndi kukana kopatulika kolikana dziko lapansi. Iwo amene anabatizidwa mu maina atatau a Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera, pakulowa kwawo moyo wachikhristu amalalikira poyera kuti iwo atsiya kutumikila Satana ndipo akhalano ziwalo za ufumu wopatulika wolemekedzeka, ana a Mfumu ya kumwamba. Iwo amakhala amvera kulamula koti; ‘Tulukani ndi kupatuka pakati pawo ndi kukhala apadera... ndi kutsakhudza konse kanthu kosakonzeka.’ Ndipo kwaiwo kumakwanilitsidwa lonjedzo loti; ‘Ndipo ine ndizakulandilani inu, ndipo ndizakhala Atate kwa inu, ndipo inu mudzakhala ana anga aamuna ndi akazi, atelo Ambuye wa mphanvu zonse.’ 2 Akolinto 6:17, 18.” – *Testimonies for the Church, Vol. 6, p. 91.*

b. Kodi ndi chiyani chimene chinanenedwa zokhuzana ndi kuipa kwa khalidwe lathu lachibadwa ndi dongotsolo la Mulungu lotisintha ife? Yohane 3:6; Yeremiya 17:9, Aefeso 5:26, 27.

“Ndizosatheka kwa ife, ndi mwaife tokha, kuti tikathawe mu zenje la uchimo mmene ife tinamilamo. Mitima yathu ndi yoipa, ndipo sitingaisinthe tokha... maphunziro, chikhalidwe, kuchita kwa chifuniro, kuyesetsa kwa munthu, zonsezi zili ndi malo ake othekela, komano apa pokha ndi zopanda mphanvu konse. Zikhonza kutulutsa khalidwe looneka lolondola kunjaku, komano sizingasinthe mtima; sizingakhonze kuyeletsa akasupe amoyo. Pakuyenera kukhala mphanvu yomagwira ntchito kuyambira mkati, moyo watsopano ochokela kumwamba, anthu asanatembenuke kuchoka kuuchimo ndi kupita ku chiyero. Mphanvu zimenezo ndi Khristu. Chisomo chake chokha ndi chimene chingafulumizitse zochitika zopanda moyo za moyo, ndi kuzibweretsa kwa Mulungu, ku chiyero.” – *Steps to Christ, p. 18.*

- a. **Kodi ndi uthenga wanji pambuyo pake atumwi amayenela kuulemba okhuzana ndi kusintha kumene kumadza molingana ndi kubadwanso mwatsopano? Agalatiya 2:20; 1 Yohane 2:15-17.**

“Mphanvu zotsintha za Mulungu zimasintha zizolowezi zachibadwa ndi zotengela; popedza chipembezo cha Yesu ndi chokwedza. ‘Kubadwanso’ kumatanthauza kubadwanso mwatsopano mwa khristu Yesu.” – *The Adventist Home*, p. 206.

“[Paulo] anasimikiza mu mtima kuti ngati malingaliro aanthu akanabweretsedwa kukudzindikila nsembe yodabwitsa imene inapangidwa ndi wolemekezeka wa kumwamba, kuzikonda ndi undekha wonse zikanathamangitsidwa kuchoka mumitima yawo. Iye akulondolera malingaliro koyambilira kuudindo umene Khristu anali nawo kumwamba, mu nyumba ya Atate wake; Ndipo mtumwi akumuonetsera iye pamwamba, mu nyumba ya Atate wake; ndipo mtumwi akumuonetsera iye pambuyo pake kuti anatula pansu ulemelero wake, ndi kuzipereka Yekha mwachifuniro kumakhalidwe onse azochitika zozichepetsa amakhalidwe aumunthu, ndi kutenga maonekedwe akapolo, ndi kukhala onvera kufikila imfa, ndipo imfa yake yochititsa manyazi ndi yachitonzo, yonvetsa chisoni zedi, ndi yowawa zedi-imfa yapamtanda. Kodi akhristu angathe kulingalira za chionetsero chodabwitsachi cha chikondi cha Mulungu kwa munthu popanda kukhala ndi nthumadzi ya chikondi ndi kukhala ndi lingaliro loganiza za choona choti ife sindife ayife tokha? Mbuye wotele sakuyenela kutumikilidwa kudzela mukukakamizidwa, muchitsiliro, ndi muzolinga a undekha.” – *Testimonies for the Church, Vol. 4, p. 458.*

“Ndikulankhulani monga Khristu analankhulira kwa Nikodemo; ‘Ukuyenera kubadwanso mwatsopano.’ Iwo amene amalamulilidwa ndi Khristu mkati mwa mtima mwawo amanva kusakhala ndi khumbo lotsatira zochitika zozionetsera za dziko lapansi. Ndipo iwo amatengera kulikonse muyeso wa mtanda, ndi kumachitila umboni nthawi zonse za mfundo za pamwamba ndi zabwino kupotsera iwo amene zochitika za dziko zawadya moyo. Mavalidwe athu, pokhala pathu, machezedwe athu, zonsenzi zikuyenera kuchitila umboni za kuzipereka kwathu kwa Mulungu. Kodi ndi mphanvu zotani zimene zikanawatsata iwo amene akamazinva kuti analeka zonse chifukwa cha Khristu.” – *Ibid, Vol. 5, p. 189.*

6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

Lachisanu ndi chimodzi, Jan 31

1. Chifukwa cha ntchito zake zabwino kodi ndi motani mmene Nikodemo amazionera yekha?
2. Kodi ndi motani mmene Nikodemo anachitila pamaso pa Khristu?
3. Kodi zimatanthauza chiyani kukhala “Obadwanso”?
4. Kodi ndi motani mmene kubadwanso mwatsopano kumachitikira?
5. Kodi ndi kusintha kotani kwa khalidwe kumene kumadza chifukwa cha kubadwanso mwatsopano, ndipo chifukwa chiyani?

KUYENDA KWA MZIMU WOYERA

VESI LOLOWEZA: “Ndipo monga Mose anakweza njoka mchipululu, chotero mwana wa munthu ayenera kukwezedwa; kuti yense wakukhulupilira akhale nawo moyo wosatha mwa iye” (Yohane3:14, 15).

Zowelenga Zoonjezera: Christ’s Object Lessons, pp. 95-102.

“Yang’anani, O! yang’anani kwa Yesu ndikukhala ndi moyo.” Christian Education, p. 76.

1. KUFUNSIKISA KWA KHAMA

Loyamba, Feb 2

a. Kodi ndi funso lanji la Nikodemo limene likuwonesha kuti mtima wake unafewetsedwa? Yohane3:9.

“Yesu ananenetsa kwa Nikodemo: Simkangano womwe udzakuthandize mlandu wako; simtsutso womwe udzabweretse kuunika ku moyo. Ukuyenera kukhala ndimtima watsopano, apo ayi sungathe kuzindikira ufumu wa kumwamba. Siumboni waukuru womwe udzakubweretseni inu mumalo abwino, koma cholinga chatsopano, akasupe atsopano amachitachita. MUYENERA kubadwa mwatsopano. Kufikira kusinthika uku kutachitika kupanga zinthu zonse zatsopano, maumboni amphanvu omwe angaonetsedwe akhala opanda ntchito. Chosowa chili mkati mwanu chilichonse chikuyenera kusinthidwa, apo ayi simungathe kuona ufumu wa Mulungu.

“Awa anali mawu ochititsa manyazi kwambiri kwa Nikodemo...Iye analibe malingaliro auzimu okwanira kuti azindikire thandauzo la mawu a Khristu. Koma mpulumutsi sanakumane ndi mtsutso ndi kutsutsana...

“Kuthwanima kwina kwa choonadi kunali kukulowa mmalingaliro amdindoyu. Mawu a Khristu anamudzadza iye ndi mantha, ndi kumutsogolera iye kuti afunsenso kuti, ‘Kodi zinthu zimenezi zingatheke bwanji? Ndikutsimikiza kwakukulu Yesu anayankha, ‘Kodi uli mphuzitsi wa Israeli, ndipo sudziwa zinthu izi?’ Mawu ake anapereka kwa Nikodemo phunziro lakuti, mmalo mokumva kuphyetsedwa mtima ndi mawu omveka bwino a choonadi, ndikulorera kukhala ouma mtima, Iye anayenera kukhala ndi lingaliro lozichepetsa kwambiri la iye yekha chifukwa cha umbuli wake wauzimu. Komabe mawu aKhristu amalankhulidwa ndi ulamuliro otsindika,ndipo zonse, maonekedwe ndi mawu zinafotokoza chikondi choona chotero kwa iye, kotero kuti iye sanakhumudwitsike pamene anazindikira kusikisisa komwe iye ali nako.” – *Testimonies to Ministers*, pp. 368,369.

a. Kodi ndi muchiyani momwe Afarisi anali kudzikwedzera okha? Luka 18:9-12.

“Ayuda anali oyambirira kuitaniridwa ku munda wampesa wa Ambuye, ndipo chifukwa cha ichi iwo anali odzikwedza komanso odzilungamitsa. Zaka zawo zochulukira za utumiki iwo anazitenga ngati chowayenereza iwo kulandira mphoto yokulirapo koposa ena. Panalibe chinthu chokwiyitsa kwambiri kwa iwo kuposa kulengezetsa kuti amitundu anayenera kuloledwa kukhala ndi mwayi wofanana ndi iwo eni muzinthu za Mulungu.” – *Christ’s Objects Lessons, p. 400.*

b. Kodi Yesu anaonetsera bwanji ntchito ya mzimu woyera mumtima? Yohane 3:8.

“Mphepo imanveka munthambi za mitengo, kugwetsa masamba ndi maluwa; chonsecho ndiyosaoneka, ndipo palibe munthu amadziwa komwe ikuchokera kapena komwe ikupita. Choteronso ndintchito ya Mzimu woyera pamtima. Sizizngafotokozedwe konse kuposa momwe mphepo ingayendere. Munthu sangathe kuchula nthawi yeniyeni kapena malo enieni, kapena kuzindikira zochitika zonse za mundondomeko yakusinthika; koma ichi sichimamusonyeza iye kukhala osasinthika. Kudzera mwa mthenga monga mpepo yosaoneka, Khristu amagwira ntchito mokhazikika pamtima.” – *The Desire of Ages, p. 172.*

c. Kodo ndimotani momwe chithuzithunzi cha umulungu chimakhazikitsidwira mumtima? Yesaya 30:21; Yereimiya 42:3 ; Mateyu16:17.

“Pang’ono ndi pang’ono, mwinanso mosadziwika kwa ochirandira, chilimbikitso chimachitidwa kuti chiusendezero moyo kwa khristu. Izi zimatha kukhala zolandira kuzera mukukangamira pa iye, kudzera mukuwerenga malembo kapena kudzera mukunvetsera mawu kuchokera kwa mlaliki wamoyo. Mwadzidzi, pamene mzimu akubwera ndi kudandaulira kwakukuru kwa chindunji, moyo mwachimwemwe umazipereka okha kwa Yesu. Mwa ambiri ichi chimatchulidwa kusinthika kodabwitsa; koma chimakhala chotsatira cha kudandaulira kwa nthawi yaitali kwa mzimu wa Mulungu-ndondomeko yochitidwa modekha.”—*Ibid.*

“Bvomerezani mitima yanu kuti ifewetsedwa ndi kugonjetsedwa ndi mzimu wa Mulungu. Lolani mmoyo youma ngati myala isukunuke pansu pakugwira ntchito kwa mzimu woyera.” – *Letters and Manuscripts, Vol. 12, Letter 53, 1897.*

a. Kodi ndimotani momwe kugwira ntchito kwa mkati kwa mzimu woyera kumaonetsedwera kunja? Agalatiya 5:22-25.

“Pamene mphepo payokha iliyosaoneka, imatulutsa zotsatira zomwe zimaoneka komanso kunvedwa. Chomwecho ntchito yamzimu pa moyo idzazibvumbulutsa yokha mmachitachita alionse aiye amene wanva mphanvu yake yopulumutsa. Pamene mzimu wa Mulungu watenga ulamuliro wa mtima, umasintha moyo. Malingaliro auchimo amachotsedwa, machitachita oipa amadzudzulidwa; chikondi, kudzichepetsa ndi mtendere zimatenga malo amkwiyo, msanje ndi kulimbana. Chimwemwe chimatenga malo a kukhumudwa, ndipo maonekedwe a nkhope amaonetsera kuunika kwa kumwamba.” – *The Desire of Ages*, p. 173.

b. Kodi ndiliti lomwe munthu amalandira mdalitso wakusinthika? Aroma 10:9, 10, 1 Yohane 1:9.

“Palibe munthu amaona dzanja lomwe limanyamula zothodwetsa, kapena kuona kuunika kukutsika kuchokera kumabwalo akumwamba. Mdalitso umabwera pamene mwachikhulupiriro moyo wazipereka okha kwa Mulungu. Tsopano mphanvu imeneyo yomwe palibe maso a munthu angathe kuiona imalenga munthu watsopano mchifaniziro cha Mulungu.” – *Ibid.*

“Ngati muli ndi mzimu woyera kuumba komanso kukonza mtima wanu tsiku ndi tsiku, tsopano mudzakhala ndikunvetsetsa kopatulika kozindikira khalidwe la ufumu wa Mulungu. Nikodemo analandira chiphuzitso cha Khristu ndipo anakhala wokhulupilira owona.” – *Testimonies to Ministers*, pp. 369,370.

c. Kodi Khristu akuionetsa motani ndondomeko imeneyi? Mateyu 13:33.

“Chotupitsa chosungidwa mu ufa chimagwira ntchito mosaoneka kubweretsa choumbidwa pasi pa ndondomeko yake yakufufumitsa chotero chotupitsa cha choonadi chimagwira ntchito mwachinsinsi, mwakachetechete, mokhazikika, ku kusintha moyo. Zokonda zachibadwa zimafewetsedwa ndi kugonjetsedwa malingaliro atsopano, zolinga zatsopano zimadzalidwa. Muyeso watsopano wa khalidwe umakhazikitsidwa- moyo wa Khristu. Malingaliro amasinthidwa; mphanvu zimazutsidwa kukugwira ntchito munjira yatsopano. Munthu samavekedwa ndi mphanvu zatsopano, koma mphanvu zomwe analinazo zimayeretsedwa. Chikumbumtima chimadzutsidwa. Timadzazidwa ndi makhalidwe omwe amatiyenerereza ife kuchita utumiki kwa Mulungu.” – *Christ’s Object Lessons*, pp. 98, 99.

a. Kodi Yesu analongosola bwanji kupachikidwa kwake komwe kuchitike posachedwa? Yohane 3:14, 15.

“[Potengera Yohane3:14,15] Apa panali pabwalo pomwe Nikodemo amapadziwa pwinobwino. Chizindikiro cha njoka yamkuwa yokwezedwa zinampanga iye kumvesesa bwino utumiki wa mpulumutsi. Pamene anthu a Israeli anali kufa ndi ululu wa njoka za moto, Mulungu anatsogolera Mose kupanga njoka yamkuwa, ndikuika iyo pamwamba mkatikati mwa nsonkhano. Tsopano liwu linamveka kuzungulira msasa wonse kuti onse omwe angayang’ane pa njoka yamkuwa akhala ndi moyo. Anthu amadziwa bwino kuti mwa iyo yokha njoka yamkuwa inalibe mphanvu ya kuwathandiza iwo. Inali chizindikiro cha Khristu. Monga chifaniziro chinapangidwa mofanana ndi njoka zoononga chinakwezedwa pamwamba kumachilitso awo, chotero mmodzi opangidwa mchifaniziro chathupi lauchimo anayenera kukhala mpulumutsi wawo. Aroma8:3.Ambiri a Israeli amautenga utumiki wa zinsembe ngati uli ndi ubwino mwa iwo okha owamasula iwo kutchimo. Mulungu amakhumba kuwaphunzitsa iwo kuti zinalibe mphanvu zoposa njoka yamkuwa. Unali wotsogolera malingaliro awo kwa mpulumutsi. Kaya kumachilitso a mabala awo kapena kukukhululukidwa kwa machimo awo, iwo sakanatha kuzichitira kanthu kena kalikonse kiwo wa okha koma kuwonetsa chikhulupiro chawo mumphatso ya Mulungu. Iwo anayenera kuyang’ana ndikukhala ndi moyo.” – *The Desire of Ages*, pp. 174,175.

b. Ngakhale panali thandizo kodi ndichifukwa chiyani ena amafa? 1 Akolinto 10:9; Ahebri 3:12.

“Ambiri a Israeli samaona thandizo mumankhwala omwe kumwamba kunasankha. Anthu okufa ndi ena oti akufa anawazungulira iwo,ndipo iwo anadziwa kuti, popanda thandizo lakumwamba, imfa yawo inaliyotsimikizika; koma iwo amapitilizabe kudandaula zilonda zawo, ululu wawo, imfa yawo yotsimikizika, kufikira mphanvu zawo zimatha,ndipo maso awo anachita khungu, pamene iwo akanatha kupedza machilitso achanguchangu.” – *Patriachs and Prophets*, p. 432.

c. Ngati tikufuna kupulumutsidwa, kodi tikuyenera kuyang’ana kuti? Ahebri 6:19, 20.

“Zotsatira zoopya za tchimo zngathe kuchotsedwa pokhapokha kuzera muthandizo lomwe Mulungu analikhazikitsa. Aisraeli amapulumsa miyoyo yawo poyang’ana pa njoka yokwezedwa. Kuyang’ana kemeneko kumaphatikizilapo chikhulupiro. Iwo amakhala ndi moyo chifukwa amakhulupirira mawu a Mulungu, ndikudalira mu njira zomwe zinabweresedwa kumachilitso awo. Chotero wochimwa atha kuyang’ana kwa Khristu ndikukhala ndi moyo. Iye amalandira chikhulukiwo kuzera muchikhulupiro mu nsembe yotetezera... Khristu ali ndi mphanvu komanso njira mwa iye yekha yochizira ochimwa wolapa.” – *Ibid.*, p. 431.

- a. Kodi ndiphunziro lanjilimene patapita nthawi linamvetsetsedwa ndi Nikodemo lomwe tikusoweka kulitenga- ndikulisunga nthawi zonse mmalingaliro? Aefenso 2:8; Luka 13:20, 21.

“Kawirikawiri funso limabwera, chifukwa chiyani, tsopano, pali anthu ambiri, ozitchula okhulupirira mawu a Mulungu, omwe mwa iwo simukuoneka kukonzanso mmawu, muuzimu ndi mukhalidwe? Nduchifukwa chiyani kuli ambiri omwe sangathe kupirira kutsutsa kuzolinga ndi madongosolo awo, omwe amaonesa kupsa mtima kodetsedwa, komanso omwe mawu awo ali aukali, ozitamandira, ndi okwiya? Pamaoneka mmoyo mwawo chikondi chomwechomwecho cha undekha zizolowezi zomwezo za kuzikonda, mkwiyo omweomwewo ndi mawu okalipa, zomwe zimaoneka mmoyo wa anthu akudziko. Pali kudzikudza kowonekera, komwenso kwakhazikika mmakhalidwe akuthupi, makhalidwe omwewo amphulupulu kukhala ngati choonadi sichikuziwikilatu kwa iwo. Chifukwa ndichakuti iwo sanatembenuke. Iwo alibe chotupitsa chobisidwa cha choonadi mumtima mwawo. Sichinapatsidwe mwayi wochita ntchito yake. Zizolowezi komanso zikhalidwe zawo zachibadwa za zoipa sizinaperekedwebe kumphanvu zake zosintha. Miyoyo yawo imabvumbulutsa kusowekera kwa chisomo cha Khristu, kusakhulupirira mumphanvu zake zosintha khalidwe.

‘Chikhulupiriro chimadza pakumva, ndi kumvetsera kumawu a Mulungu.’ Aroma 10:17. Malemba opatulika ali chida champhanvu mukusinthika kwa khalidwe. Khristu anapemphera, ‘patulani iwo mchoonadi mawu anu ndichoonadi.’ Yohane 17:17. Ngati aphunziridwa ndikumveredwa, mawu a Mulungu amagwira ntchito mumtima, kugonjetsa khalidwe lililonse losapatulidwa. Mzimu woyera amabwera kutsutsa za tchimo, ndipo chikhulupiriro chomwe chimatumphuka mumtima chimagwira ntchito mwachikondi kwa Khristu, kutifananitsa ife mthupi, moyo ndi mzimu kuchifaniziro chake. Tsopano Mulungu angathe kutigwiritsa ntchito ife kuchita chifuniro chake. Mphanvu zomwe tinapatsidwa zimagwira ntchito kuyambira mkati kufikira kunja, kutitsogolera ife kuyankhula kwa ena choonadi chomwe chinayankhulidwa kwa ife.” – *Chirst Object Lessons, pp. 99,100.*

6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

Lachisanu ndi chimodzi, Feb 7

1. Kodi khalidwe lalikulu la afarisi linali lanji mmatsiku a Khristu.
2. Fotokozani momwe ife timabadwiranso kuchifaniziro cha Khristu.
3. Ndimotani momwe kusinthika kwa mtima kumaonetseredwa?
4. Fotokozani choimilira cha njoka yokwezedwa.
5. Kodi fanizo la chotupitsa likubvumbulutsa bwanji kukula muchisomo cha Mulungu?

YESU NDI YOHANE M'BATIDZI

VESI LOLOWEZA: “Iyeyo ayenera kukula koma ine ndichepe” (Yohane 3:30).

Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, Vol.5, pp. 721-729.

“Yohane m’batizi anatchulidwa ndi mpulumutsi wathu kuti ndi mneneri wamkulu. Komabe ndikusiyana kotani pakati pa mawu amunthu wa Mulungu ameneyu ndi ambiri omwe amazitchula kukhala atumiki amtanda. Pamene anafunsidwa ngati iye anali Khristu, Yohane anazifotokoza yekha kukhala osayenela ngakhale kumasula zingwe za msapato za mbuye wake.” – *Testimonies for the Church, Vol. 5, p. 224.*

1. BVUTO PAKATI PA WOPHUNZIRA

Loyamba, Feb 9

a. Kodi ndi funso lanji lomwe linabuka mwa ophunzira a Yohane ndi Ayuda? Yohane 3:25.

“Ophunzira a Yohane amayang’ana ndi nsanje pa kukula kwa kuchuka kwa Yesu. Iwo anali okonzekera kutsutsa ntchito yake, ndipo sipanadutse nthawi yaikulu iwo asanapedze chochitika. Funso linabuka pakati pa iwo ndi aYuda ngati mwina Ubatizo umathandiza kuyetsa moyo kuchimo; Iwo amalimbikira kuti ubatizo wa Yesu umasiyana kwakukulu ndi wa Yohane. Mosachedwetsa iwo anali mumkangano ndi ophunzira a Khristu zokhuza kakonedwe ka mawu oyenera kugwiritsidwa ntchito kuubatizo, komanso kumapeto kwake kuyenera kwa kubatiza kwa Yesu.” – *The Desire of Ages, p. 175.*

b. Kodi ndimotani momwe ophunzira a Yohane anaonetsera nsanje yawo kuntchito ya Khristu-ndipo ndiyankho lanji loyenera lomwe iye analipereka? Yohane 3:26, 27.

“Yohane mwachibadwa anali ndi zophophonya ndi zofowoka zomwe anthu amakhala nazo, koma kukhuza kwa chikondi chopatulika kunamusintha iye. Iye amakhala mumpweya wosaonongedwa ndiundekeha komanso zikhumbokhumbo, ndimopitirira apo mpweya wa msanje. Iye samaonetsa kugwirizana ndikutsakhutisidwa kwa ophunzira ake, koma amaonetsera momwe iye amanvetsetsera mwabwinobwino ubale wake kwa Mesiya, ndimomwe mwachisangalalo iye anamulandilira Yemwe iye amamukonzera njira.” – *Ibid., p. 179.*

a. Kodi Yohane anaonetsera bwanji kuti iye anamvetsesa utumiki wake? Yohane 3:28, 29.

“Yohane anazifotokoza yekha monga bwenzi lomwe limachita ngati wamithenga pakati pa abwenzi otomerana, kukonzetsera njira ya ukwati. Pamene mkwati wamalandira mwatibwi wake, cholinga cha bwenzi chimakwanilitsidwa. Iye amasangalala muchimwemwe cha onse omwe iye analinawo mukukuza mgwirizano. Chotero Yohane anaitanidwa kuwalondolera anthu kwa Yesu. Ndipo chinali chimwemwe chake kuchitira umboni chipambano cha ntchito ya Mpulumutsi.” – *The Desire of Ages*, p. 179

b. Fotokozani ntchito ya Yohane- ndi yathu. Yohane1:23, 29.

“Poyang’ana mwachikhulupiriro kwa mpulumutsi, Yohane anakulitsidwa kufikira ku nsinkhu wakudzikanzidza yekha. Iye sanafune kukokera anthu kwa iye yekha, koma kukweza malingaliro awo pamwamba ndi pamwamba, kufikira iwo atapumula pa mwana wankhosa wa Mulungu. Iye mwini anali mawu okha ofuula mchipululu. Tsopano ndi chimwemwe iye anachilandira mwachifatso komanso mokondwa, kuti maso aonse atha kutembenukira kukuunika kwa moyo, “Onse omwe ali owona kumaitanidwe awo monga amithenga a Mulungu sadzafuna ulemu wakwa iwo okha. Chikondi chakwa wekha chidzamizidwa mu chikondi cha Khristu. Sipadzakhala makani olepheretsa ntchito yamtengo wapatali ya uthenga wabwino. Iwo adzazindikira kuti ndintchito yawo kuyankhula monga anachitila Yohane m’batizi, ‘onani mwana wankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo ladziko lapansi.’ Yohane1:29. Iwo adzakwedza Yesu, ndipo pamodzi ndi iye umunthu udzakwezedwa. ‘Atelo iye amene ali wantali wotukulidwa, amene akhala mwachikhalire, amene dzina lake ndiye woyera, ndikhala mmalo aatari ndi oyera, pamodzi ndi yense amene ali ndi mtima wozichepetsa ndi mzimu wosweka, kutsisimutsa mzimu wozichepetsa, ndikutsisimutsa mtima wosweka.’ Yesaya 57:15.” – *Ibid.*, pp.179,180.

“Musamafunefune kukondwa ndi ubwino wa inu nokha, koma funani kudziwa ndikuchita chifuniro cha Mulungu. Tiyeni aliyense azifunse, Kodi sindingalozere moyo wina wake kwa mwana wankhosa wa Mulungu, amene achotsa tchimo lake ladziko lapansi? Kodi sindingatonthoze wina wotaya chiyembekezo? Kodi sindingakhale njira yopulumutsira moyo wina kupita mu ufumu wa Mulungu? Tikufuna kuyenda kozama kwa mzimu wa Mulungu mmitima kuti tisakhale kokha ongokwanitsa kutetedza kwa ife tokha chovala choyela, koma kuti tithe kukopa ena kuti maina awo akathe kulembedwa m’buku lamoyo, osadzafufutidwamo.” – *Historical sketches*, p. 140.

a. Kodi unyinji wa anthu unachita nawo bwanji uthenga wa Khristu? Yohane 3:32.

“Ophunzira a Yohane anayankhula kuti anthu onse akubwera kwa Khristu; Koma ndi masomphenya a bwino Yohane anati, ‘Palibe munthu akulandira umboni wake;’ chotero wochepetsetsa anali okonzeka kumulandira iye ngati opulumutsa ku tchimo. Koma ‘iye amene analandira umboni wake anaikapo chizindikiro chake kuti Mulungu ali owona.’ Yohane 3:33.”
– *The Desire of Ages, p. 181.*

b. Ndikwandani komwe mphatso ya mzimu woyera ikuperekedwa? Yohane 3:34.

“Tingathe kulandira kuunika kwa kumwamba pokhapokha ngati tikufuna kutaya undekha. Sitingathe kuzindikira khalidwe la Mulungu, kapena kumlandira Khristu mwachikhulupiriro, pokhapokha titalorera kubweretsa muukapolo lingaliro lililonse kukumvera kwa Khristu. Kwa onse omwe achita ichi Mzimu woyera umaperekedwa kwa iwo opanda muyeso. Mwa Khristu ‘chikhalira chizalo cha Umulungu mthupi, ndipo muli odzadzidwa mwa iye.’ Akolose 2:9, 10, R. V.” – *Ibid.*

c. Ndimotani momwe mfungulo wakulandirila muyeso waukulu wa mzimu woyera unabvumbulutsidwira mopitilira mmalemba? Yohane 14:15-17; Machitidwe 5:32.

“Sitikuyenera kumangoyankhula kokha kuti ndimakhulupilira koma kuchita choonadi. Ndikudzera mukutsatira kuchifuniro cha Mulungu mmawu athu, mmayendedwe athu, mukhalidwe lathu, zomwe zimachitira umboni kulumikizana kwathu ndi iye. Nthawi iliyonse pamene wina wasiya tchimo, lomwe liri kuphwanya kwa lamulo, moyo wake udzabweretsedwa kukufanana ndi lamulo, mukunvera kwangwiro. Iyi ndintchito ya mzimu woyera. Kuunika kwa mawu owerengedwa mosamalitsa, mawu achikumbumtima, kuyesesa kwa mzimu woyera, zimabereka mumtima chikondi chenicheni cha Khristu, yemwe anazipereka yekha nsembe yapumphu kuombola munthu yense, thupi, moyo ndi mzimu. Ndipo chikondi chimaonetsedwa mukunvera. Mzere osiyanitsa udzaonekera bwino bwino ndikusiyantsa pakati pa onse omwe amakonda Mulungu ndikusunga malamulo ake, ndi onse omwe samakonda iye ndiosamala malemba ake.” – *Testimonies for the Church, Vol. 6, p. 92.*

a. Ndichifukwa chiyani chili chofunikira kumvetsetsa khwerero lomwe tikulitenga chifukwa cha Khristu pamene tapanga chiganizo chobatizidwa? Yohane 3:36.

“Kuchotsapo Khristu, ubatizo monga utumiki wina ulionse, uli mwambo opanda phindu.” – *The Desire of Ages, p. 181.*

“Sipakusowekera mtsuso monga wakuti kaya ubatizo wa Khristu kapena wa Yohane umayeretsa ku tchimo. Ndichisomo cha Khristu chomwe chimapereka moyo ku moyo.” – *Ibid.*
 “Ndikudzela mwa Khristu mokha momwe umuyaya ungapezedwe. Yesu anati: ‘ Iye wokhulupirira pa mwana ali nawo moyo wosatha: ndipo iye amene sakhulupirira mwana alibe moyo.’ Yohane3:36. Munthu wina aliyense angathe kubwera mukukhala nawo m’dalitso limeneli lopanda mtengo ngati iye angazagwirizane ndi zoyenerenza. ‘Kwa iwo amene afunafuna ulemelerondi ulemu ndi chisaonongeko, mwa kupilira pa ntchito zabwino, azabwezera moyo wosatha.’ Aroma 2:7.” – *The Great Controversy, p. 533.*

“Ubatizo ndi kulengeza kopatulika kwambiri kwa kusiya dziko lapansi. Onse omwe anabatizidwa mmaina atatu a Atate, mwana ndi mzimu woyera, mukulowa kwawo mmoyo wawo wa chikristu amalengeza poyera kuti iwo asiyana nawo utumiki wa Satana ndipo akhala mamembala a banja lachifumu, ana a mfumu ya kumwamba.” – *Testimonies for the Church, Vol. 6, p.91.*

b. Fotokozani mawu ochitisa mantha a Yohane m’batizi omwe akuonetsera kuya kwa kudzipereka kwamoyo kwenikweni komwe kumaonetseredwa kudzera muubatizo? Luka 3:7, 8.

“Yohane anaika mkhwanga ku midzu ya mtengo. Iye amadzudzula tchimo mosaopa zotsatira,ndi kukonzera njira mwana wankhosa wa Mulungu.

“Herodi anakhuzika pamene iye amanvetsera maumboni amphanvu otchulidwa ndi Yohane, ndipo ndichidwi chachikulu iye anafunsa chomwe iye akuyenera kuchita kuti akhale ophunzira wake. Yohane anadziwa nkhani yakuti iye akufuna kukwatira mkazi wa mchimwene wake, pomwe mwamuna wake anali moyo, ndipo mokhulupirika amamuuza Herodi kuti ichi sichinali chololedwa mmalamulo.” – *Early Writings, p. 154.*

“Yohane m’batizi anakumana ndi tchimo ndikudzudzula koonekera mwa anthu antchito zapansi komanso mwa anthu amaudindo apamwamba. Iye analankhula choonadi kwa mafumu ndi anthu olemekezeka, kaya iwo amva kapena achikana icho. Iye amayankhula mwachindunji kwa munthu.” – *Selected Messages, bk. 2, p. 149.*

- a. Pakuzindikira kuti Afarisi anali kuyesesa kubweretsa kulimbana pakati pa yohane ndi iye mwini, kodi Yesu anachita chiyani? Yohane 4:1-3.**

“Yesu anadziwa kuti [Afarisi] anali kuyesesa kukonza zolimbana pakati pa ophunzira ake ndi a Yohane. Iye anadziwa kuti mphepo inali kusunkhana yomwe itha kuchotsa mmodzi wa aneneri aakuru kwambiri omwe sanaperekedwepo kudziko lapansi. Pofuna kupewa zochitika zonse zosamvetsetseka kapena ndewu, iye anasiyiratu ntchito yake, ndikuchoka ku Galireya. Ifenso, pamene tiri ozipereka kuchoonadi tikuyenera kuyesesa kupewa zonse zomwe zingatsogolere kukusagwirizana ndi mkangano. Chifukwa paliponse pamene izi zabuka, zimathera kukutaya miyoyo. Paliponse pamene chochitika chachitika chochititsa mantha kuti chiyambitsa mpatuko, tikuyenera kutsatira chitsanzo cha Yesu ndi cha Yohane m’batizi.” – *The Desire of Ages, p. 181.*

- b. Kodi tikuyenera kuphunzirapo chiyani kuchokera kukhalidwe la Yohane ku kuthetsa vuto? Yohane 3:30.**

“Monga ophunzira a Yohane, ambiri amazimva kuti kupambana kwa ntchito kumadalira pa ogwira ntchito oyambirira. Chidwi chimakhazikidwa pa munthu mmalo mwa kumwamba, nsanje imalowapo, ndipo ntchito ya Mulungu imasiidwa. Munthu yemwe mosasamala walemekezedwa amayesedwa kukukondwerera kuzidalira yekha. Iye samazindikira chidaliro chake pa Mulungu. Anthu amaphuzitsidwa kudalira pa munthu kuti awatsogolere, ndipo pakutero iwo amagwa mukulakwitsa, ndikutsogoleredwa kuchoka kwa Mulungu.

“Ntchito ya Mulungu siikuyenera kukhala ndichithunzi ndi chizindikiro chamunthu. Nthawi ndi nthawi Ambuye adzabweretsa amithenga osiyanasiyana, omwe kuzera mwa iwo cholinga chake chingazakwaniritsidwe mwabwino. Odala ali iwo omwe akufuna kuti undekha uchepetsedwe, kuyankhula pamodzi ndi Yohane m’batidzi, ‘Iye ayenera kukula koma ine ndichepe.’ ” – *Ibid., p. 182.*

1. Kodi ndi chifukwa chiyani ophunzira a Yohane anakhala ansanje ndi ntchito ya Khristu?
2. Kodi Yohane analengeza chiyani kwa ophunzira ake?
3. Ndikucholinga chanji chomwe mphatso ya Mzimu woyera inaperekedwa?
4. Kodi ubatizo umakwaniritsa bwanji cholinga chake chenicheni?
5. Kodi ndichiyani chomwe Yesu ndi Yohane anachita pamene iwo anazindikira choopsa cha kulimbana pakati pa ophunzira awo?

YESU NDI MZIMAYI WAKUSAMARIYA

VESI LOLOWEZA: “Koma iye wakumwa madzi amene ine ndizampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse; koma madzi amene ine ndizampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha” (Yohane 4:14).

Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, Vol. 4, pp. 384-387.

“Iye amene akufuna kuthetsa ludzu lake ku akasupe adziko lino lapansi adzamwa ndikukhalanso ndi ludzu. Kulikonse anthu ali osakhutitsidwa. Iwo akufunitsitsa chinachake kukwanilitsa chosowa cha moyo. Ndimmodzi yekha yemwe angakwaniritse chosowa chimenecho. Chosowa cha dziko lapansi; cha mitundu yonse ndi Khristu.” – *The Desire of Ages*, p. 187.

1. YESU MU SUKARI

Loyamba, Feb 16

a. Paulendo wake wopita ku Galileya, kodi ndi kuti komwe Yesu ndi ophunzira ake anaima? Yohane 4:6.

“Pamene Yesu anakhala pambali pa chitsime, Iye anafooka ndi njala komanso ludzu, ndipo tsopano dzuwa lausana linaombela pa iye. Ludzu lake linakulirakulira poganizira zakudzidzirila, madzi otsitsimutsa omwe anayandikira, komabe osafikilika kwa iye chifukwa iye analibe chingwe ngakhale chitin chotungila, ndipo chitsime chinali chokuya. Gawo la Umunthu linali pa iye, ndipo iye anadikirira kuti wina abwere kudzatunga.” – *The Desire of Ages*, p. 183.

b. Kodi ndindani yemwe anabwera kuchitsime ndipo ndikukoma mtima kwanji komwe Yesu anakupempha kwa iye- ndipo ndi chiyani chimene tikuyenera kuphunzira ku zimenezi? Yohane 4:7.

“Udani pakati pa Ayuda ndi a Samariya unapewetsa Mzimayi kuti apereke chifundo kwa Yesu: Koma mpulumutsi anafunafuna kupeza mfungulo kumtima uwu, Ndipo ndichikondi chobadwa nacho cha umulungu, Iye anapempha kukondera osati kupatsidwa. Kupereka kwa chikondi kukanatha kukanidwa ; koma chidaliro kudzutsa chidaliro.Mfumu yakumwamba inadza ku moyo osowa abwenziwu, kupempha utumiki ku dzanja lake. Iye amene anapanga Nyanja, amene amalamulira madzi ozamitsitsa, amene anatsigula akasupe ndi modutsa mwake adziko lapansi, anapumula kukutopa kwake pachitsime cha Yakobo, ndipo anadalira pa chikondi cha mlendo kumphatso ngakhale ya madzi akumwamba.” – *Ibid.* p.184.

a. Kodi Yesu anaitanitsa bwanji chidwi cha mzimayi kumphatso ya chipulumutso? Yohane 4:10.

“Madzi omwe Khristu amatanthaudza anali bvumbulutso la chisomo chake mmawu ake; mzimu wake, chiphunzitso chake, zili ngati kasupe okwaniritsa kumoyo wina ulionse. Kasupe wina aliyense kumene iwo azapite azatsimikizira kukhala osakhutiritsa. Koma mawu achoonadi ali odzidzilira ngati misinje, anathandauridwa ngati madzi aku lebanu, omwe nthawi zonse amakwaniritsa. Mwa Khristu ndimodzadza ndi chimwemwe kunthawi zanthawi.” – *Testimonies to Ministers*, p. 390.

b. Kodi mzimayi anayankha chiyani ku chopereka cha Khristu? Yohane 4:11, 17.

“Kumvetsetsa kwa mzimayi sanadziwe tanthaudzo la Khristu; Iye amayerekedza kuti iye amanena za chitsime chomwe chinalipo pamaso pawo.” – *The Spirit of Prophecy, Vol. 2, pp. 140, 141.*

c. Kodi Yesu anasiyanitsa bwanji pakati pa mtundu umodzi wa madzi ndi wina ndipo ndimotani, momwe uthengawu ukuyenera kutidalitsira ifenso? Yohane 4:14, 14, Chibvumbulutso 22:17.

“Tikuyenera kukulitsa chikondi ndi chiyamiko, tikuyenera kuyang’ana kwa Yesu ndikukhala otsinthika kufanana ndi iye. Mapeto a izi adzakhala kulimbika koonjezeredwa, chiyembekezo, kupilira ndi kulimba mtima. Tidzamwa madzi amoyo omwe Khristu amanena kwa mzimayi wakusamaria. Iye anati; ‘ukadadziwa mphatso ya Mulungu ndi iye amene alikunena ndi iwe, undipatse ine ndimwe, ukadapempha iye, ndipo akadakupatsa madzi amoyo....Yense wakumwako madzi amene ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse; koma madzi amene ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha.’ Madzi awa akuimirira moyo wa Khristu, ndipo moyo ulionse ukuyenera kukhala nawo awa kudzera mu kubwera kukulumikizana kwa moyo ndi Mulungu. Kenako chidaliro, chodalitsika, chodzichepetsa choyamika zidzakhala mfundo zokhazikika mmoyo. Mantha osakhulupilira adzachotsedwa ndipo padzakhala chikhulupiro cha moyo. Tidzalingalira khalidwe la iye amene anatikonda ife koyambilira.” – *Testimonies to Ministers*, p. 226.

- a. Kodi mzimayi wakusamariya anaonetsa bwanji kuti iye samamvetsetsabe mawu a Khristu? Yohane 4:15.

“Chisomo chakumwamba chomwe ndi iye yekha yemwe angachipereke, chilingati madzi amoyo, kuyereza, kutsitsimutsa ndi kulimbikitsa moyo.

“Yesu sanapereke lingaliro lakuti kumwa kamodzi kokha kwa madzi amoyo ndikokwaniritsa wolandira. Iye amene walawa chikondi cha Khristu adzafunafunabe choonjezera; koma sadzafuna chinthu china. Kulemera, Ulemu, ndizokondweretsa za dziko sizizamukopa iye. Kulira kokhazikika kwa mtima wake ndikokuti, zina za iye. Ndipo iye amene wabvumbulutsa ku moyo kufunikira kwake akudikirira kukhutitsa njala ndi ludzu lake. Katundu ndi zodalira zonse za munthu zidzalephera. Mathamanda onse adzaumitsidwa, dzithapwi zonse zidzauma; koma mpulumutsi wathu ndi kasupe wosaphwa. Tingathekumwa, ndikumwanso, ndipo tidzapeza nthawi zonse madzi atsopano. Iye amene khristu akhala mwa iye ali ndimkati mwake kasupe wamadalitso- chitsime cha ‘madzi a moyo chotumphukira kumoyo wosatha.’ Kuchokera ku kasupe ameneyu iye atha kutunga mphanvu ndi chisomo chokwaniritsa ku zosowa zake zonse.” – *The Desire of Ages*, p. 187.

- b. **Monga mzimayi wakusamariya ndi apaulendo mchipululu mu Exsodo, kodi ndimotani momwe ife kawirikawiri timalephera kuzindikira chisomo chodabwitsa chomwe chimayenda kuchokera mwa Khristu? Masalmo 78:15, 16, 20 (mbali yoyamba); 114:7, 8.**

“Mose anamenya tanthwe, koma anali mwana wa Mulungu yemwe, anaphimbika mumtambo, amene anaima pambali pa Mose, ndikupangitsa madzi opatsa moyo kuti ayende. Osati Mose ndi akuluakulu okha, koma msonkhano wonse womwe unaima patali, unaona ulemelero wa Ambuye; koma zikadakhala kuti mtambo wachotsedwa, iwo akanaphedwa ndi kuwala kowopsa kwa Iye amene anali mkatimo.” – *Patriarchs and prophets*, p. 298.

“Chisomo cha Khristu chopezeka mmawu ake nthawi zonse chimayankhulabe ku moyo. Kumuimilira iye monga chitsime cha madzi amoyo kutsitsimutsa moyo wa ludzu. Ndimwayi wathu kukhala ndi mpulumutsi wamoyo, wopirira. Iye ndi gwero la mphanvu za uzimu zozalidwa mkati mwathu, ndipo chikoka chake chidzasefukira ndi kuyenda kudzera mmawu ndi mmachitachita, kutsitsimutsa onse okhala mumpweya wachikoka chathu, kubereka mwa iwo zikhumbokhumbo ndi kufunitsitsa kwa chilimbikitso komanso ungwiro, kwa chiyero komanso mtendere, komanso kwa chimwemwe chomwe sichimabweretsa chisoni pamodzi ndi icho. Ichi ndichotsatira cha mpulumutsi wokhala mkati.” – *Tetsimonies to Ministers*, p. 390.

- a. **Kodi ndi nkhani yanji yatsopano yomwe Yesu anaibweretsa mukuyankhulana kwake ndi Mzimayi wakusamaliya –ndipo ndimotani momwe iye anayankhira? Yohane 4:16, 17 (Mbali yoyamba).**

“Yesu tsopano mwachangu anatembenuza zokambirana. Moyo uwu usalandire mphatso yomwe iye amafuna kuipereka, iye anayenera kubweretsedwa kukuzindikira tchimo lake ndi mpulumutsi wake. Iye anati kwa iye, ‘pita kamuitane mwamuna wako, nudze kuno.’ Iye anayankha, ndiliba mwamuna’; Chotero iye anayembekezera kupewa mafunso onse olozera mu chimenecho.” – *The Desire of Ages*, p. 187.

- b. **Kodi Yesu anayamikira motani yankho lake- ndipo ichi chikutikumbutsa ife chiyani zokhuza zonse zomwe iye akudziwa zokhuza wina aliyense wa ife? Yohane 4:17 (mbali yotsiliza) 18; Masalimo 139:7, 8, 11, 12.**

“Ukulu wa Mulungu uli kwa ife wovuta kuumvetseta. ‘Mpando wa chifumu wa Ambuye uli m’mwamba(masalmo 11:4); Komabe kuzera mwa Mzimu wake iye amapezeka paliponse. Iye ali ndichiziwitso chosabisika cha, ndi chidwi chachikulu, cha ntchito zonse za dzanja lake.”- *Education*, p. 132.

“Angelo akumwamba amafufuza ntchito yomwe yaikidwa mmanja aanthu, ndipo pamene pali kuchoka kumfundo zachoonadi, ‘kuperewera’ kumalembedwa mu mbiri.” – *Child Guidance*, p. 155.

“Lamulo la Mulungu limafikira zokumva muntima ndi zolingalira, komanso mmachitachita akunja limabvumbulutsa zinsinsi za muntima, kuonetsera kuwala pazinthu zisanakwaniridwe mumtima. Mulungu amadziwa lingaliro lililonse cholinga chilichonse, dongosolo lililonse, ndi ganizo lililonse. Mabuku a kumwamba amasunga machimo omwe akanachitidwa pakanakhala kuti pali mwayi. Mulungu adzabweretsa ntchito iliyonse muchiweruzo, ndi zinthu zonse zachinsinsi. Mwalamulo lake iye amayeza khalidwe la munthu aliyense. Monga wojambula waluso amasamutsa kuika pa nsalu yokhutala maonekedwe ankhope chotero maonekedwe a khalidwe la munthu wina aliyense amasamusilidwa kumabuku akumwamba. Mulungu ali ndi chithunzi changwiwo cha khalidwe la munthu wina aliyense ndipo chithunzi chimenechi iye amachifanizira ndi malamulo ake. Iye amabvumbulutsa kwa munthu zolakwitsa zomwe zadetsa moyo, ndikuitatsa pa iye kulapa ndi kubwerera kuchoka kuuchimo.” – *The SDA Bible Commentary [E.G White Comments]*, Vol. 5, p. 1085.

a. Kodi ndi chiyani chimene mzimayi wa pachitsime uja mapeto ake anachizindikira zokhuza Yesu? Yohane 4:19. Kodi kuzindikiraku kunali kokwanira?

“Omvetsera ananjenjemera. Zanja lodabwitsa linabvundukula masamba a mbiri ya moyo wake, kubweretsa poonekera icho chimene iye anayembekezera kuchisunga mobisa mpaka kalekale. Kodi Iye anali ndani kuti angathe kuwerenga zinsinsi za moyo wake? Tsopano munabwera mmalingaliro ake malingaliro a umuyaya, a chiweruzo cha mtsogolo, pamene zonse zomwe zikubisidwa tsopano zidzabvumbulutsidwa mukuunika kwake. Mukuwala kwake, chikumbumtima chinazutsidwa.

“Iye sanakane kanthu; koma iye anayesesa kupewa zonenapo kanthu za nkhaniyi yosalandiridwa. Ndikulemekeza kwakukulu iye anati, ‘Abuye ndizindikira kuti muli mneneri.’ Tsopano, kuyembekezera kukhazikitsa chete kususika, iye anatembenukira kumfundo ya mkangano wachipembezo. Ngati uyu anali mneneri motsimikidzika iye akanapereka kwa iye malangizo okhuza nkhani zimenezi zomwe zinali mkangano wa nthawi yaitali.” – *The Desire of Ages*, pp. 187,188.

b. Pamene mzimayi anaonetsa chikhulupiriro mukubwera kwa Mesiya, kodi Yesu anayankhula chiyani kwa iye? Yohane 4:25, 26.

“Kuitanira kwa uthenga wabwino sikukuyenera kuchepetsedwa pansu, ndikuperekedwa kwa osankhika ochepa okha, omwe ife tikuganiza kuti zizatipatsa ife ulemu ngati iwo ataulandira iwo. Uthenga ukuyenera kuperekedwa kwa onse. Kulikonse komwe mitima yatseguka kulandira choonadi, Khristu ali wokonzeka kuulangiza iwo. Iye amabvumbulutsa kwa iwo Atate, ndi kupembedza kolandilika kwa iye amene amawerenga mtima. Chifukwa cha izi iye amagwiritsa ntchito mafanizo kwa iwo, monga kwa mzimayi wa kuchitsime, Iye akuti, ‘Ine wakulankhula nawe ndine amene.’” – *The Desire of Ages*, pp. 194.

6. MAFUNSO WOBWEREZA PAWEKHA

Lachisanu ndi chimodzi, Feb 21

1. Kodi ndichifwa chiyani Yesu sanachite konse chozwizwa kudzichitira iye mwini?
2. Kodi Yesu anagwiritsa ntchito thandizo lanji kumtsogolera mzimayi wakuSamariya ku uthenga wabwino?
3. Kodi Ambuye akulankhula chiyani zokhuza madzi amoyo?
4. Ndichifukwa chiyani Khristu anatchula moyo weniweni wa Mzimayi wa ku Samariya?
5. Tchulani lonjezo lophatikizana ndi kubwera kwa Mesiya.

Zopereka Za Sabata Loyamba SABATA,

Marichi 1, 2025



“Ana a khalidwe”

Malo ophunzirako a ku Romania

“Maphunziro oyambirira achinyamata kwambiri amaumba makhalidwe awo ku moyo.” – *Testimonies for the Church, Vol. 3, 135.*

Mawu ouzilidwa amafotokoza za machitachita achilimbikitso amene ‘misonkhano ya ana, kapena sukulu za ana aang’ono ophunzira Baibulo, zachitira ntchito yabwino. Maphunziro operekedwa amabwerezedwa ndi ana manyumba awo, ndipo amayi amaonesa chidwi chawo pomukonzekeretsa mwana mwaukhondo ku Sukulu. Ena ndi ana amakolo osakhala achikhulupiliro chatu.”-
- *Evangelism, p. 583.*

Malo ophunzirira a “Ana a Khalidwe” anakhazikitsidwa mu 2019 mu fagaras, mzinda wamphiri mu Romania. Ana apakati pa zaka ziwiri ndi zisanu akukulira mokongora pamenepa. Mophatikizirapo kuntchito zapadera zolingana ndi zaka, iwo amaphunzira nthano za m’baibulo, kupemphera, kuimba ndi kumupanga Mulungu kukhala bwenzi lawo. Mwauchichepere momwe iwo ali, iwo amamvetsetsa kuti Mulungu akutetezera ndipo iwo amaphunzira kumupempha iye thandizo kumavuto awo. Khalidwe lawo likumangika tsiku ndi tsiku. Mwachisomo cha Mulungu tingathe kuona kusinthika kowonekera mmiyoyo ya ana achichepere chifukwa cha tsogolo, ife tikufuna kuphunzitsa onse omwe zodutsamo za zinthu zawo sizikulolera ichi. Muchaka choyamba tinayamba ndi ana khumi ndi awiri 12; muchaka cha chinayi tinali ndi ana 32,31 a iwo ochokera kunja kwa mpingo. Panopa zochitika zikuchitiridwa mu zipinda 4 zomangidwa ndi likuru la union ya Romania, koma awa akuonetsera kukhala opanikizika pamene mapemphero ofuna kudzayamba ali opitilira malo athu. Mwa ichi, tikumvetsetsa kuti Mulungu akufuna ife kupitiliza komanso kukudza ntchito yodabwitsayi ndipo chotero ana ambiri abwere mukulumikizana nafe ndi mabanja awo ngati mkotheke. Chotero, mu 2021, gawo la malo linagulidwa kunja kwa mzinda ndipo tinapedza zilolezo zofunikira kuti tiyambe ntchito yakumanga. Tsopano madziko aikidwa kale. Tikuthokoza kwambiri kwa Mulungu pokhuza, mitima yaanthu ambiri mwa inu omwe akuthandiza ntchitoyi kufikira mulingo umenewo ndi inu nonse omwe mudzachite chomwechi mwaufulu moolowa manja tsopano. Ndimphanso zanu, mudzawapatsa ana omwe sakumziwa Mulungu mwayi obwera chifupi kwa iye ndikulandira maphunziro a chikristu. Tikupempha kufuna kwabwino kwanu ndipo tasimikizika kuti inu simudzakhala chimodzimidzi, koma mudzatithandiza ife kubweretsa ntchito imeneyi ku chipambano chomalizitsa ndikutiikiza ife mmapempheronso.

Abale ndi Alongo anu kuchokera ku Union ya Romania

KUBADWA KWA MTUMIKI

VESI LOLOWEZA: “Kodi simunena inu, kuti yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, kwezani maso anu, nimuyang’ane m’mindanda, kuti mwayera kale kufikira kumweta” (Yohane 4:35).

Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, Vol. 5, pp. 182-187

“Yesu anayamba kugumula khoma lolekanitsa pakati pa ayuda ndi Amitundu, ndikulalikira chipulumutso kudziko lapansi. Ngakhale anali muyuda, Iye amasakanikirana mwaufulu ndia Samaliya, kuthetsa myambo ya chifarisi ya mtundu wake.” – *The Desire of Ages*, p. 193.

1. MOYO WATSOPANO, ZOKHUMBA ZATSOPANO

Loyamba, Feb 23

a. Atamuzindikira Yesu ngati Mesiya, kodi mzimayi waku samariya anachita chiyani mwachangu? Yohane 4:28, 29.

“Mzimayi anazazidwa ndi chimwemwe pamene iye amanvetsera ku mawu a khristu. Bvumbulutso lodabwitsa linali pafupifupi likulamulira. Posiya msuko wake wamadzi, iye anabwerera ku mzinda, kupitisa uthenga kwa ena. Yesu anadziwa chifukwa chomwe iye anapitira. Kusiya msuko wake wamadzi kunayankhula mosalakwa munga kuchotsatira cha mawu ake, linali khumbo losasewera la moyo wake kutenga madzi amoyo; ndipo anaiwala chiwiya chake kumadzi, iye anaiwala ludzu lampulumutsi, lomwe iye amafunika kulisamalira. Ndipo mtima wosefukira ndi chimwemwe, iye anafulumizitsidwa pa njira yake, kukapereka kwa ena kuunika kwamtengo wapatali komwe iye anakulandila.” – *The Desire of Ages*, p. 191.

b. Kodi ndichiyani chomwe anthu okhala mu Sukali anachita pamene iwo anamva umboni wa mzika mzawo? Yohane 4:30.

“Mawu amzimayi anakhuza mitima yao. Panali mafotokozedwe atsopano pa nkhope pake, kusinthika mmaonekedwe ake onse. Iwo anali ofunitsisa kukaona Yesu.” – *Ibid.*

a. Pamene Yesu anaona anthu okhala ku Sukali akubwera, kodi iye analankhula chiyani kwa ophunzira ake? Yohane 4:37-38.

“Iye wakumweta alandira kulipira,’ Iye anatero, ‘ndipo asonkhanitsira zobala ku moyo wosatha; kuti wofesayo akakondwere pamodzi ndi womwetayo pakuti momwemo chonenacho chiri choona, wofesa ndi wina, womweta ndi winanso.’ Apa khristu anatchula utumiki wopatulika operekedwa ndi Mulungu kwa onse omwe alandira uthenga wabwino. Iwo akuyenera kukhala amithenga ake amoyo. Iye akufuna utumiki wawo wapayekhapayekha. Ndipo kaya tadzala kapena tamweta, tikugwirira ntchito Mulungu. Wina afesa mbewu; wina asonkhanitsa zokolola; ndipo onse ofesa ndi omweta alandira kulipira. Onse akondwera pamodzi muchobwezera cha ntchito yawo.” – *The Desire of Ages*, pp. 141, 192

b. Kodi chotsatira cha umboni wa mzimayi wokhuza Khristu chinali chiyani- ndipo tingaphunzirepo chiyani kuchokera ku zotsatira zamphanvu zomwe unali nawo? Yohane 4:39.

“Pamene talumikizidwa kwa Khristu, timakhala ndi malingaliro a khristu. Chiyero ndi chikondi chimawalira mu khalidwe, chifatsondi choonadi zimalamulira moyo. Zofotokoza zonse za maonekedwe a nkhope zimasintha. Khristu kukhazikika mmoyo amaikamo mphanvu zosinthira, ndipo machitidwe akunja amachitira umboni ku mtendere ndi chimwemwe zomwe zikulamulira mkati. Timamwa muchikondi cha Khristu, monga nthambi zimatenga zakudya ku mpesa. Ngati talumikizidwa mwa Khristu, ngati nyewa ndi mnyewa talumikizana ndi mpesa wamoyo, tidzapereka umboni wa chenicheni pobereka zolemera zofanana za chipatso cha moyo. Ngati talumikizana ndi kuunika, tidzakhala njira za kuunika, ndipo mmau ndi ntchito zathu tidzaonetsera kuunika kudziko lapansi....

“Pakuyang’anitsitsa timakhala osinthika; ndipo pamene tikulingalira pa ungwiro wa khalidwe lakumwamba, tidzakhumba kukhala osinthika apumphu, ndiokonzedwanso muchifaniziro cha ungwiro wake. Ndikuzera mwachikhulupiriro mwa mwana wa Mulungu momwe kusinthika kumachitika mukhalidwe, ndipo mwana wa mkwiyo amakhala mwana wa Mulungu. Iye amadutsa kuchoka ku imfa kupita kumoyo iye amakhala mu uzimu ndipo amadzindikira zinthu za uzimu. Mzeru za Mulungu zimawalira malingaliro ake, ndipo iye amaona zinthu zodabwitsa kuchokera mmalamulo ake. Pamene munthu wasinthika ndi choonadi, ntchito ya kusinthika kwa khalidwe imapitilira.” – *Selected Messages*, bk. 1, pp. 337,338.

a. Kodi ndipempho lanji lomwe anthu aku Samariya analipereka kwa Yesu- ndipo chifukwa chiyani? Yohane 4:40.

b. Fotokozani chotsatira cha nthawi yakukhala kwa Khristu mu Samariya. Yohane 4:41.

“Mmawu oyankhulidwa kwa mzimayi pachitsime, mbewu yabwino, inadzalidwa, ndipo ndimofulumira motani momwe zokolola zinalandiridwa. Anthu aku Samariya anabwera ndikuzamunva Yesu, ndikukhulupilira mwa iye. Pozinga mozungulira iye pachitsime, iwo anamudzadza iye ndi mafunso, ndipo mokondwera analandira kufotokozera kwake kwa zinthu zambiri zomwe zinakhala zophimbika kwa iwo. Pamene iwo amamvetsera, nkhawa zao zinayamba kuchoka. Iwo anali ngati anthu amundima waukulu kusatira mlezo wodabwitsa wakuunika kufikira iwo atapeza usana.. Koma iwo sanakhutitsidwe ndi mkumano waufipiwu. Iwo anali chidwi choti amve zambiri, ndikukhalanso ndi abwenzi awo kudzamvetsera kwa mphunzitsi wodabwitsayu. Iwo anamuitanira iye ku mzinda wawo; kwa matsiku awiri iye anakhala mu Samariya, ndipo ambiri ena anakhulupirira pa iye.”--*The Desire of Ages*, p. 192.

“Khristu anabvumbulutsa Mulungu kwa ophunzira ake munjira yakuti anachita mmitima yawo ntchito yapadera, yotere yonga yomwe iye wakhala akudandaulira ife kuti timlolle kuichita mmitima yathu. Pali ambiri omwe, akukhalanso kwambiri pa zolembedwa, ataya chiyang’aniro cha mphanvu zamoyo za chitsanzo cha Mpulumutsi. Iwo ataya chiyang’aniro cha iye monga, wantchito wozikaniza yekha, wozichepesa. Chomwe iwo akusowa ndikuyang’ana kwa Yesu. Tsiku lililonse tikusoweka kubvumbulutsidwa kwatsopano kwa kupedzeka kwake.” -*Reflecting Christ*, p. 302.

c. Kodi a Samariya ambiri anayankhula chiyani atatha kumlandira Yesu monga Mesiya? Yohane 4:42.

“Afalisi ananyoza kuzichepetsa kwa Yesu. Iwo ananyozera zozizwa zake, ndikupempha chizindikiro kuti iye anali mwana wa Mulungu. Koma a Samariya sanafunse chizindikiro, ndipo Yesu sanachite zozizwa pakati pawo, kupatula mukubvumbulutsa zinsinsi za moyo wake kwa mzimayi pachitsime. komabe anthu ambiri anamlandira iye. Muchimwemwe chatsopano iwo anati kwa Mzimayi, ‘Tsopano takhulupirira, Osati chifukwa cha kulankhula kwako; pakuti tanva tokha ndipo tidziwa kuti uyudi ndithu ndi Khristu, Mpulumutsi wa dziko lapansi.’” – *The Desire of Ages*, pp. 192,193.

a. Kodi ndi pauneneri wanji pomwe a Samariya anakhazikitsa chikhulupiriro chawo mwa Mesiya olonjzedwa? Genesis 49:10.

“A Samariya anakhulupilira kuti Mesiya anayenera kubwera monga mpulumutsi, osati kwa Ayuda okha, koma kudziko lapansi. Mzimu woyera kuzera mwa Mose analosera iye ngati mneneri wotumizidwa kuchokera kwa Mulungu. Kuzera mwa Yakobo chinakhala chikulankhulidwa kuti kwa iye anthu akuyenera kusonkhanira; ndipo kudzera mwa Abraham kuti mwa iye mitundu yonse yadziko lapansi ikuyenera kudzadalitsidwa. Pa malemba amenewa, anthu aku Samariya anakhazikitsa chikhulupiriro chawo mwa Mesiya. Mfundo yakuti Ayuda amatanthauzira molakwika aneneri obwera pambuyo, kumakhulupirira za ulemerero wakubwera kwa Khristu kwachiwiri kumakusokoneza ndi koyamba, zitsogolera a Samariya kusiya zolembedwa zopatulika zonse kupatula zomwe zinaperekedwa kudzera mwa Mose. Koma pamene Mpulumutsi amachotsa zothandauzira zabodzazi, ambiri analandira mauneneri osatira komanso mawu a Khristu mwiniwake okhuza ufumu wa Mulungu.” – *The Desire of Ages*, p. 193.

b. Kodi tingaphunzire chiyani lero kuchokera kuchoona chakuti Asamariya anali otsegukira modabwitsa ku choonadi? Mlaliki 11:4, 5.

“Kudziko lonse lapansi Abambo ndi Amayi akuyang’ana mwachidwi kumwamba. Mapemphero ndi misodzi ndi mafunso zokwera kuchokera mmiyoyo yofunafuna kuunika, chisomo, mzimu woyera. Ambiri ali pa gombe la ufumu, kudikirira chabe kusonkhanisidwira mkati.” – *The Acts of the Apostle*, p.109

c. Kodi ndichiyani chomwe anthu amakhala pamene iwo moonadi alandira Khristu? Perekani chitsanzo. Marko 5:18-20; 7:31-37.

“Mzimu wa Khristu udzayambisa mwa munthu zonse zomwe zidzakometse khalidwe ndikulemekedza umunthu. Udzammanga munthu, ku ulemerero wa Mulungu muthupi, mmoyo ndi mzimu. Ndipomiyoyo yomwe yakhala inachepetsedwa ndi kupitidwa pansu kukhala zida za Satana kudzera mumphanvu ya Khristu akusinthikabe kukhala amithenga a chilungamo, ndikutumizidwa chitsogolo ndi mwana wa Mulungu kuyankhula za zinthu zazikulu zomwe Ambuye wachita kwa iwo ndi chifundo choonetsedwa pa iwo.” – *The Desire of Ages*, p. 341.

a. Kodi ndimaphunziro anji amene Ife tikuphunzira kuchokera kwa mzimayi waku Samariya? 1 Yohane 1:1-3, 2 Akolinto 5:14 (mbali yoyamba).

“Nthawi yomweyo pamene iye anapeza mpulumutsi Mzimayi wa ku Samariya anabweretsa ena kwa iye. Iye anazionesa yekha mtumiki wamphanvu kwambiri kuposa ophunzira a iye mwini. Ophunzira sanaone kanthu mu Samariya chosonyeza kuti unali munda wolimbikitsa. Malingaliro awo anakhazikika pantchito yaikulu yoyenera kuchitidwa mtsogolo. Iwo sanaone kuti ufulu owazungulira iwo zinali zokolora zoyenera kusonkhanitsidwa. Koma kudzera mwa mzimayi yemwe iwo amamunyoza, mzinda wonse unabweretsedwa kumunva mpulumutsi. Iye ananyamulira kuunika kwa anthu amziko nthawi yomweyo.

“Mzimayi uyu akuimilira kugwira ntchito kwa chikhulupiriro chochitachita mwa khristu. Ophunzira aliyense oona amabadwa mu ufumu wa Mulungu monga mtumiki. Iye amene wamwa madzi amoyo amakhala kasupe wa moyo. Wolandira amakhala opereka. Chisomo cha Khristu mmoyo chili ngati kasupe wamadzi muchipululu, otungidwa mpaka kutsitsimutsa onse, ndikuwapangitsa onse omwe ali okonzeka kuonongeka kufuna kukumwa madzi amoyo.”

– *The Desire of Ages, p. 195.*

b. Kodi chochitika chimenechi chingatilimbikitse ife bwanji lero? Mlaliki 11:6

“Sitikusoweka kupita kumalo achilendo kukakhala atumiki a Mulungu. Onse otizungulira ife ali minda. ‘Yoyera yokonzeka kukumweta,’ ndipo aliyense amene angafune angathe kusonkhanitsira ‘zobala ku moyo wosatha.’ Mulungu akuitanira ambiri mu Battle creek omwe akufa kuuzimu waulesi kuti apite komwe ntchito yawo ikusowekela muntchito yake. Tulukani mu Buttle Creek, ngakhale ichi chitafunikira msembe yapadera. Pitani kwinakwake kuti mukakhale mdalitso kwa ena. Pitani komwe mungakalimbikitse mpingo wina wofooka. Gwiritsani ntchito mphanvu zomwe Mulungu wakupatsani inu.” – *Testimonies for the Church, Vol. 5, p. 187.*

1. Kodi mzimayi anachita chiyani pamene iye anaona Yesu monga mpulumutsi yekhayo?
2. Fotokozani chomwe chikutanthauza kuti minda yayera yokonzeka kukholola.
3. Kodi ndimatsiku angati omwe Yesu anakhala ndi a Samariya?
4. Kodi ndiumboni wanji omwe a Samariya anapereka okhuza Yesu?
5. Chimachitika ndichiyani kwa anthu nthawi yomweyo pamene iwo amlandira Yesu ku miyoyo yawo?

YESU NDI MWANA WA MKURU WA AYUDA

VESI LOLOWEZA: “Ndipo kwa Iye amene angathe kuchita koposa-posatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganiza, monga mphamvu yakuchita mwa ife, kwa Iye ukhale ulemerero mu mpingo ndi mwa Yesu Khristu, kufikira mibado yonse ya nthawi za nthawi. Amen” (Aefeso 3: 20, 21).

Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, Vol.9, pp. 107,108,164-166.

“Osati tizikhulupirira chifukwa choti tikuona ndi kuchimva mumtima kuti Mulungu akutimva ife. Tikuyenera kumadalira mu malonjezo ake. Pamene ife tibwerra kwa iye mwachikhulupiriro pempho lililonse limalowa mumtima mwa Mulungu. Pamene tapempha dalitso lake tikuyenera kukhulupirira kuti talirandira ilo, ndipo timuthokoze kuti ife talirandira ilo kenako tipitilize kugwira ntchito zathu, motsimikizika kuti dalitso lizakwanilidwa pamene talifunitsitsa ilo kwambiri.” – *The Desire of Ages*, p. 200.

1. KUDZUTSA CHIDWI

Loyamba, Marichi 2

a. Atatha kukhala masiku awiri ndi a Samaliya, kodi ndi kuti kumene Yesu anapitanga ndi ndani amene anakopeka ndi mbiri imeneyi? Yohane 4:43-46.

“Mbiri ya kubwereranso kwa Khristu ku Kana mwamsanga inafalikira mu Galireya monse ndipo inabweretsa chiyembekezo kwa odwala ndi osausika. Ku kapernamu mbiri imeneyi inakopa chidwi cha mkuru wa aYuda amene anali mdindo otumikira mfumu.” – *The Desire of Ages*, p. 196.

b. Kodi ndi chifukwa chiyani mdindo wa mkuruyi anapita kuti akakumane ndi Yesu? Yohane 4:47.

“Mwana wamwamuna wa mdindoyu amadwala nthenda yooneka yosachilitsika. Madotolo anamulephera ndi ndikumadikira basi kuti afe. Koma pamene bamboo ake anamva za Yesu, iye anatsimikizika zokapempha thanzizo kuchokera kwa iye.” – *Ibid.*, p 197.

a. Fotokozani mmene Khristu anabvumbulutsira kusautsika kwa mkati mwa mtima wa mdindo wa mkulu amene anamupempha iye kuti amuchiritse mwana wake ku kaperenamu. Yohane 4:48.

“Mwanayo anali atadwalika zedi, ndipo panali mantha akulu, oti mwina sakhala moyo mpaka kufikira iye abwerenso, komabe mdindoyo anachimva kuti ndibwino akamufotokozere Khristu nkhanayi maso ndi maso. Iye anayembekezera kuti mapemphero a tate akhoza kudzutsa chifundo cha Dokotala wamkulu.

“Atafika ku kana iye anapedza khamu lalikulu litamuzungulira Yesu. Ndi Mtima wankhawa iye anazipanikiza kufikira anafika pamaso pa mombolo. Chikhulupiriro chake chinazirara pamene iye anaona munthu chabe obvala zobvala za wamba wotuwa ndi wotopa ndi kuyendayenda. Iye anakaika ngati munthu ameneyu angathe kuchita chimene iye anabwera kudzamupempha iye; komabe iye anapedza mwayi woyankhulana ndi Yesu, namuza iye chomwe anabwerera ndikumupempha mpulumutsi kuti atsagane naye kupita kunyumba kwake. komabe Yesu anaziwiratu nkhwawa ya mdindoyo asananyamuke kunyumba kwake, Mombolo anaona kutsautsika kwake.

“Koma iye anadziwa kutinso tateyu, anali ndi zinthu zimene anazikhazikitsa mumtima mwake, zokhuzana ndi zoyenereza za kukhulupirira kwake mwa Yesu. Pokhapokha pempho lake ngati lingabvomeredwe iye sangamulandire iye ngati Mesiya...

“Posatengela umboni wonse woti Yesu ndi khristu, wopemphathandizo anatsimikiza mtima kuti apange chikhulupiriro chake mwa khristu kukhala ndi choyenereza ngati iye angabvomeredwe pempho lake basi.” – *The Desire of Ages*, pp. 199,198.

b. Tikayesedwa kuti tifune zizindikiro, kodi ife tikuyenera kumakumbukira chiyani? Mateyu 12:38, 39.

“Khristu anapwetekedwa mumtima kuti anthu ake enieni, amene kwa iwo kunaperekedwa malembo opatulika, akulephera kumva mawu a Mulungu kuyankhulidwa kwa iwo mwa mwana wake.” – *Ibid.*, p. 198.

“Anthu amafuna chizindikiro monganso mmasiku a Khristu. Koma Ambuye anawauza iwo kuti palibe chizindikiro chimene chikuyenera kuperekedwa kwa iwo. Chizindikiro chimene chikuyenera kuonekera tsopano komanso nthawi zonse ndiko kugwira ntchito kwa mzimu woyera mu mtima wa mphunzitsi kuti apange mawu kukhala okhuza monga momwe angathere. Mawu a Mulungu sinthano yokufa, youma koma mzimu ndi moyo. Satana sangakondenso chinthu china kwambiri kuposa kuchosa malingaliro aanthu kuchoka ku malembo kuti azifunafuna ndi kuyembekezera zinthu zina za kunja kwa Malemba kuti ziziwakomera iwo.” – *Selected Messages*, bk. 2, p. 95.

a. Fotokozani kusiyana pakati pa Ayuda ndi Asamaliya mokhuzana ndi chikhulupiliro chawo mwa Yesu. Marko6:2-6; Yohane 4:40-42.

“Kodi ndi mwakhama motani mmene Afalisi amafunitsitsa kuonetsa umboni moonekera woonetsa khristu kuti ndiwachinyengo! Ndi motani mmene amayang’anitsitsa liwu lake lililonse, kufunafuna kuti apotoze ndi kutanthauza molakwika zoyankhula zake zonse, kunyada ndi kuweruziratu ndi zikhumbitso zinatseka njira iliyonse ya moyo kuumboni wa mwana wa Mulungu. Pamene iye poyera anazuzula zochimwa zawo ndi kumafotokoza kuti ntchito zawo zimachitira umboni woonetsera iwo kuti ndi ana a Satana, iwo mokwiya anamubwezera kuneneza uku ponena kuti, “kodi sitinanene choona kuti inu ndi msamaliya, ndi kuti muli ndi chiwanda.” – *Selected Messages, bk.1,p. 70.*

“Mpulumutsi anasiyanitsa kusakhulupilira kwamafunso koteleku ndi chikhulupiliro chophweka cha a Samariya, amene samafunsa chozizwa ndi chizindikiro. Mawu ake, umboni wosasusika wanthawi zonse wa umulungu wake, anali ndi mphanvu zokhuza zimene zimakafikira mmitima yawo. “ – *The Desire of Ages, p. 198.*

“Ngakhale [Yesu] anali muyuda, iye amalumikizana momasuka ndi Asamaliya, osasamala konse miyambo yachifalisi ya Ayuda yokhuzana ndi anthu onyozeka amenewa. Iye amagona mu nyumba zawo, nadya pa magome awo, ndipo anaphunzitsa mu misewu yawo. – *The Acts of the Apostles, p. 19.*

b. Fotokozani zomwe amadusamo ambiri mwa anthu amene amalankhula choonadi chalero kwa anthu ozinena a Mulungu mu mibado yonse. Yereimiya 20:8-11.

“Milandu yonse yomwe amaimbidwa khristu inapangidwa kuchokera muchinyengo. Chimodzimidzinsu mu mlandu wa Stefano, ndi wa Paulo. Koma kufotokoza kosadalilika konse kumene kumapangidwa ku mbali yolakwa kuli ndi chikoka chifukwa pali anthu ambiri amene mitima yawo ndi yosayeretsedwa, amene amafunitsitsa kuti mawu amenewo akhale oona, oterewa nthawi zonse amakhala ndi chidwi choti alimbikitse bodza, cholakwa ndi chophophonya cha iwo amene amayankhula kwa iwo choonadi chosakondedwa.

“Sizikuyenera kudabwitsika ife konse pamene malingaliro oipa alandilidwa mwachangu monga ngati choonadi chosakaikitsa ndi iwo amene ali ndi khumbo la bodza. Wosusa khristu kawiri ndi kawiri amasokonezedwa ndi kukhazikitsidwa chete kudzera mu mzeru za mawu ake; komabe iwo anali ofunitsitsa kumvetsera mpheketsera iliyonse, ndi kumapedza mawu ena kuti amukore iye kawiri ndi mafunso osusa.” – *Selected Messages, bk. 1, pp. 70, 71.*

a. Pamene chikhulupiriro cha mdindo wolemekezeka chinagwira zolimba pa Khristu kodi ndi motani mmene iye anabwerezera pempho lake? Yohane 4:49.

“Monga kuthwanima kwa kuwala, mawu a Mpulumutsi kwa mdindo olemkezeka anaika poyera za mumtima mwake. Iye anaona kuti zolinga zake mukufuna yesu zinali zaundekha. Chikhulupiriro chake choipa chinaonekera kwa iye mukhalidwe lake lenileni. Mwa nkhwawa yaikulu iye anazindikira kuti kukaika kwake kukhoza kutaikisa moyo wa mwana wake. Iye anazindikira kuti anali pamaso pa yekhayo amene amatha kuwerenga malingaliro, kwa iye amene zinthu zonse ndi zotheka ... Chikhulupiriro chake chinagwira zolimba pa Khristu monga anachitira Yakobo, pamene amalimbana ndi ngelo, iye analira, ‘Sindizakuleka iwe kuti umuke, ukapanda kundidalitsa ine.’ Geneses 32:26.” – *The Desire of Ages, p. 198,*

b. Kodi ife tikuyenera kuphunzira chiyani kuchokera ku zomwe Yesu anachita mmalo mopita kunyumba ya mdindo olemkezeka? Yohane 4:50.

“Yesu anali ndi mphatso yaikulu kuti aipereke. Iye amafuna, osati kungomuchilitsa mwanayo chabe koma kuti ampange mdindo ameneyu ndi apanyumba ake onse kukhala ogawana nawo madalitso a chipulumutso, ndi kuyatsa nyali mu kaperenamu, amene posachedwa akhale munda womwe iye azigwiramo ntchito zake. Koma mdindo wolemekezekayu akuyenera kuzindikira chosowa chake kaya iye asanayambe kufuna chisomo cha khristu. Mdindo ameneyu amaimirira anthu ambiri a mudziko lake. Iwo anali ndi chidwi mwa Yesu koma ndi zolinga za undekha. Iwo amayembekezera kulandira phindu lapadera kuchokera ku mphanvu zake, ndipo iwo anakhazikitsa chikhulupiriro chawo mu kupatsidwa kukondeledwa kumeneku kwa zinthu zakanthawi. Koma iwo samazindikira konse za nthenda yawo ya uzimu ndipo samaona konse chosowa chawo cha chisomo cha Umulungu...

“Mpulumutsi sangazichotse konse kuchoka kumoyo umene ukukangamira kwa iye, kuchonderera chosowa chake chachikulu. Mdindo wolemekezekayu anachoka pamaso pa mpulumutsi ndi mtendere ndi chimwemwe zimene iye sanayambe wakhala nazo mbuyo monsemu. Sanangokhulupilira kokha kuti mwana wake achilitsidwa, koma ndi chidaliro champhanvu iye anakhulupirira mwa khristu monga mombolo.” – *Ibid., pp. 198,199.*

“Ife tonse timafunitsitsa mayankho achangu ndi achindunji amapemphero athu, ndipo timayesedwa kuti tigwetsedwe mphwayi pamene mayankho achedwa kapena abwera munjira imene sitimayiyembekeza. Koma Mulungu ndi wamzeru zonse ndi wabwino kwambiri kuti amayankha mapemphero athu nthawi zonse munthawi yomweyo ndi munjira yomweyo mmene tikufunira. Iye azachita zambiri ndi zabwino kwa ife kuposa kungokwaniritsa zofuna zathu zonse... Zochititika izi zimene zimayesa chikhulupiriro ndi zakuubwino wathu.” – *The Ministry of Healing, pp. 230,231.*

a. Kodi ndi munjira yanji mmene Yesu anachilitsira mwana wa mdindo wolemekezeka? Yohane4:51-53. Kodi choona ichi chikutikumbutsa ife chiyani? Aefeso3:20-21.

“Pa mphindi yomweyo imene chikhulupiliro cha Atate chinagwira chitsimikizo choti, mwana wako ali ndi moyo, chikondi cha Umulungu chinakhuza mwana amene amafayo.” – *The Desire of Ages*, p. 199.

“Pa Mphindi yomweyo anthu amene amayang’anira amene anali pa mbali pa mwana amene anali pafupi kufayu kunyumba ku kapenamu anaona kusintha kodabwitsa ndi kwachangu. Mthunzi wa imfa unachotsedwa kuchoka pankhope pa wodwalayo kuocha kwa thupi kunachoka ndipo mmalo mwake kubwereranso kwa nthanzi kwa pumphu. Maso ofooka anawalitsidwa ndi chiziwitso cha mzeru, ndipo mphanvu zinabwerera ku thupi lofooka ndi lodwalika. Palibe chizindikilo china chilichonse cha nthenda yake chomwe chinasalira pa mwanayu. Thupi lake lotentha linasandulika lofewa ndi lanthete, ndipo mwakachetechete anagona tulo labata. Nthenda inamuleka iye pakatikati pa usana. Banja lonse linadabwitsika, ndipo chimwemwe chawo chinali chachikulu.” – *Ibid.*

b. Kodi ndi motani mmene Yesu amayankhulira kwa aliyense amene akuchonderera thandizo? Mateyu11:28-30.

“Mpulumutsi sangachoke kuchoka kumoyo umene ukukangamira kwa iye kuchonderera chosowa chake chachikulu.” – *Ibid.*, p. 198.

“Kodi inu mukuzinva mumtima kuti chifukwa choti ndi inu ochimwa simungayembekezere kulandira mdalitso kuchoka kwa Mulungu? Kumbukirani kuti Khristu anabwera kudziko lapansi kudzapulumutsa ochimwa. Tilibe kenakalikonse kotiyamikira ife kwa Mulungu; pempho limene ife tingathe kulipereka tsopano komanso nthawi zonse ndi khalidwe lathu losoweratu thandizo, limene likupangitsa mphanvu zake zoombola kukhala chosowa chachikulu. Posiya kuzidalira tokha konse, tikhoza kuyang’ana ku mtanda wa kavale ndi kunena kuti; “Mmanja mwanga mulibe chopereka chilichonse chimene ndikuchibweretsa ndikungokangamira ku mtanda wanu basi.” – *The Ministry of Healing*, p. 65.

1. Kodi ndi chifukwa chiyani kawirikawiri aneneri salandiridwa bwino kwawo?
2. Kodi ndi mawu anji amdindo amene akuonetsera kusakhulupilira kwake?
3. Kodi ndi motani mmene Khristu anachitira ku kusakhulupilira kwa anthu?
4. Kodi ndi ndani amene anaonetsera chikhulupiliro chachikulu mwa Yesu- Ayuda kapena aMitundu?
5. Kodi Yesu akulonjeza chiyani kwa onse amene abvomereza kuitana kwake?

YESU NDI OPUWALA WA KU BETESAIDA

VESI LOLOWEZA: “Koma Yesu anayankha iwo, Atate wanga amagwira ntchito kufikira tsopano, Inenso ndigwira ntchito” (Yohane 5:17).

Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, Vol. 1, pp. 560-567.

“Ntchito ya Khristu ya kuchiritsa odwala inali yogwirizana bwino ndi lamulo, imalemekeza sabata.” – *The Desire of Ages*, p. 207.

1. MADZI OCHIRITSA

Loyamba, marichi 9

a. Kodi ndi chifukwa cha cholinga chanji chimene anthu ambiri opuwala amapitira ku Yerusalemu? Yohane 5:2, 3.

b. Kodi ndi chikhulupiliro chanji chimene anthu anali nacho chokhuza thamanda la Betesida? Yohane 5:4.

“Pa nthawi ina madzi athamanda limeneli amatakasidwa ndipo chimakhulupiliridwa kwambiri kuti chimenechi chinali chotsatira cha mphanvu za uzimu, ndi kuti winaaliyense amene angalowe mmadzimu koyambilira madziwo akatakasidwa, azachilitsidwa nthenda iliyonse imene iye alinayo. Mazana mazana aanthu odwala amakayendera kumalowa; koma khamu linali lalikulu zedi kotero kuti pamene madziwo atakasidwa amathamangira patsogolo, kuponda ndi mapazi awo azibambo, azimayi, ndi ana, ofooka kuposa iwo eni. Ambiri amatha kuyandikira pafupi ndi thamanda. Ambiri amene amakwaniritsa kufika pa thamandalo amafa ali mphepete. Makumbi anamangidwa pozungulira malo amenewa, kuti odwala azitha kutetezeka ku dzuwa la masana ndi kukuzizira kwa utsiku. Panali ena amene anagona mumakumbi amenewa, omakwawira mbali mwa thamandali tsiku ndi tsiku, kwa chabe ndi chiyembekezo cha kupeza thandizo.” – *The Desire of Ages*, p. 201.

c. Kodi kuyankhulana kwa pakati pa Yesu ndi munthu wina pa thamandapa kunayamba motani? Yohane 5:5-7

a. Kodi ndi ntchito yanji yosatheka mwa umunthu imene Yesu anamulamulira munthu wopuwala kuti achite- nanga zotsatira zake zinali zotani? Yohane 5:8, 9 (mbali yoyamba).

“Yesu sanamufunse odwala ameneyu kuti akhale ndi chikhulupiliro mwa iye. Iye anangonena naye chabe kuti `tauka yalula mphasa yako, nuyende. ‘ Koma chikhulupiliro cha munthuyu chinagwira pa mawu amenewa minyewa ndi misempha iliyonse inatakasika ndi moyo watsopano, ndipo mchitidwe wa thanzi unabwera ku myendo yake yopuwala popanda funso iye anakhazikitsa mtima wake kuti amvere lamulo la Khristu, ndipo minofu yake inachita monga mwa chifuniro cha mtima wake. Pozuka ndi myendo yake, iye anazipeza yekha munthu wamphanvu.

“Yesu sanampatse iye chitsimikizo chilichonse cha thandizo la umulungu. Munthuyu akanatha kuima kumakaikira, ndikutaya mwayi wake umodzi wa kuchilitsidwa. Koma iye anakhulupilira mawu a Khristu, ndipo pakuchita mawuwo iye analandira mphanvu.” – *The Desire of Ages*, pp. 202,203.

b. Kodi ndi mukhalidwe lanji la uzimu mmene anthu amene achotsedwako kuchoka kwa Khristu amazipeza okha? Yesaya 1:5, 6; Aroma 7:24.

“Kudzera mu uchimo ife tadulidwa kuchoka ku moyo wa Mulungu. Miyoyo yathu ndi yopuwala. Mwa ife tokha tilibe ife kuthekera kwa kukhala moyo wachiyero monganso analili munthu opuwala kuti analibe kuthekera kwa kuyenda. Pali anthu ambiri amene amazindikira kusowa thandizo kwawo. Amene amafunitsitsa moyo wauzimu umene ungawabweretse iwo muchiyanjano ndi Mulungu; mwachabe amayesesa kuti awupeze iwo.” – *Ibid*; p 203.

c. Kodi ndi mankhwala anji okha amene angachilitse khalidwe limeneli? Machitidwe 9:34.

“Mpulumutsi akuwelamira pa amene anagulidwa ndi mwadzi wake, ndi kunena ndi chifundo ndi chikondi chosaneneka, `ufuna, kuchiritsidwa kodi? Iye akukulamulirani inu kuti dzuka mwa thanzi ndi mtendere. Musadikire kuti muzimve mumtima kuti mwachiritsidwa. Khulupilirani mawu ake, ndipo azakwaniritsidwa. Ikani chifundo chanu ku mbali ya Khristu. Chifuniro choti mutumikira iye, ndipo mukuchita monga mwa mawu ake inu muzalandira mphanvu kaya ndi khalidwe loipa lanji, chikhumbokhumbo chachikulu chimene kudzera mukuchita kwa nthawi yaitali chikumanga zingwe thupi ndi moyo, Khristu ndi wothekera ndi ofunitsitsa ku pulumutsa. Iye adzapereka moyo ku moyo umene uli okufa mu uchimo.’ Aefeso2:1. Iye azamasula kuti akhale amfulu ansinga mukufgooka ndi masoka ndi maunyolo a chimo.” – *Ibid*.

a. Kodi ndimotani mmene Khristu amatithandizira ife kuti tigonjetse? Aefeso 2:1-6

“Munthu mwachibadwa amakondwera kutsatira malingariro asatana, ndipo iye sangathe kumukaniza mwachipambano mdani woopsa ameneyi pokhapokha Khristu, mgonjetsi wamphanvu, akhala mwa iye, natsogolera zikhumbokumbo zake, ndikumpatsa iye mphanvu...Satana amaziwa bwino kwambiri kuposa anthu aMulungu mphanvu zimene iwo angakhale nazo zomugonjesera iye pamene mphanvu zawo zili mwa Khristu. Pamene iwo mozichepetsa achonderera thandizo kwa mgonjesi wamphanvu, okhulupirira ofooketsetsa wachoonadi, wodalira modzadza mwa Khristu, angathe mwachipambano kumlaka Satana ndi khamu lankhondo lake lonse.” – *Testimonies for the church, Vol. 1, p. 341.*

“Tikuyenera kuphunzira za Khristu. Tikuyenera ife kuziwa chimene iye ali kwa onse amene iye wawaombola. Tikuyenera kuzindikira kuti kudzera muchikhulupiriro mwa iye ndimwayi wathu kukhala otenga nawo mbali khalidwe la umulungu, ndipo kotelo kuthawa chibvundi chimene chili mudziko lapansi kudzera muchilakolako. Kenako ife timayelesedwa kuchokera kuuchimo onse, zilema zonse za khalidwe. Sitikufunika ife kulekerera khalidwe limodzi lauchimo...”

“Pamene ife tikutenga nawo mbali khalidwe la umulungu zizolowezi za chibadwa ndizotengela za zoipa timadulidwako kuchokera kukhalidwe, ndipo ife timapangidwa mphanvu zamoyo timapangidwa kukhala mphanvu zabwino kuubwino. Nthawi zonse kuphunzira za mphuzitsi wa umulungu, tsiku nditsiku otenga nawo khalidwe lake, ife timagwirizana ndi Mulungu mukugonjetsa mayesero asatana. Mulungu amagwira ntchito, ndiponso munthu amagwira ntchito, kuti munthu athe kukhala mmozi ndi Khristu monga khristu ali amodzi ndi Atate. Kenako ife timakhala pamodzi ndi Khristu mmabwalo akumwamba. Malingaliro amapumula ndi mtendere ndi chitsimikizo mwa Yesu.” – *The Review and Herald April 24, 1900.*

b. Fotokozani mtendere umene umabwera kudzera mumphanvu zochokera mwa Khristu. Aroma 8:3-6.

“Mwana aliynse amakhala moyo Kudzera mmoyo wa atate wake. Ngati inu muli mwana wa Mulungu, wobadwa kudzera mwa mzimu wake, mumakhala moyo wodzera mmoyo wa Mulungu...[ndipo]Moyo wa Khristu umaonekera mmoyo kudzera mu` thupi lathu la kufa’[2Akolinto4:11]. Moyo umenewo umene uli mwa inu udzatulutsa khalidwe lomwelo ndikuonetsera ntchito zomwezo monga unachitila mwa Khristu. Motelo inuyo mudzakhala muchiyanjano ndi lemba lina lililonse lalamulo lake; pakuti `malamulo a Yehova ali angwiwo, akubwezera moyo.’Masalmo19:7, mwatanthauzo. Kudzera muchikondi `choikika chake chakulamulo’ chizakwanilitsidwa mwa ife, `amene sitiwendayenda monga mwa thupi koma monga mwa mzimu.’ Aroma 8:4” – *Thoughts from the Mount of Blessings, p.78.*

a. Posalabadira mdalitso umene unapelekedwa kwa opuwala, kodi ndichifukwa chiyani afalisi anakwiya kwambiri? Yohane 5:9 (gawo lomaliza), 10.

“Pamene opuwala ochilitsidwayo anathamanga mwa changu kumapita ndi kuyenda kwa mphanvu ndimastepe omasuka, kumayamika Mulungu ndi kumakondwerera mumphanvu zake zatsopano zomwe anazipedza, iye anakumana ndi Afalisi ambiri, ndipo mwachangu anawauza iwo zakuchilitsidwa kwake. Iye anadabwitsika pakusasamala kumene iwo anali nako pomvetsera kunkhani yake.

“Ndikhope zakugwa anamudula iye pakamwa, pomufutsa chifukwa chiyani iye ananyamula mphatsa yake patsiku lasabata. Iwo mwamkwiyo anamkumbutsa iye kuti sichololeka kwa iye kusenza katundu patsiku la Ambuye. Muchisangalaro chake munthuyu anaiwala kuti tsikuli linali lasabata; komabe iye samachinva muntima kususika pa kumvera lamulo la iye amene anali ndi mphanvu zotere zochokera kwa Mulungu. Iye molimba mtima anayankha kuti, ‘Iye amene anandichilitsa, yemweyu anati kwa ine, yalula mphasa yako, nuyende.’ Ndipo iwo anamufunsa iye kuti ndi ndani amene anachichita ichi koma iye samamdziwa kuti ndi ndani. Atsogoleri amenewa amadziwa bwinobwino kuti ndi mmodzi yekha wakhala akuzionetsera yekha kuthekera kwa kuchita chozizwa chimenechi; koma iwo amafunitsitsa umboni wachindunji woti ndi Yesu, kotero kuti iwo akathe kumuimba mlandu iye kuti ndi wophwanya sabata. Mukuweruza kwawo iye sanangophwanya kokha lamulo mu kuchiritsa munthu pa tsiku la sabata komanso wachita chinthu choipitsitsa mu kulamulira iye kuti anyamule mphasa yake.” – *The Desire of Ages*, pp. 203,204

b. Kodi Ayuda analipanga Sabata kukhala chiyani? Mateyu 23:4.

“Ayuda anapotozeratu lamulo kotero kuti analipanga ilo kukhala gori la ukapolo. Zofuna zawo zopanda tanthauzo zinakhala manong’onong’o pakati pa maiko ena. Makamaka sabata linachingilidwa ndi zolesa zopanda tanthauzo zambirimbi. Kwa iwo silinali losangalatsa; tsiku loyera la Ambuye, lolemekezeka. Alembi ndi Afalisi anapanga kusunga kwake cholemetsa chosapilirika. Muyuda samaloledwa kusonkha moto kapena kuyasa kandulo pa Sabata. Zotsatira zake anthu amadalira anthu amitundu muzochitika zambiri zimene myambo yawo imawaletsa iwo kudzichitira iwo eni. Iwo samaonetsera kuti ngati machitidwe awa ali uchimo, iwo amene akugwiritsa ntchito ena kuti achite zimenezo ndi olakwa chimodzimidzi ngati kuti achita ntchito zimenezo iwo eni. Iwo amaganiza kuti chipulumutso chinali cha Ayuda basi, ndipo khalidwe la anthu ena onse, pokhala lopanda chiyembekezo ndi kale, silingaipitsidwenso. Koma Mulungu sanapereke malamulo amene sakuyenera kumveredwa ndi onse. Malamulo sakubvomereza zoletsa zosamveseseka kapena zaundekha.” – *Ibid.*, p. 204.

a. Kodi Khristu amagwirizana bwanji ndi lamulo la Mulungu komanso ndi Sabata? Yesaya 42:21.

“Yesu anabwela kudzakwedza lamulo ndi kulipanga ilo kukhala lolemekezeka. Iye samachepetsa kulemekezeka kwake, koma kulikweza ilo...Iye anabwera kuzamasula zosafunikira zolemetsa kuchoka ku Sabata zimene zimalipanga ilo kukhala themberero mmalo mwa mdalitso.” – *The Desire of Ages*, p. 206.

b. Kodi ndi chiyani chimene chikuyenera kapena chimene sichikuyenera kuchitidwa pa tsiku la Sabata? Eksodo 20:8-11.

“Pakati pa anthu osausika amene anali pa thamanda [Khristu] anasankha munthu wobvutikitsisa kuti agwiritse ntchito mphanvu zake zochilitsa, ndipo analamula munthu kuti anyamule mphasa yake kudutsa mu mzinda ndi cholinga choti afalitse ntchito yaikulu imene inachitidwa pa iye. Ichi chikhoza kuutsa mafunso okhuzana ndi kuti kodi choyenera kuchitidwa pa Sabata ndi chiyani, ndipo chikhoza kutsegula njira kuti iye azuzule zoletsa za Ayuda zokhuza tsiku la Ambuye, ndi kulengeza za kutha kwa myambo yawo.

“Yesu anafotokoza kwa iwo kuti ntchito yakuthandiza osausika inali yogwirizana ndi lamulo la Sabata. Ndi yogwirizana ndi ntchito ya angelo a Mulungu amene nthawi zonse amakwera ndi kusika pakati pa kumwamba ndi dziko lapansi kukatumikira anthu obvutika...

“Munthunso ali ndi ntchito yoti ayigwire mutsiku limeneli. Zofunikira za moyo zikuyenera kuchitidwa, odwala akuyenera kusamalilidwa, zosowa za osowa zikuyenera kuperekedwa. Sazatengedwa kukhala opanda mulandu iye amene amanyozera kuthandiza osausika pa sabata. Tsiku loyera lopuma la Mulungu linapangidwa chifukwa cha Munthu, ndipo ntchito za chifundo ndi zogwirizana bwino ndi cholinga chake. Mulungu samafuna kuti zolengedwa zake zisauke ndi ululu ngakhale mkamphindi umene angathe kuthandizidwa pa Sabata kapena pa tsiku lina.” – *Ibid.*, pp. 206,207.

6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

Lachisanu ndi chimodzi, Marichi 14

1. Kodi ndi chikhulupiriro chanji chimene chinaliponseponse chokhuzana ndi thamanda la Betsida.
2. Kodi ndi odwala wanji wapadera amene anakopa chidwi cha Khristu.
3. Kodi ndi motani mmene kupuwala kwathu kwa uzimu kungachilitsidwire?
4. Kodi ndi chiyani chimene chinakwiwitsa Ayuda kwambiri chokhalana ndi kuchilitsidwa kozwizwitsaku?
5. Kodi ndi ntchito zANJI zimene zili zogwirizana ndi lamulo la Sabata?

ULAMULIRO WA MWANA WAMUNTHU

VESI LOLOWEZA: “Pakuti monga Atate ali ndi moyo mwa iye yekha, momwemonso anapatsa mwana kukhala ndi moyo mwa iye yekha; ndipo anampatsa iye mphanvu yakuchita mlandu pakuti ali mwana wa Munthu”(Yohane 5:26,27).

Zowelenga zoonjezera: Thoughts from the Mount of the Blessing, pp. 123-129.

“Ulamuliro wanga, [Yesu] anati, wakuchitila ntchito imene inuyo mukundineneza Ine, ndiwoti Ine ndine mwana wa Mulungu, Mmodzi ndi Iye muchilengedwe, muchifuniro, ndi mucholinga. Muntchito zake zonse za chilengedwe ndi chisamaliriro, ndimagwirizana ndi Mulungu.” – *The Desire of Ages*, p. 208.

1. OFANANA NDI MULUNGU

Loyamba, Marichi 16

a. Pambali pa kuchilita munthu wopuwala pa dzuwa lasabata, ndichifukwa china chitino chimene Ayuda anadanira ndi Yesu? Yohane 5:17, 18.

“Yesu anazinena kukhala ndi ulamuliro wofanana ndi Mulungu...

“Mtundu wonse wa Ayuda umamuchula Mulungu kuti Atate wawo, chotelo iwowo sakanakwiyitsidwa kwambiri chotelo ngati Khristu akanazionetsera yekha kuti ali ndi chibale chofanana chotele ndi Mulungu. Koma iwo anamuimba mlandu wakuchita mwano, kuonetsera kuti iwo amumvetsetsa iye kuti akuzinena yekha mulingaliro lapamwamba.” – *The Desire of Ages*, pp. 207,208.

b. Kodi ndimotani mmene Khristu anasimikizira ulamuliro wa malamulo a Mulungu pamwamba pa miyambo ya anthu? Mateyu 15:1-9, 13.

“Adani awa akhristu analibe zotsutsa zina zilizonse zoti athe kukwanitsa kutsutsa choonadi chimene iye amachibweretsa mosindika kuchikumbumtima chawo. Iwo amangofotokoza chabe za miyambo ndi malamulo awo, ndipo zimenezi zimaoneka zofooka ndizopanda pake pamene zikufanizilidwa ndi mfundo zimene Yesu amazipeleka kuchokera mumalembo a Mulungu ndi muzochitikachitika zosalekeza za chilengedwe.” – *Ibid.*, p. 208.

a. **Kodi ndimotani mmene Yesu anafotokozera ubale wake ndi Atate? Yohane 5:19, 20.**

b. **Kodi ndiulamuliro ndi mphanvu zANJI zochokera kwa Atate zimene Khristu analengeza kuti iyenso alinazo? Yohane 5:21-23.**

“Ansembe ndi atsogoleri anaziika iwo okha monga oweludza oti azitsutsa ntchito za Khristu, koma iye anazilengezetsa yekha kukhala oweludza wawo, ndi oweludza wadziko lonse lapansi. Dziko lapansi linaperekeka kwa Khristu, ndipo kudzera mwa iye kwakhala kukubwela mdalitso winaulionse wochokela kwa Atate kupita kumtundu wakugwa wa Anthu. Iye anali mombolo mmbuyo monsemu monganso analiri atabwela ndi kukhala munthu. Pomwepo pomwe chimo linapezeka, Pomweponso panali mpulumutsi. Iye anapeleka kuunika ndi moyo kwaonse, ndipo molingana ndimuyeso wakuunika komwe kunapelekedwa, wina aliyense azaweluzidwa. Ndipo iye amene anapeleka kuunika, iye amene wakhala akuutsatila moyo ndi kuchonderera kwa chifundo, kufunafuna kuti aupindule iwo kuchokera kuuchimo kupita kuchiyelo, ndimmodzi yemweyo mkhala pakati ndi oweludza wake.” – *The Desire of Ages*, p. 210.

c. **Fotokozani kusintha kwa khalidwe kumene kumachitika pamene ife tikuzindikira kuti khristu ndioweludza wathu. Aroma2:1-3; Mateyu 7:1.**

“Iye amene akuzipereka kukhala ndi Mzimu wakuneneza ali ndi mlandu wachimo lalikulu kupotsera iye amene iye akumuneneza, popedza iye sakungochita chabe chimo lomwelo, koma akuphatikizira ku ilo chinyengo ndikutola zifukwa.

“Khristu ndi muyeso woona wokha wa khalidwe, ndipo iye amene amaziika yekha pamwamba monga muyeso wa ena akuziika yekha pamalo pa Khristu. Ndipo popedza Atate ‘anapereka kuweludza konse kwa mwana’ (Yohane 5:22), Iye amene amaziika yekha kuti aziweludza zolinga za ena kawilinsu akuukila udindo wa mwana wa Mulungu. Ozinena kukhala oweludzawa ndi otsutsa ena akuziika okha kumbali yawokana Khristu, ‘amene atsutsana nazo nadzikuza pazonse zochedwa Mulungu, kapena zopembezeke; kotelo kuti iye wakhala pansu kukachitsi wa Mulungu, nazionetsera kuti ali Mulungu.’ 2Atesalonika 2:4.” – *Thoughts from the Mount of Blessings*, pp.125,126.

“Ife sitingathe kuwelenga mtima. Ife eni olakwa, sindife oyenela kukhala pansu ndi kumaweluzwa ena. Anthu amalire akhoza kuweludza zooneka zokha zakunja. Kwa iye yekha amene amaziwa zinsisi zimene zimatsogolera machitachita, amenenso amachita ndi anthu mwachifundo ndi mwachikondi, ndi amene anapatsidwa mphanvu yakuweludza moyo wina ulionse.” – *Ibid.*, p. 124.

a. Kodi ndi chisimikizo chanji chimene chapatsidwa kwa okhulupilira aliyense odzipereka kwa Khristu? Yohane 5:24.

“Mukulamula kulikonse ndimulonjezo lilonse la mmawu a Mulungu ndimphanvu, moyo weniweni wa Mulungu, pkumene kudzera mmenemo kulamulako kudzakwanilitsidwa ndi lonjezo kukwanilitsidwa. Iye amene mwachikhulupiliro akulandira mawu akulandira moyo weniweni ndi khalidwe la Mulungu.” – *Christ’s Object Lessons, p. 38.*

“Ntchito yayikulu imene anachitilidwa ochimwa amene wadetsedwa ndikukhala ndi chilema ndizoipa ndi ntchito yakulungamitsidwa. Kudzera mwa iye amene amalankhula choonadi iye amalengezetsedwa kuti ndiolungama. Ambuye amaika pa okhulupilira aliyense chilungamo cha Khristu ndikumulengeza iye kuti ndiolungama pamatso pa chilengedwe chonse. Iye amasamusira machimo ake kwa Khristu, amene ndimlowa mmalo, chikole, ndi dipo la ochimwa. PaKhristu iye amaika mphulupulu ya moyo wina ulionse umene wakhulupirira ‘ameneyo sanaziwa uchimo anamuyesera uchimo mmalo mwathu kuti ife tikhale chilungamo cha mulungu mwa iye.’ (2 Akolinto 5:21)...

“Ngakhale monga ochimwa momwe tilili pansu pakutsutsidwa ndi lamulo, komabe Khristu kudzera mukunvera kwake kumene anakuonetsera ku Lamulo, iye amanenera ku moyo wolapa kuyenera kwa chilungamo cha iye mwini. Kuti tipedze chilungamo cha Khristu, ndichofunikira kwa ochimwa kuti aziwe tanthauzo la kulapa kumene kumabweretsa kusintha mmalingaliro, muuzimu ndi mmachitidwe. Ntchito yakusinthika ikuyenera kuyambira mumtima, ndikuonetsera mphanvu zake mugawo lililonse la munthu; koma munthu alibe kuthekera kwakuyambitsa kulapa kotere, Ndipo angakhale nako kudzera mwa Khristu yekha basi, amene ‘anakwera kumwamba, ndikukamanga amsinga, ndikukapatsa mphanvu kwa anthu.’ ” – *Selected Messages, bk. 1, pp. 392, 393.*

b. Kodi ndimaudindo anji aumulungu amene Khristu anabvumbulutsa kuti alinawo? Yohane 5:25-29.

“Chifukwa choti iye analawa matsautso ndi mayetsero aanthu, ndipo amamvetsetsa kufooka ndi machimo anthu; Chifukwa choti mmalo mwathu iye analimbana ndikugonjetsa Satana, Ndipo azachita molungama ndi mwachifundo ndimoyo ulionse umene mwadzi wake wa iye yekha unakhesedwa kuti ukapululumutse-chifukwa cha ichi, mwana wa munthu anasankhidwa kuti akapeleke chiweludzo.” – *The Desire of Ages, p. 210.*

“Khristu ndiovekedwa ndi mphanvu zakupatsa moyo kuzolengedwa zonse.” – *Selected Messages, bk. 1, p. 249.*

a. Kodi ndi motani mmene Khristu anafotokozera chifukwa cha kusakhulupirira kwa Ayuda? Yohane 5:37, 38.

“Mmallo mopepetsa chifukwa cha machitidwe amene iwo amadandaula, kapena kufotokoza cholinga chake mukuchita ichi, Yesu anatembenukira kwa atsogoleri, ndipo onenezedwa anakhala oneneza. Iye anawadzuzula iwo za kuuma kwa mitima yawo, ndikusazindikira kwawo kwa malembo. Iye anafotokoza kuti iwo akana malembo a Mulungu, monganso mmene iwo amukanira iye amene Mulungu anamutuma.” – *The Desire of Ages*, p. 211.

b. Kodi ndi chifukwa chiyani aYuda amalephera kuzindikira malembo? Yohane 5:39, 40.

“Musamba lililonse, kaya mbiri, kapena lamulo, kapena uneneri, malembo achipangano cha kale ndi owalitsidwa ndi ulemerero wa Mulungu. Monga mmene zinaliri malamulo khumi, dongosolo lonse la chiyuda unali uneneri odzadza wa uthenga wabwino. Kwa Khristu ‘aneneri onse amuchitira umboni.’ Machitidwe 10:43. Kuyambira kulonjezo limene linapelekedwa kwa Adamu kufikira kupyola munthawi ya akuluakulu achikhulupiliro ndikwa oweludza, kuunika kwa ulemerero kwa kumwamba kunaonetsera poyela mapadzi ampulumutsi. Aneneri anaona nyenyezi yaku Beterehemu, Silo amene azabwere, pamene zinthu za msogolo zimadutsa pamaso pawo mundanda wodabwitsa wa chinsinsi. Munsembe iliyonse imfa ya Khristu imaonetsedwa. Mu mtambo ulionse wazofukitsa chilungamo chake chimakwela. Kudzera mulipenga lililonse lachikondwerero dzina lake limaveketsedwa. Muchophimba chodabwitsa cha chinsinsi chochititsa mantha chakumalo opatulikitsitsa ulemerero wake umakhalako.

“Ayuda anali anthu amene amasunga malembo, ndipo amalingalira kuti kudzera muchidziwitso chawo cha pamwamba chamalembo iwo alinawo moyo wosatha. Koma Yesu anati, ‘Mulibe inu mawu ake akukhala mwa inu.’ Pokana Khristu mmawu ake, iwo anamukana iye pamaso. ‘simukudza kwa ine,’ iye anatelo, ‘Kuti mukhale nawo moyo.’

“Atsogoleri aYuda amawelenga ziphuzitso za aneneri zokhuzana ndi ufumu wa Mesiya; koma iwo amachita ichi, osati ndikhumbo loona lakuti adziwe choonadi, koma ndicholinga choti apedze maumboni olimbikitsira ziyembekedzo zawo za undekha. Pamene Khristu anabwera munjira yosiyana ndi mmene iwo amayembekezera, iwo sanathe kumulandira iye; ndipo ndi cholinga chozilungamitsa okha, iwo anayestetsa kuti aonetsere umboni kuti iye ndiwachinyengo. Pamene kamodzi iwo anaika mapadzi awo munjira imeneyi, zinali zophweka kuti Satana alimbikitse kutsutsa kwawo komutsutsa Khristu. Mawu omwewo amene amayenera kulandilidwa ngati umboni wa umulungu wake amathanthauziridwa momutsutsa iye. Chotelo iwo anatembenudza choonadi cha Mulungu kukhala bodza.” – *Ibid.*, pp. 210, 212.

a. Kodi ndi chiyani chimene chinasogolera Ayuda kuti akane Yesu ndikufuna aphuzitsi abodza? Yohane 5:41-44.

“Yesu anati, ‘Sindilandira ulemu kuchokera kwa anthu.’ Sichinali chikoka cha aSanihedrin, sichinali chibvomerezo chawo chimene iye amachifuna. Iye sakadatha kulandira ulemu kuchokera kukuyamikira kwawo. Iye anali ovekedwa ndi ulemu ndi ulamuliro wa kumwamba. Ngati iye akanakhala kuti amachifuna chimenechi, angelo akanatha kubwera ndikuzampatsa iye ulemu; kawirinsu atate anachitira umboni za umulungu wake. Koma chifukwa cha kuubwino wawo, kuubwino wadziko limene iwowo anali atsogoleri ake, iye anafunitsitsa atsogoleri a Ayuda kuti adzindikire khalidwe lake, ndikulandira madalitso amene iye anabwera kudzawapatsa iwo.

“`Ndaza ine mudzina la atate wanga, ndipo simundilandira ine; akadza wina mudzina lake la iye mwini koma iyeyo muzamulandira.’ Yesu anabwera kudzera muulamuliro wa Mulungu, anali ndi chithunzithunzi chake, anakwanilitsa mawu ake, ndikufunafuna ulemerero wake; komabe iye anali osalandilidwa ndi atsogoleri a Israeli; koma pamene ena adzabwere, omanamizira khalidwe la Khristu, koma omadzazidwa ndi chifuniro cha iwo eni ndikumafunafuna ulemerero wa iwo eno, iwo adzalandiridwa. Nanga chifukwa chiyani? Chifukwa iye amene amafunafuna ulemerero wa iye mwini amakopa khumbo lakufuna kudzikweza wekha mwa ena. Kukopa kotele Ayuda azakukondwerera, iwo azatha kulandira mphuzitsi wabodza chifukwa choti iye amayamikira mwabodza kunyada kwawo kudzera mukubvomeredza malingaliro awo okonedwa ndi miyambo yawo. Koma chiphuzitso cha Khristu sichimabvomelezana ndi mfundo zawo. Chinali cha uzimu, ndipo chimafuna kupereka nsembe undekha; chotelo iwo sanathe kuchilandira icho. Iwo sanali ozolowelana ndi Mulungu, ndipo kwa iwo mawu ake kudzera mwa Khristu anali mawu a Mlendo.

“Kodi chinthu chomwechi sichikubwelezedwa mmatsiku athu? Sipali ambiri, Ngakhale atsogoleri azipembedzo amene akuumitsa mitima yawo kulimbana ndi mzimu woyera, kuchipanga kukhala chosatheka kwa iwo kudzindikira mawu a Mulungu? Kodi iwo sakukana mawu a Mulungu, kuti azitha kusunga myambo yawo?.” – *The Desire of Ages*, pp. 212, 213.

6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

Lachisanu ndi chimodzi, Marichi 21

1. Kodi ndi ulamuliro ndi kuyenera kwanji kumene Khristu akunena kuti ali nawo?
2. Kodi ndi ubale wanji umene wakhala ulipo pakati pa Khristu ndi Atate?
3. Kodi ndi mphanvu zANJI zopereka moyo zimene Khristu ali nazo?
4. Fotokozani Yohane 5:39.
5. Fotokozani zotsatira za mtundu wachiyuda kukana Khristu monga Mesiya.

YESU ADYETSA KHAMU LA ANTHU

VESI LOLOWEZA: “Koma Yesu anati kwa iwo, Iwo alibe chifukwa cha kumukira, apatseni ndinu adye” (Mateyu 14:16).

Zowelenga zoonjezera: Testimonies for the Church, Vol. 6, pp. 341-348.

“Kawirikawiri timanyalanyaza, osafuna kuti tipereke zonse zomwe tilinazo, kuopa kuononga chuma ndi kubvutika chifukwa cha ena. Koma Yesu akutilamulira ife kuti, ‘Apatseni iwo kuti adye.’ Kulamula kwake ndi lonjezo ndipo kuseri kwa ilo kuli mphanvu zomwezo zimene zinadyetsa khamu la anthu pambali pa nyanja.” -The Desire of Ages, p. 369.

1. MIYOYO YANJALA

Loyamba, Marichi 23

a. Kupatula ophunzira, kodi ndi ndani enanso amene anasagana naye Yesu pamene iye amaoloka nyanja ya Galileya isanafike paskha? Yohane 6:1, 2.

“Khristu anapita kumalo achinsinsi kukapuma ndi ophunzira ake, koma nthawi yopuma yabata yosowayi inasokonezedwa. Mwansangansanga ophunzira anaganiza kuti iwo apita kukapuma kumalo amene iwo sangasokonezedwe; koma khamu la anthu mwansanga nsanga pamene linayamba kusowa Mphunzitsi wa umulungu, iwo anafunsana, ‘Kodi ali kuti iye?’ ena mwa iwo anaona komwe Khristu ndi ophunzira ake analowela. Ambiri anayenda pa mtunda kuti akakumane nawo, pamene ena anatsatira ndi mabwato awo kudutsa pa Nyanja. Paskha anali pafupi kuti achitike, ndipo, kuchokera kutali ndi pafupi, magulu magulu a anthu apaulendo opita ku Yerusalemu anasonkhana kuti aone Yesu. Amachulukira chulukira kufikira anasonkhana amuna pafupifupi zikwi zisanu osawerenga ana ndi azimayi. Yesu asanafike pa gombe, khamu linali litasonkhana kale likumuyembekezera iye koma iye anafika mwakachetechete iwo osazindikira, ndipo anakhala kanthawi kochepea ndiophunzira ake ali paokha.” – *The Desire of Ages*, p. 364.

b. Fotokozani khalidwe la uzimu la anthu omwe anasonkhana pamenepa. Marko 6:34.

a. Kodi ndi chiyani chimene khristu mwachifundo anachizindikira kuti anthu akuchisowa-nanga ndi motani mmene iye anagwiritsira ntchito mwayi umenewu kuti ayese chikhulupiliro cha ophunzira wake Filipo? Yohane 6:3-6.

“Kuchokera pa phiri [Yesu] anayang’ana pansi pa khamu la anthu limene limayendayenda, ndipo mtima wake unatakasidwa ndi chifundo. Osokonezedwa monga momwe anariri, ndi wolandidwa kupuma kwake, Iye sanakwiye. Iye anaona chosowa chofunikira chachikulu chosoweka kulowelerapo kwake pamene amayang’ana anthu akubwera ndi kumabwerabe. Iye anakhuzika ndi chifundo ndi iwo chifukwa anali ngati nkhoa zopanda m’busa. Posiya malo ake opumulira, iye anapeza malo oyenera amene iye angathe kuwatumikira iwo. Iwo sanalandire thandizo lililonse kuchokera kwa Ansembe ndi atsogoleri; koma madzi amachiritso a Moyo amayenda kuchokera mwa Khristu pamene iye amaphunzitsa khamu njira ya chipulumutso...

“Tsikuli linaoneka kwa iwo monga kumwamba padziko lapansi, ndipo iwo samazindikira konse za kutalika kwa nthawi imene iwo anakhala osadya kanthu.

“Mapeto ake tsiku linafika madzulo. Ndipo dzuwa linali kulowa kumadzulo, komabe anthu anakhalabe pamalopo. Yesu anatumikira tsiku lonse popanda kudya kapena kupumula. Nkhope yake imaoneka yotopa komanso anali ndi njala, ndipo ophunzira anamupempha iye kuti aleke kutumikira kwake. Koma iye sakanakhonza kuzipatula yekha kuchoka ku khamu limene limazipanikiza kwa iye...

“Iye amene anaphunzitsa anthu njira imene angapezere mtendere ndi chimwemwe anali wolingalira zedi za zosowa zawo za kuthupi monganso zosowa zawo za uzimu. Anthu anali otopa ndi olema ndi kukomoka. Panali azimayi amene anali ndi makanda mmanja mwawo komanso ana achichepere amene amazendewera kumasiketi awo. Ambiri anali ataimilira kwa maola ambiri...

“Ambiri anali ochokera kutali, ndipo anali asanadye kanthu kalikonse kuyambira mmamawa. Kumizinda ndi midzi yozungulira iwo akanatha kukagula zokudya....Koma Yesu anati, ‘Apatseni kudya ndiinu’ ndipo kenako, potembenukira kwa Filipo, iye anamufunsa iye, ‘kodi tidzagula kuti mikate kuti adye awa?’ Koma ananena ichi kuti ayese chikhulupiliro cha ophunzira ameneyu.” – *The Desire of Ages*, pp. 364, 365.

b. Kodi yankho la Filipo linali lotani? Yohane 6:7.

“Filipo anayang’ana pa khamu lalikulu lomwe linali pamenepa, ndipo analingalira momwe chinalili chosatheka kuwapatsa iwo chakudya chokwanira kukhutitsa njala ya khamu lotere. Iye anayankha kuti mikate yokwana malupiya atheka mazana awiri siili yokwanira kugawira iwo ngakhale kuwagawanitsa pang’onopang’ono, kotero kuti aliyense athe kukhala ndi kochepe.” – *Ibid.*

a. Kodi ndi chidziwitso chanji chimene Andreyana anachipereka kwa Yesu- nanga kodi ndi chiyani chimene Ambuye anawalamulira ophunzira kuti achite? Yohane 6:8-10.

“Yesu anafunsa kuti kodi ndi chakudya chochuluka bwanji chimene chingapedzeke pagulu pamenepo. Pali nyamata pano, ananenanso Andreyana, `Amene ali nayo mikate isanu yaberere, ndi tinsomba tiwiri, koma nanga izi zifikira bwanji ambiri otere?’ Yesu anapempha kuti zimenezi zibwerestedwe kwa iye. Kenako anawauza ophunzira kuti awakhalitse anthu pansi pa udzu mmagulu amakumi asanu kapena zana, kuti pakhale dongosolo, ndi kuti onse athe kuchita umboni kuchomwe iye amafuna kuti achichite.” – *The Desire of Ages*, p. 365.

b. Fotokozani ndandanda wa zimene Khristu anachita kuti achulukitse zakudya-nanga kodi ndi maphunziro anji amene ife tingathe kuphunzira kuchokera ku chimenechi? Mateyu 14:19; Marko 6:37-41; Yohane 6:11.

“Yesu sanafune kuti akope anthu kupita kwa iye kudzera mukuwapatsa zofuna zawo za manyado. Kukhamu lalikulu limenelija, lotopa ndi lanjala chifukwa cha tsiku lalitali, lodzala ndi zosangalasa chakudya chophweka chinali chitsimikizo cha mphanvu zake komanso chisamaliro chake cha chifundo kwa iwo mu zinthu zophweka zammoyo. Mpulumutsi sanalonjeze osatira ake zinthu zamanyado za dziko lapansi; akhoza kukhala anthu osauka; koma mawu ake alonjeza kuti zosowa zawo zizapatsidwa, ndiponso iye analonjeza icho chimene chili chabwino kwambiri kuposa chuma cha dziko lapansi- chitonthonzo cha kupezeka kwake kwa iye mwini kwa iwo.” – *The Ministry of Healing*, pp.47,48.

“Mu chozizwitsa ichi Khristu analandira kuchokera kwa Atate; iye napereka kwa ophunzira ake nagawira kwa anthu, ndipo anthu anagawana wina ndi mzake. Chotero onse amene alumikizidwa kwa Khristu azalandira kuchokera kwa iye mkate wa Moyo, naugawira iwo kwa ena. Ophunzira ake ndiye njira imene inakhazikitsidwa yolumikizira Khristu ndi anthu.” – *Ibid.*, p.49.

c. Ndi za phunziro lanji la utumiki woona limene ife tikukumbutsidwa pamenepa? Yesaya 16:6.

“Ophunzira anabweretsa kwa Yesu zonse zimene iwo anali nazo; koma iye sanawaitane kuti akhale pansi nadye. Iye anawalamulira iwo kuti apereke chakudiyacho kwa anthu. Chakudya chinachulukirachulukira mmanja mwake ndi mmanja mwa ophunzira, pomatenga kuchokera kwa Khristu, sizimatha. Nkhokwe yaing'onoyi inali yokwanira kwa onse. Pamene khamu lonse linamaliza kudya, ophunzira anadya ndi Khristu, chakudya chamtengo wapatali, choperekedwa kuchokera kumwamba.” – *Ibid.*

a. Kodi tikuyenera kuphunzirapo chiyani kuchokera ku langizo lalikulu limene Yesu analipereka atatha kudyetsa khamu? Yohane 6:12, 13.

“Pamene mitanga ya zakudya zotsara inatoleledwa, anthu analingalira za abwenzi awo amene anali kunyumba. Iwo amafunanso anzawo agawane nawo mkate umene Khristu anaudalitsa. Zomwe zinali mmitanga imeneyi zinagawidwa pakati pa khamu lomwe linali ndi khumbo loti ligawiridwe, ndipo iwo anapita nazo kumadera onse ozungulira.”-*The Desire of Ages*, p. 368.

“Yesu analamulira ophunzira ake ‘sonkhanitsani makombo kuti kasatayike kanthu.’ Yohane 6:12. Mawu awa ali ndi tanthauzo lalikulu kuposa kungoika zakudya mumitanga. Phunziroli ndi lambali ziwiri. Pasamakhale kutayika kwa chilichonse. Tisamalore kutaya mwayi ulionse. Tisamanyozere china chilichonse chimene chingathe kupindulira munthu –lolani kuti kena kalikonse kasonkhanitsidwe kamene kangathandize kupeputsa zosowa za anthu anjala a kudziko lapansi. Ndi kusamalitsa komweku tikuyenera kumayamikira mkate ochokera kumwamba kuti ukhutitse zosowa za moyo. Kudzera muliwu linalililonse la Mulungu tikuyenera kukhala. Chinachilichonse chimene Mulungu anayankhula mmawu ake sichikuyenera kutayika. Ngakhale liwu limodzi limene limakhuza chipulumutso chathu chamuyaya sitikuyenera kulinyozera, liwu limodzi silikuyenera kugwa panso osasamalidwa.”

– *The Ministry of Healing*, p. 48

b. Ngakhale zitamaoneka ngati zosakukomera kapena zosatheka, kodi ndi makhalidwe anji a chikristu amene ife tikulamuliridwa kuti tiwakudze? Yesaya 58:6-8; 1 Petro 4:9.

“Mu chazizizi chilichonse tikuyenera ife kumapempha thandizo kuchokera kwa iye amene ali ndi zinthu zamuyaya pamaso pake...”

“Pamene ife tikuona zosowa za osauka, osazindikira, osauka, kodi ndi kangati kamene mitima yathu imakhumudwa, timafunsa kuti, kodi zingathandize chiyani mphanvu zathu zofooka ndi chuma chathu chochepa kuti zithandize zosowa zazikulu zotere? Kodi sitikuyenera kudikira munthu wina wake amene ali ndi kuthekera kwakukulu kuti atsogolere ntchito kapena bungwe lina lake lithandize izi? Khristu akuti; ‘Apatseni iwo kuti adye’; gwiritsani chuma, nthawi ndi kuthekera, zimene muli nazo. Bweresani mikate yanu kwa Yesu.

“Ngakhale kuti zomwe mulinazo sizingathe kukhala zokwanira kudyetsa zikwizikwi, zikhoza kukwanira kudyetsa mmodzi. Mumanja a khristu zimenezo zikhoza kudyetsa ambiri. Monga ophunzira, perekani zimene mulinazo; Khristu azachulukitsa mphoto imeneyo. Iye azabwezera mphoto kukudalira koona kophweka mwa iye. Icho chimene chimaoneka chochepa zedi chizakhala phwando lalikulu.” – *Ibid.*, pp. 49, 50.

a. **Kodi ndi makhalidwe odabwitsa anji a Mulungu amene ife sitikuyenera kumawaiwala? Masalmo 37:25, 26; Afilipi 4:19.**

“Ndi chisomo cha Mulungu mu zinthu zazing’ono chimene chimazipanga izo kukhala zokwanira. Dzanja la Mulungu litha kuzichulukitsa izo kukhala mazanamazana. Kuchokera ku zomwe alinazo. Iye akhoza kuyala gome Muchipululu. Kudzera mu kukhuza kwa dzanja lake iye akhoza kuchulukitsa zinthu zochepe ndi kudzipanga izo kukhala zokwanira kwaonse. Ndi mphanvu zake zimene zinachulukitsa mikate ndi ufa mmanja a ana a aneneri...

“Pamene Yesu analamurira ophunzira ake kuti apatse khamu zoti adye, iwo anayankha kuti, ‘Ife tilibe mikate koma isanu yokha ndi nsomba ziwiri, kapena timuke ndikukagulira anthu awa onse zakudya.’ Luka 9:13. Kodi zinthu zimenezi zinali chiyani pa gulu lalikulukulu?

“Phunziro limeneli ndi la ana a Mulungu mu m’bado ulionse. Pamene Ambuye wapereka ntchito kuti igwiridwe, musalore munthu wina aliyense ayime ndi kumafunsa za mzeru imene ili mukulamula, kapena zotsatira zomwe zingathe kukhalapo za kuyesesa kwawo kuti amvere. Zinthu mmanja a anthu zikhoza kuoneka zochepe kuti sizingakwanire kukwaniritsa chosowacho; koma mmanja mwa Ambuye zizaoneka kuti ndi zambiri koposa....

“Kukula kwa kumvesesa kwa ubale wa Mulungu kwa onse amene iye anawagula ndi mphatso ya mwana wake, chikhulupiriro chachikulu mukupita patsogolo kwa ntchito yake pa dziko lapansi- ichi ndi chosowa chachikulu cha mpingo lero. Musalore wina aliyense azitaya nthawi mukumafotokoza za kuchepa kwa chuma chawo chomwe chikuoneka. Zooneka zikhoza kukhala zosapasa chiyembekezo, koma mphanvu ndi chidaliro mwa Mulungu zizabweretsa chuma, Mphatso imene yabweretsedwa kwa iye ndi chiyamiko ndi pemphero lopempherera mdalitso lake, Iye azaionjezera monga momwe iye anaonjezerera zokudya zimene zinaperekedwa kwa ana a aneneri ndi khamu lotopa.” – *Prophets and Kings*, pp. 241-243.

6. MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

Lachisanu ndi chimodzi, Marichi 28

1. Fotokozani malingaliro aanthu mmene amamvesera mawu a Khristu.
2. kodi ndi motani mmene ambuye anaperekera thandizo ku zosowa zawo zakuthupi?
3. kodi ndi chiyani chimene ife tikuphunzirapo kuchokera ku mmene Khristu anasungira khamu mwadongosolo?
4. Kodi ndikuyenera kukumbukira chiyani ndikamakakamizika mumtima kuti, “Apatseni iwo kuti adye.”?
5. Chulani nthawi zimene chisamaliro cha Mulungu kwa inu mwapaderadera chinaonekera.

Chopereka cha Sabata Loyamba



Sabata Januwale 4

Malo avochitachita ra
Thanci ndi maphunziro ku
Paraguay
Mphunziro rana zovuluka manja
zidzansoimutsa
thanci ndi chikhulapiriro cha
ambiri (onani tsamba 4).



Sabata, Febuluwale 1

Chinsofeso cha ma Teoka a Padre
Lance Chopereka ichi chimapenka
chibandiro kwa anthu oswe ali
m'madira oswe akhadzidwa ndi
masoka, masenda, imfa, kapena
zovuta (onani tsamba 25).



Sabata, Malichi 1

"Ana a Khalidwe" Malo
amaphunziro Thandizani
kumaliza kumanga kwatsopano
maphunziro oyambirira kwa
achinyamata ana ku Romania
(onani tsamba 46)